Chisindikizo Choyamba

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano kwa pemphero.

Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu usikuuno chifukwa cha ichi, mwayi wina wobwera kudzakupembedzani Inu. Ife tiri othokoza chifukwa chokhala ndi moyo ndi kukhala nalo vumbulutso lopambana ili la Moyo Wamuyaya ukukhala mkati mwa ife. Ndipo ife tabwera, usikuuno, Atate, kudzaphunzira Mawu Anu, limodzi, zinsinsi zazikulu zobisika izi zomwe zakhala zobisika chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi. Ndipo Mwanawankhosa ali Mmodzi yekhayo yemwe angakhoze kuwulula Izo kwa ife. Ine ndikupemphera kuti Iye abwere pakati pathu, usikuuno, ndipo adzatenge a Mawu Ake ndi kuwaulula Iwo kwa ife, kuti ife tikhoze kudziwa momwe tingakhalire antchito abwinoko kwa Iye, mu nthawi zotsiriza izi. O Mulungu, pamene ife tikuwona kuti ife tiri tsopano mu nthawi yotsiriza, tithandizeni ife kuti tidziwe malo athu, Ambuye, ndi umunthu wathu wofooka, ndi chitsimikizo cha Kudza kwa Ambuye, posachedwapa. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

2 Ine ndikukhulupirira anali Davide, amene ananena kuti, "Ine ndinali wokondwa pamene iwo anati kwa ine, tiyeni ife tipite ku nyumba ya Ambuye." Nthawizonse umakhala mwayi waukulu kubwera. Ndipo—ndipo kuphunzira kwa Mawu, limodzi, kumatipatsa ife chiyembekezo chachikulu ichi.

3 Tsopano pali ambiri amene ayimirira, ndipo ine ndingofulumira momwe ine ndingathere. Koma ine ndikudalira kuti inu mwasangalala ndi Kukhalapo kwa Mzimu Woyera, monga ine ndachitira, mu nthawi izi zingapo zapitazi.

4 Ndipo, lero, ndinali nacho chinachake chinachitika chimene ine sindinakhale nacho kwa nthawi yaitali. Ine ndinali kuwerenga pa izi, pa vumbulutso ili apa, pa kutsegula kwa Chisindikizo.

5 Zaka zapitazo ine ndinadutsa mu Izi apa, pafupifupi zaka twente zapitazo, ine ndikuganiza, kapena chinachake monga chomwecho, koma mwanjira ina kapena imzake ine sindinakhutitsidwe kwenikweni basi. Izo zinkawoneka ngati panali zinthu zina, makamaka mu Zisindikizo izi, chifukwa Zisindikizo zimenezo ndi Bukhu lonselo. Mukuona? Izo ndizo Bukhulo. Bukhu lonseli ndi Bukhu limodzi, litasindikizidwa. Ilo likuyambira . . .

6 Mwa chitsanzo, ngati ndikanakhala ndi chinachake apa, ine ndikanakusonyezani inu chimene ine ndikutanthauza. [M'bale Branham akugwiritsa ntchito mapepala kuwonetsera kukulungiza ndi kusindikiza kwa mpukutu—Mkonzi].

Apa pali chisindikizo chimodzi. Icho ndi chimodzi, ndipo iwe umachikulunga icho mwanjira *iyi,* momwe icho chinkakulungidwira. Ndipo iwe unkachikulunga icho mwanjira iyi. Ndipo, pamapeto, apo pamakhala kachidutswa kakang'ono kakutulukira kunja, monga *chomwecho*. Ndicho chisindikizo choyamba. Chabwino, ndiye, ilo ndiro gawo loyamba la bukhulo. Kenako, chisindikizo chotsatira chimakulungidwa mwanjira *iyi*, cha pambali pa icho. Ndipo icho chinkakulungidwa mwanjira iyi, monga *apa*. Ndiyeno, pa mapeto, cha *apa*, pamakhala china chikutulukira panja. Kutanthauza, zisindikizo ziwiri.

7 Ndipo umo ndi momwe Baibulo lonse linalembedwera, mmipukutu. Ndipo, chotero, ku . . . kumatula Zisindikizo izi, kumatsegula zinsinsi za Bukhulo.

8 Kodi inu munakawerenga mu Yeremiya, momwe iye analembera izo, ambiri a inu mumalemba izo usiku watha? Momwe zisindikizo zimenezo zinkalembedwera ndi kuyikidwa kutali, kuti zikasungidwe, mpaka iye atabwerera zitatha zaka sevente, za ukapolo. Iye anabwereranso ndipo anadzatenga zomwe zinali zake.

9 Ndipo ine ndithudi ndimakonda kuwerenga Izo. Iwe sungathe . . . Palibe njira yofotokozera Izo zonse, chifukwa Iwo ndi Mawu Amuyaya. Ndipo Ili ndi Bukhu Lamuyaya, chotero ife tikuyenera kungokhala ngati tikukhudza malo apamwambawo. Ndipo lero, powerenga, ine ndalemba Malemba ambiri kotero kuti inu mukhoza kuwawerenga Iwo. Ndiponso . . . Ndipo matepiwa akawulula zochuluka za Izo, pamene inu muzikamvetsera. Ndipo muli zinthu zochuluka kwambiri!

10 Ngati ine nditangokwanitsa kuyima pano pa nsanja ndi kuwulula Izo kwa inu, mwanjira yomwe Izo zinawululidwira kwa ine mchipinda, mai, izo zingakhale zopambana. Koma, pamene iwe ufika pano, iwe umakhala wopsyinjika, ndipo iwe umakhala ngati umangozilumpha zinthuzo, ndi kumayesetsa kumangotengera gawo lenilenilo kwa anthu, kuti iwo akhoze kuchiwona Icho.

11 Ine ndithudi ndimayamikira nyimbo ija imene M'bale Ungren wangoyimba kumene; *Kutsika Kuchokera Ku Ulemelero Wake*. Ngati Iye akanapanda kubwera kuchokera ku Ulemelero Wake, ife tonse tikanakhala tiri kuti usikuuno? Chotero ndife othokoza kuti Iye anabwera kuno kuti adzatithandize ife.

12 Tsopano, ndi ambiri ataimirira, ife tingofulumira molunjika kudutsa umu, mo—momwe ife tingathere. Ine sindikuti ife tidutsamo mothamanga, koma ine ndikutanthauza kuti ife tiyamba mofulumira momwe ife tingathere. Ndipo tsopano tiyeni titsegule, tsopano, zitatha . . .

13 Ife takhala tiri ndi mutu wa 1, wa 2, wa 3, ndi wa 4. Ndi wa 5, usiku watha. Ndipo usikuuno ife tikuyambira pa mutu wa 6 wa Chivumbulutso.

14 Tsopano, pamene ife tikuwerenga mutu uwu, ife tikulozera ku malo osiyanasiyana, ngakhale ku Chipangano Chakale ndi Chatsopano, mofanana, chifukwa Bukhu lonseli ndi vumbulutso la Yesu Khristu. Mukuona? Zonsezo limodzi ndi vumbulutso la—la Ambuye Yesu, vumbulutso la Yesu Khristu. Ndi Mulungu, akudziwulula Yekha mu Bukhu; akudziwulula Yekha, kupyolera mwa Khristu, mu Bukhu. Ndipo Khristu ndiye vumbulutso la Mulungu. Iye anabwera kuti adzaulule Mulungu, chifukwa Iye ndi Mulungu anali mmodzi. "Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini." Mwa kuyankhula kwina, inu simukanadziwa chimene Mulungu anali mpaka Iye atadziulula Yekha kupyolera mwa Khristu; ndiye inu mukukhoza kuwona.

15 Ine ndinkakonda kuganiza, zaka zapitazo, kuti mwinamwake Mulungu anali wokwiya nane ine, koma Khristu ankandikonda ine. Ndinadzapeza kuti, ndi Munthu yemweyo, mwaona. Ndipo Khristu ndi mtima kumene wa Mulungu.

16 Ndipo tsopano pamene ife tikuphunzira izi, ife tikufanizitsa izi tsopano. Mabuku atatu oyambirira a Baibulo, a Chivumbulutso, amene ife tawatambasula bwinobwino, ndi mibadwo ya mpingo, a—mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Tsopano ilipo mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, Malipenga Asanu Ndi Awiri, ndi Miliri, ndi—ndi mizimu yoyipa yonga achule, ndipo zonsezi zimayenda limodzi.

17 Mai, momwe ine ndikufunira ndikanakhala nawo a—mapu aakulu opambana, ndi kuzijambula izo pamenepo, momwe ine ndikuziwonera izo, inu mukudziwa, basi momwe chirichonse chikutengera malo ake. Ine ndazijambula izo pa tsamba la pepala laling'ono, koma ine . . . Inu mukuzidziwa izo. Ndipo chirichonse, mpaka apa, chikulumikizana bwino ndendende molondola basi. Ndipo ndi nthawi ndi mibadwo, momwe iyo yabwerera ndi kupita, ndipo chirichonse chalowererana mwangwiro basi. Kotero, izo zonse zikhoza kusakhala molondola, koma ndi zopambana momwe ine ndikudziwira za izo, mulimonse. Ndipo ine ndikudziwa, ngati—ngati ndingachite mopambana, ndipo ine nkulakwitsa pa kuyesetsa kuchita mwa kudziwa kwanga, ndi mopambana momwe ine ndikudziwira, kuti Mulungu ndithudi adzandikhululukira ine pakutero . . . chifukwa cha kulakwitsa ngati ndingachite molakwitsa.

18 Koma, tsopano, mabuku oyambirira atatu amenewo ndi oyamba, Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Ndipo kenako ife tikupeza kuti, mu mutu wa 4 wa Chivumbulutso, Yohane akutengedwera mmwamba. Mukuona? Ife tikuiwona mipingo. Palibe zambiri zikunenedwa zokhudza mibadwo ya mpingo. Apo ndi pamene ine ndikuganiza kuti anthu adabwitsidwa kwambiri. Iwo ali—iwo ali—iwo akukawuyika Mpingo kutali uko mu Chisautso, kwa zinthu izo zimene ziti zidzachitike.

Ndipo monga ine ndinanenera, Lamlungu, dzulo: chinthu choyambirira inu mukudziwa, zisautso zimenezo zidzabweramo, ndipo inu mudzadabwa kuti nchifukwa chiyani sizinati... Choyamba kubwera chimayenera kukhala Mkwatulo. Ndipo zidzakhala monga zakhala zikuchitikira: iwo unachitika ndipo inu simunadziwe izo. Mukuona?

19 Tsopano, palibe zochuluka kwambiri zikulonjezedwa kwa Mpingo umenewo, Mpingo wa Amitundu umenewo, Mkwatibwi. Tsopano, ine ndikufuna kuti musunge mmalingaliro, pali mpingo ndi Mkwatibwi. Mukuona?

20 Inu nthawizonse mumayenera kumazipanga izo ziziyenda mu zitatu; zinai ndi kulakwitsa. Mafirii! Mafirii, maseveni, mateni, mathwelovu, ndi ma twente-foro, ndi maforte, mafifite, manambala osasweka amenewo. Baibulo ndiro...ndipo Mulungu amayendetsa Mauthenga Ake mu—mu mawere-... mawerengero a Baibulo, mmanambala amenewo. Ndipo inu mukapeza chinachake chimene chikuwulukira kutali kwa imodzi ya manambala amenewo, inu kulibwino musamalitse. Icho sichitulukako bwino bwino, pa chinthu chotsatiracho. Muyenera kuchibweretsa icho mmbuyo apa pamene inu munayambira.

21 M'bale Vayle, M'bale Lee Vayle, iye—iye...ine ndikuganiza iye ali pano. Ife tinali kuyankhula tsiku lina za anthu amene akuchoka mu njira. Basi ziri ngati kuwombera pa chandamale. Ngati mfutiyo yakhazikika mwangwiro, yaphunzitsidwa mwangwiro ndi kulunjikidwa, iyo iyenera kuwombera pa chandamale; pokhapokha ngati mpopewo utasuntha, kapena kugwedera, kapena kunjenjemera kuiponyera iyo kumbali, ndipo paliponsepo...kapena kuwomba kwa mphepo. Paliponse pamene iyo ikuyambira, pali njira imodzi yokha yoyenera kuchita, ndiyo kubwerera kumene iyo inasiyira njirayo, ndi kuyambiranso, ngati iyo ili yakuti iwombera chandamale. Ngati iyo siyitero, bwanji, iyo siyimawombera pa chandamale.

22 Ndipo ndi momwe zimakhalira mu kuwerenga Lemba, ine ndikukhulupirira. Ngati tipeza kuti ife tikuyamba chinachake apa, ndipo icho sichikutuluka bwino, inu mukuona kuti icho sichikutero, eya, ife talakwitsa penapake, inu muyenera kubwerera mmbuyo. Inu simudzakhoza kuwaganizira Iwo ndi maganizo anu. Basi sizimatero ayi...

23 Ife tangopeza kumene, mwa Malemba, kuti kulibe munthu Kumwamba, kapena pa dziko lapansi, kapena pansi pa dziko, kapena aliyense amene anayamba wakhalapo konse, kapena ati adzakhalepo konse, yemwe angakhoze kuchita zimenezo. Mwanawankhosa yekha angakhoze kuchita izo. Kotero, kulongosola kwa seminare, chirichonse chomwe chingakhale, sichiri kanthu basi. Mukuona? Izo zimatengera

Mwanawankhosa kuti awulule Iwo, ndizo zonse, kotero ife tikudalira kuti Iye atithandiza ife.

24 Yohane, anatengedwera mmwamba, mu mutu wa 4, kuti akawone zinthu "zomwe zinali, zomwe ziripo, ndi zomwe ziri nkudza." Koma Mpingo ukutsirizitsa pa mutu wa 4. Ndipo Khristu akuwutengera mmwamba Mpingo, kukwatulidwira mu mlengalenga, kukakomana naye Iye, ndipo sukuwonekanso mpaka pa mutu wa 19, pamene Iye akubwerera nawo . . . ngati Mfumu ya mfumu ndi Ambuye wa ambuye, limodzi ndi Mpingo. Ndipo tsopano, oh, ine ndikuyembekeza tsiku lina ife tidzadutsa mu zonsezo, mwinamwake Iye asanabwere. Ngati ife sitidzatero, ife tidzaziwona izo, mulimonse, kotero nzosadandaulitsa.

25 Tsopano, mu mutu wa 5 uwu, kumatula kwa Zisindikizo izi, ndipo tsopano Bukhu losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Choyamba, ife tikufuna kuti tiwerenge Chisindikizo Choyamba.

26 Usiku wathawu, kuti tingoyika maziko a izo mowonjezera pang'ono, ife tikupeza kuti, kuti, pamene Yohane anayang'ana naliwona Bukhu ilo likadali mmanja mwa Mwini wapachiyambi, Mulungu. Kodi inu mukukumbukira momwe Ilo linatayikira? Ndi Adamu. Iye analanditsa Bukhu la Moyo, potenga nzeru za Satana, ndipo anataya cholowa chake, anataya chirichonse; ndipo panalibe njira ya chiwombolo. Kenako, Mulungu, atapangidwa mu chifaniziro cha munthu, anadzatsika nadzakhala Muwomboli kwa ife, kuti adzatiwombole ife.

27 Ndipo tsopano ife tikupeza kuti, mmasiku apitawa, zinthu izi zimene zinali zachinsinsi ziri zoti zidzatsegulidwe kwa ife mmasiku otsiriza.

28 Tsopano ife tikupeza, aponso, mu izi, kuti, mwamsanga pamene Yohane anamva kulengeza uku kwa—Muwomboli Wachibale kuti abwere powonekera ndi kudzapanga zodzinenera Zake, panalibe munthu amene akanakhoza kuchita ichi; panalibe munthu Kumwamba, panalibe munthu pa dziko lapansi, panalibe munthu pansi pa dziko lapansi. Panalibe amene anali woyenera ngakhale kuyang'ana pa Bukhulo. Tangoganizani za zimenezo. Panalibe munthu, nkomwe, woyenera ngakhale kuyang'ana pa Ilo.

29 Ndipo Yohane anangoyamba kulira. Iye ankadziwa kuti, oh, panalibe mwayi wa chiwombolo ndiye. Chirichonse chinalephera.

30 Ndipo mwamsanga ife tikupeza kulira kwake kukuleka, mwamsanga, chifukwa kunalengezedwa ndi chimodzi cha Zamoyo zinayi, kapena akulu, kani. M'modzi wa—wa akuluwo anati, "Usalire, Yohane, pakuti Mkango wa fuko la Yuda walakika," mwakuyankhula kwina, "walakika, ndipo wagonjetsa."

31 Yohane, pochewuka, iye anawona Mwanawankhosa akutulukira. Iye ayenera kuti anali wamagazi ndi wotemedwa ndi wovulazidwa. Iye anali ataphedwa, a . . . ananena, kuti, “Mwanawankhosa amene anali ataphedwa.” Ndipo, zedi, iye anali akadali wamagazi; ngati inu mukanadula mwanawankhosa ndi—ndi kumupha iye momwe Mwanawankhosa uyo analiri, mulimonse. Iye anadulidwa mzidutswa pa mtanda, nthungo mu nthiti, ndipo misomali ili mmanja ndi mmapazi, ndi minga pa zikope. Iye anali mu chikhalidwe chowopsya. Ndipo Mwanawankhosa uyu anatulukira, ndipo anapita kwa Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, amene anali ndi chikalata chaumwini chathunthu cha Chiwombolo. Ndipo Mwanawankhosayo akupita nakatenga Bukhulo kuchokera mdzanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, ndipo linatengedwa, ndipo anatsegula Zisindikizo ndi kudzatsegula Bukhulo.

32 Ndiyeno pamene zinachitika zimenezo, ife tinapeza kuti payenera kuti panali—chinachake chachikulu chimene chinachitika Kumwamba. Pakuti, akuluwo, ndi akulu twente foro, ndi Zamoyozo, ndi—ndi chirichonse Kumwamba, anayamba kufuula, “Mwayenera!” Ndipo apa panabwera Angelo, ndipo anadzatsanulira Mbale za mapemphero a oyera. Oyera pansi pa guwa anafuula, “Woyenera muli Inu, O Mwanawankhosa, pakuti Inu mwatiwombola ife, ndipo tsopano Inu mwatipanga ife kukhala mafumu ndi ansembe, ndipo ife tidzalamulira padziko lapansi.” Oh, mai! Ndipo zinali chomwecho, pamene Iye anatsegula Bukhu limenelo.

33 Inu mukuona, Bukhulo makamaka linakonzedwa ndi kulembedwa asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi. Bukhu ili, Baibulo, kwenikweni linalembedwa asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi. Ndipo Khristu, pokhala Mwanawankhosa, anaphedwa asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi. Ndipo zi—ziwalo za Mkwatibwi Wake, maina awo anaikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi. Koma, Ilo lakhala liri losindikizidwa, ndipo tsopano Ilo likuwululidwa; amene maina awo anali mmenemo, zonse za Ilo, ndipo ndi chinthu chachikulu bwanji.

34 Ndipo Yohane, pamene iye anawona izo, iye—iye anati, “Chirichonse Kumwamba, chirichonse pansi pa dziko lapansi . . .” Chirichonse chinamumva iye akunena, “Ameni, madalitso, ndi ulemu!” Iye basi anali nayo kwenikweni nthawi yopambana, ndipo, pakuti, “Mwanawankhosayo anali woyenera.”

35 Ndipo tsopano Mwanawankhosayo akuimirira. Tsopano, usikuuno, pamene ife tikulowa mu mutu wa 6 uwu, Iye ali nalo Bukhu mdzanja Lake, ndipo akuyamba kuliwululula Ilo.

36 Ndipo, oh, ine ndikanakhoza mwamtheradi lero. . . Ndipo ine ndikuyembekeza kuti anthu ndi auzimu. Ine ndikanakhoza kukhala nako kulakwitsa kowopsya pa Izo, ngati zikanati zisakhale, pafupifupi thwelovu koloko lero, pamene Mzimu Woyera unabwera mchipindamo ndi kudzandikonza ine pa chinachake chimene ine ndinali kulemba kuti ndidzanene.

37 Ine ndinali kuzitenga Izo kuchokera mu zolemba zakale. Ine ndinalibe chirichonse pa Izo. Ine sindikudziwa chomwe Chisindikizo Chachiwiri chiri, osaposanso chirichonse. Koma ndinali nditatenga zolemba zina zakale za chinachake chimene ine ndinachiyankhulapo zaka zingapo zapitazo, ndipo ndinazilemba izo. Ndipo ine ndinali nditasonkhanitsa zolemba izi, zolemba zochokera kwa Dr. Smith, ambiri aakulu, aziphunzitsi odziwika amene ine—ine ndinali nditazisonkhanitsa izo. Ndipo onse a iwo ankakhulupirira zimenezo, kotero ine ndinali nditazilemba izo. Ndipo ndinali kukonzekera kuti ndinene, "Chabwino, tsopano ine ndiwerenga Icho kuchokera pa mfundo imeneyo."

38 Ndipo mmenemo, pafupifupi thwelovu koloko masana, Mzimu Woyera unadzangosesa kutsikira mchipindamo, ndipo chinthu chonsecho basi chinatsegulidwa kwa ine, ndipo Icho chinali pamenepo, mwaona, chotero. . . za ichi—za Chisindikizo Choyamba ichi kukhala chikutsegulidwa. Ndine wotsimikiza basi monga ndaimira pano usikuuno, kuti ichi ndi Choonadi cha Uthenga chimene ine ndikuti ndinene apa. Ine—ine ndikungodziwa kuti ndi zimenezo.

39 Chifukwa, ngati vumbulutso likhala losiyana ndi Mawu, ndiye ilo si Vumbulutso. Ndipo, inu mukudziwa, pali zinthu zina zomwe zimakhoza kuwoneka ngati zoona mwamtheradi, ndipo komabe zisali zoona. Mukuona? Zimawoneka ngati ziri, koma si ziri.

40 Tsopano, ife tikumupeza, Mwanawankhosa ali ndi Bukhu, tsopano. Ndipo tsopano mu mutu wa 6 ife tikuwerenga.

> *Ndipo ndinawona pamene Mwanawankhosa anatsegula chimodzi cha zisindikizo, ndipo ine ndinamva, ngati linali phokoso la bingu,* ndipo *chimodzi mwa zamoyo zinayi chikuti, Bwera udzawone.*
>
> *Ndipo ndinawona, ndipo taonani kavalo woyera: ndipo iye amene anakwera pa iye anali nawo uta; ndipo korona anapatsidwa kwa iye: ndipo iye anapita akugonjetsa, ndi kumagonjetsa.*

41 Tsopano, ndicho Chisindikizo Choyamba, chimene ife titi tiyesere, mwa chisomo cha Mulungu, kuchifotokoza Icho usikuuno. Mwa kukhoza kopambana. . . Ndipo ine ndikuzindikira kuti munthu, kuyesera kuchifotokoza Icho, akuyenda pamalo owopsya ngati iwe sukudziwa chimene ukuchita. Mukuona? Kotero ngati izo zibwere kwa ine mwa

vumbulutso, ine ndikuwuzani inu momwemo. Ngati ine ndingozitenga izo kupyolera mu malingaliro anga omwe, ndiye ine ndidza—ine ndidzakuwuzani izo ndisanayankhule za izo. Koma ndine wotsimikiza basi, pamene ine ndayima pano usikuuno, Icho chabwera mwatsopano kwa ine, lero, kuchokera kwa Wamphamvuzonse. Ine sindimakonda kumangonena zinthu monga chomwecho, pamene izo zifika ku gawo ili la Lemba. Ine—ndine . . .

42 Ine ndikuyembekeza kuti inu mukudziwa chimene ine ndikunena tsopano, mukuona. Tsopano, inu mukudziwa, ndipo iwe sungakhoze kunena zinthu . . . Ngati chinachake chiyenera kukhala chitagona *apa* icho chisanachitike, iwe—iwe sungachinene icho mpaka chinachake chitakachiyika icho pamenepo. Mukuona? Kodi inu mukuwerenga? Kodi inu mukumvetsera kwa chinachake? Mukuona?

43 Tsopano, Bukhu la Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, lokulungidwa tsopano likumasulidwa ndi Mwanawankhosa. Ife tikufika pamalo amenewo usikuuno. Mulungu, atithandife ife. Pamene Zisindikizo zikumatulidwa ndi kumasulidwa, zinsinsi za Bukhulo zikuwululidwa.

44 Tsopano, inu mukuona, *Ili* ndi Bukhu losindikizidwa. Tsopano, ife tikukhulupirira zimenezo, sichoncho ife? Ife tikukhulupira kuti Ilo ndi Bukhu losindikizidwa. Tsopano, ife sitimazidziwa izi mmbuyomu, koma Ilo liri. Ilo ndi losindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Ndiko kuti, kuseri kwa Bukhulo, Bukhulo ndi losindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri.

45 Ngati ife tikanamayankhula za bukhu la mtundu *uwu,* izo zikanakhala ngati kuyika chingwe pa ilo, zingwe zisanu ndi ziwiri. Koma ilo si bukhu la mtundu *uwu*.

46 Ilo ndi mpukutu. Ndiyeno pamene mpukutu ufutukulidwa, icho ndi chimodzi; ndiye mkati mwa mpukutumo muli nambala thuu. Ndipo cha *apa* Ilo likunena chimene Icho chiri, koma Icho ndi chinsinsi. Koma, komabe, ife talifufuza Ilo; koma, kumbukirani, Bukhulo ndi losindikizidwa. Ndipo Bukhulo ndi Bukhu la chinsinsi, cha chivumbulutso. Ilo ndi vumbulutso la Yesu Khristu, mwaona, Bukhu la mavumbulutso. Ndipo tsopano inu mukudziwa, kutsika kudutsa mu m'badwo, munthu wakhala akufufuza ndipo wayesetsa kuti alowe mu Izo. Ife tonse tatero.

47 Ndipo, komabe, nthawi ina, ine ndikukumbukira . . . Ngati—ngati Bambo Bohanon angakhale ali pano, kapena—kapena ena a anthu ake, ine—ine sindikutanthauza izo mwa kunyoza kulikonse. Bambo Bohanon ndi mzanga wapachifuwa, ndipo iye anali supatendanti wa Ntchito za Boma pamene ine ndinkagwira ntchito kumeneko. Pamene ndinapulumutsidwa koyamba, ine ndinali kumuuza iye za kuwerenga Bukhu la Chivumbulutso. Iye anati, "Ine ndinayesetsa kuwerenga chinthu chimenecho,"

iye anati. Ndipo Bambo Bohanon anali munthu wabwino, ndipo iye—iye anali membala wa mpingo. Ndipo—ndipo sindikudziwa kuti iye anali wa uti, koma iye anati, "Ine ndikuganiza kuti Yohane ayenera kuti anali atadya chakudya chamadzulo cha tsabola waukali usiku umenewo, ndipo anapita kukagona ndi mimba yokhuta."

48 Ndinati kwa iye, ngakhale izo zikanakhoza kuthetsa ntchito yanga, ine ndinati, "Kodi inu simukuchita manyazi kuyankhula zimenezo?" Ndipo ine ndinali mnyamata chabe. Koma ine ndinati, "Kodi inu simukuchita manyazi kunena zimenezo zokhudza Mawu a Mulungu?" Mukuona? Komabe, ndipo ndiri kamwana chabe, wosadutsa zoyambirira . . . mwinamwake usinkhu wa zaka twente-wani, twente-thuu; ndipo ntchito zikusowa, ndipo kuli mavuto a zachuma. Koma, komabe, munali mantha mmenemo, pamene ine . . . zopotozedwa, ndinkamva kupotoza kulikonse kokhudza Mawu a Mulungu. Iwo ndi Choonadi; Choonadi chonse. Chotero, ilo silinali loto nkomwe kapena kubwebweta; sichinali chimene Yohane anadya.

49 Iye anali pa Chisumbu cha Patmo chifukwa iye ankayesetsa kuti awayike Mawu a Mulungu mu mawonekedwe a bukhu, ndipo anatengedwera ku ukapolo kumeneko ndi boma la Chiroma. Ndipo anali pa chisumbu, pa Tsiku la Ambuye. Ndipo iye anamva kumbuyo kwake Liwu la madzi ambiri, ndipo anapotoloka kuti awone, ndipo anawona Zoyikapo nyali Zagolide Zisanu Ndi Ziwiri. Ndipo apo panayima Mwana wa Mulungu, pakati pa izo, tsopano.

50 Ndipo, ndiye, Bukhulo ndi vumbulutso. Chotero, vumbulutso ndi chinachake chimene chazindikiritsa za chinachake, chinachake chomwe chawululidwa. Ndipo tsopano, zindikirani, kuchitira kuti musayiwale izo, ilo ndi "lotsekedwa mpaka nthawi za mtsogolo." Mukuona? Chinsinsi chonse cha Ilo ndi "chotsekedwa mpaka nthawi za mtsogolo." Ife tikuzipeza izo mu Lemba apa.

51 Tsopano, chinsinsi cha Bukhulo chikuwululidwa pamene Zisindikizo zikumatulidwa. Ndipo pamene Zisindikizo zamatulidwa kwathunthu, nthawi ya chiwombolo yatha; chifukwa Mwanawankhosa wachoka mu bokosi lopembedzera, kuti ayende kukatenga zodzinenera Zake. Iye anali Mkhalapakati, pakati pa izo. Koma pamene vumbulutso lenileni likuchitika pa Zisindikizo, pamene Izo zikuyamba kumatulidwa, Mwanawankhosa akubwera kuchokera ku malo opatulika. Izo ziri molingana ndi Mawu. Ife tinawerenga izo usiku wathawu. Iye anabwera kuchokera ku . . . kuchokera pakati pake, ndipo anadzatenga Bukhulo, kotero Iye salinso konse Mkhalapakati. Chifukwa, ngakhale iwo anamutcha Iye Mkango, ndipo ndiyo—ndiyo Mfumu, ndipo Iye si Mkhalapakati pamenepo.

52 Ngakhale, ochita sewero a mu Zisindikizo izi akuyambira ku m'badwo wa mpingo woyamba. Tsopano muzikumbukira, kuchitira kuti—inu mumvetse maziko a izi bwinobwino, ngati ife tingathe, kapena momveka bwino mmene tingathere. "Ochita sewero," ine ndikuziyika izo chomwecho chifukwa chakuti wochita sewero ndi munthu amene amasintha zigoba. Mukuona?

53 Ndipo mu kuchita uku, usikuuno, ife tiwona kuti ndi Satana akusintha chigoba chake. Ndipo, onse, ochita sewerowo.

54 Khristu, akuchita gawo limene Iye anachita, pamene Iye anasandulika kuchokera ku Mzimu nadzakhala munthu, Iye anangovala chovala cha wochita sewero, thupi laumunthu, ndipo anabwera pansi mmawonekedwe a Munthu, kuti adzakhale Muwomboli Wachibale.

55 Tsopano—tsopano, inu mukuona, ndi mawonekedwe chabe a wochita sewero. Ndi chifukwa chake izo zonse ziri mu mafanizo ndipo sy-. . . ndi momwe izo ziriri apa, monga zamoyo, ndi zinyama, ndi zina zotero. Izo ziri mu sewero. Ndipo ochita sewero awa akuyambira mu m'badwo wa mpingo woyamba, chifukwa uyo anali Khristu kudziwulula Yekha kwa mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Tsopano inu mukumvetsetsa izi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Mukuona? Khristu akudziulula Yekha kwa mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo.

56 Kenako, kudutsa mmibadwo ya mpingo iyi, muli chisokonezo chachikulu chikutsatira. Ndiye, pamapeto a m'badwo wa mpingo, Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri uli woti udzatenge zinsinsi zotayika izi ndi kudzazipereka izo kwa Mpingo. Mukuona? Tsopano ife tizizindikira zimenezo.

57 Koma m'nthawi imeneyo sizinawululidwe mu chikhalidwe chake chenicheni. Tsopano, mu nthawi za Baibulo, zinsinsizi zinali kumeneko, ndipo iwo ankaziwona zinthu izi zikuchitika mwanjira yomwe Yohane anaziwonera zimenezo apa. Tsopano iye anati, "Pali wokwera pakavalo woyera." Koma, chomwe chinsinsi chake chiri, pali chinsinsi chimene chikupita ndi wokwerayo. Tsopano, chimene icho chinali, iwo sankadziwa, koma icho chiri choti chiwululidwe. Koma izo ziri zoti zidzaululidwe Mwanawankhosa akadzachoka pa Mpandowachifumu wa Atate, wa kupembedzera Kwake monga Muwomboli Wachibale.

58 Ine ndigwetseramo kakang'ono kenakake umu. Tsopano, ngati aliyense ati adzatenge matepi awa. . . Munthu aliyense akhoza kuyankhula chirichonse chimene iye akufuna. Iye ali nawo ufulu kwa chirichonse cha malingaliro ake. Koma ngati. . . Inu mukudziwa, ngati mtumiki sakuwafuna iwo pakati pa anthu ake, ndiye muwauze iwo kuti asawatenge iwo. Koma ine—ine. . . Awa ndi a kwa pakati pa anthu amene ine ndatumidwa

kuti ndidzayankhule kwa iwo, chotero ine ndiyenera kuwulula chimene chiri Choonadi. Mukuona?

59 Tsopano, Mwanawankhosa, mu nthawi ya kupembedzera kumbuyo *apa*, Iye ankadziwa kuti munali maina mmenemo amene analembedwamo kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Ndipo malingana ngati maina amenewo anali asanawonetseredwebe pa dziko lapansi, Iye amayenera azikhala pamenepo ngati Wopembedzera. Kodi inu mukumvetsa zimenezi? Mwangwiro, kukonzedweratu! Mukuona? Chabwino. Iye amayenera azikhala pamenepo, chifukwa Iye anabwera kudzawafera iwo amene Mulungu anali atawadzozeratu ku Moyo Wamuyaya. Mukuona? Mukuona? Mwa kudziwiratu Kwake, Iye anawawona iwo. Osati mwa chifuniro Chake Chomwe; Chifuniro chake chinali chakuti pasadzakhale aliyense wotayika. Koma mwa kudziwiratu Kwake Iye ankadziwa amene akanadzakhoza ndi amene sakanadzakhoza. Chotero, malingana ngati panali dzina limodzi limene silinali, linali lisanatchulidwe padziko lapansi apobe, Khristu amayenera azikhala pamenepo monga Wopembedzera, kuti asamalire dzina limenelo.

60 Koma mwamsanga pamene dzina lotsiriza ilo laponyedwa mu Clorox ameneyo kapena bulitchi, ndiye kuti masiku Ake opembedzera atha. "Muloleni iye amene ali woyipa akhalebe chiyipire. Msiyeni iye amene ali woyera, akhalebe chiyerere." Mukuona? Ndipo Iye akuchoka m'malo opatulikawo ndipo potero iwo akusandulika Mpando Wachiweruzo. Tsoka kwa iwo amene ali kunja kwa Khristu pamenepo!

61 Tsopano zindikirani, koma Izo ziyenera kudzawululidwa pamene Mwanawankhosa akuchoka pa malo Ake opembedzera kuchokera kwa Atate. Tsopano, ameneyo ndi Chivumbulutso 5. Tsopano Iye akutenga Bukhu la Zisindikizo, Bukhu la Zisindikizo, kapena Bukhu losindikizidwa ndi Zisindikizo, akuzimatula izo ndipo akuziwonetsa izo. Penyani. Pa mapeto a m'badwo tsopano, kupembedzera kutatha, mibadwo ya mpingo yatsirizika.

62 Iye akudzabwera mkati, mu m'badwo woyamba, M'badwo wa Aefeso; anawulula, anatumiza mtumiki.

63 Muwone zimene zinkachitika, pamene ife tikupitirira. Apa pali dongosolo la zimenezo. Chinthu choyamba chikuchitika, apo pali ku—ku—kulengeza Mmiyamba, poyamba. Chikuchitika ndi chiyani? Chisindikizo chatsegulidwa. Ndi chiyani chimenecho? Chinsinsi chafutukulidwa. Mukuona? Ndipo pamene chinsinsi chafutukuka, kenako lipenga likudzawomba. Ilo likulengeza nkhondo. Mliri ukugwa, ndipo m'badwo wa mpingo ukutsegulidwa. Mukuona?

64 Kodi gawo la "nkhondo" ndi liti? Mngelo wa Mpingowo amagwira chinsinsi cha Mulungu, chisanawululidwebe kwathunthu. Koma, pamene iye atero, iye amagwira chinsinsi

ichi cha Mulungu, ndipo kenako iye amapita kwa anthu chinsinsi ichi chitaperekedwa kwa iye. Amapita kwa anthu! Iye amakachita chiyani kunja uko? Iye amakayamba kulengeza Uthenga umenewo. Ndipo iwo umakayambitsa chiyani? Nkhondo, nkhondo yauzimu.

65 Ndipo kenako Mulungu amamutenga mtumiki Wake, limodzi ndi Osankhidwa a m'badwo umenewo, ndipo amakawayika iwo pambali, azigona. Ndipo kenako Iye amagwetsa mliri pa iwo amene anawukana Iwo; chiweruzo chakanthawi.

66 Ndiyeno izo zikatha, ndiye izo zimapitirirabe, ndipo iwo amapanga bungwe, ndi kubweretsamo zipembedzo, ndipo amayamba ndi ntchito ya munthu ameneyo, monga ya Wesley ndi ena onse a iwo. Ndiyeno zonsezo zimafika mu chisokonezo kachiwiri.

67 Ndipo zikatero chinsinsi china chimadza. Ndiye chimachitika ndi chiyani? Mtumiki wina amafika pa dziko lapansi, kwa m'badwo wa mpingo. Mukuona? Ndiye, pamene iye afika, iye—lipenga limawomba. Iye amalengeza nkhondo. Mukuona? Ndiyeno chimachitika ndi chiyani? Potsiriza, ndiye, iye amachotsedwapo. Ndipo kenako pamene iye wayikidwa pambali, ndiye mliri umagwa, nkuwaononga iwo. Imfa yauzimu imakantha mpingo, ndipo iwo wapita, gulu limenelo.

Kenako Iye amapita kwa wina. Oh, ndi dongosolo lopambana!

68 Mpaka, izo zikufika kwa mngelo wotsirizayo. Tsopano, iye alibe chinsinsi chinachake. Koma iye akusonkhanitsa zonse zomwe zinatayika mmibadwo inayo, Zoonadi zonse zomwe zinali zisanawululidwe mowona apobe, mwaona, pamene vumbulutso likubwera, ndiye iye akuwulula zinthu zimenezo mu tsiku lake. Ngati inu mukufuna kuti muwerenge zimenezo, ndi izo apo. Chivumbulutso 10, 1 mpaka . . . 1 mpaka pafupifupi 4, inu muzipeza izo. Chabwino. Mukuona? "Akutenga Bukhulo ndipo, la Zisindikizo, ndipo akumatula izo," ndipo akumuwonetsa mngelo wachisanu ndi chiwiri; pakuti izi zokha, zinsinsi za Mulungu, ndizo utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri. Tsopano, ife tangodutsa kumene mu mibadwo ya mpingo, ngakhale ndi mbiriyakale, ndipo tatsimikizira zimenezo. Mukuona? Iwo ndi—Uthenga wa mngelo, wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, chabwino, akuwulula zinsinsi zonse zomwe zakhala mmbuyomu, zinthu zonse za mmbuyo. Chivumbulutso 10:1-7, ndizo ziti zidzachitike. Tsopano, kumbukirani, "Mmasiku a mngelo wachisanu ndi chiwiri, kuwomba kwake, kuwomba lipenga la Uthenga, iye ndi wakuti adzatsirizitse zinsinsi zonse za Mulungu."

69 Monga ngati, apa iye akubwera, mmibadwo yoyambirira ya mpingo. Ife tizimvetsa zimenezo, pakapita kanthawi,

chiphunzitso. Ndipo, kenako, chinadzakhala chonenedwa, poyamba; kenako chiphunzitso; ndipo kenako chinadzakhala lamulo; kenako chinadzasanduka mpingo, ndi kudutsa mmibadwo ya mdima.

70 Kenako kuchokera mmibadwo ya mdima kunadzabwera kukonzanso koyamba, Luther. Ndipo iye anabweretsa, limodzi naye, mitundu yonse ya zinthu zachinsinsi zimene zinachitika mu m'badwo wa mpingo umenewo, zonse zinali mmbuyo umo ndiye, koma iye sanatsirizitse izo.

71 Kenako motsatira panadzabwera Wesley, ndi kuyeretsedwa, anatenga zina zochuluka za izo. Komabe, sanatsirize izo; anasiya mbali zomasuka paliponse, monga ngati kukonkha m'malo mwa ubatizo. Ndipo Luther anatenga "Atate, Mwana, Mzimu Woyera" m'malo mwa "Ambuye Yesu Khristu." Zinthu zonse izi zosiyanasiyana!

72 Kenako motsatira panadzabwera m'badwo wa Chipentekoste, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo iwo anayanga pa zimenezo. Tsopano, sipangakhalenso mibadwo ina. Iyo ndi yonse ya iyo. Ndi wa Filadefiya . . . kapena, tsopano, M'badwo wa Laodikaya. Komano . . .

73 Ife tinapeza, mu kuwerenga kwa Lemba, kuti mtumiki wa m'badwo amadza kumapeto a m'badwo komwe, nthawi zonse. Paulo anadzabwera kumapeto a m'badwo. Ife tikupeza kuti Ireniyasi anadzabwera kumapeto a m'badwo. Martin, kumapeto a m'badwo. Luther, kumapeto a m'badwo wa Chikatolika. Ndipo (chiyani?) Wesley kumapeto a m'badwo wa Chilutera. Ndipo Chipentekoste kumapeto a m'badwo wa kuyeretsedwa, kupita ku ubatizo wa Mzimu Woyera.

74 Ndipo pamapeto a m'badwo wa Chipentekoste, ife tikuyenera kulandira, molingana ndi Mawu, monga Mulungu andithandizire ine usikuuno kuti ndikuwonetseni inu, kupyolera apa, kuti ife ndi oti tiwona, tilandira mtumiki amene ati adzatenge mbali zonse zomasukazo kunja uko ndi kudzawulula chinsinsi chonse cha Mulungu, kuti Mpingo ukwatulidwe.

75 Ndiye kenako apo padzabwera Mabingu asanu ndi awiri achinsinsi amene sanalembedwe nkomwe. Uko nkulondola. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti, kudzera mu Mabingu Asanu Ndi Awiri amenewo, adzawululidwa mmasiku otsiriza kuti adzamubweretse Mkwatibwi palimodzi ku chikhulupiriro chokwatulitsa. Chifukwa, zimene ife tiri nazo pakali pano, ife—ife sitingakhoze kuti tichite zimenezo. Pali chinachake. Ife tiyenera kusunthira patsogolo. Ife, ife tikulephera kukhala nacho chikhulupiriro chokwanira cha machiritso Auzimu, nkomwe. Ife tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro chokwanira kuti tidzasinthidwe, mkamphindi, ndi kudzasesedwera mmwamba kuchoka padziko lapansi ili. Ndipo ife tizipeza

izo, pakapita kanthawi, Ambuye akalola, tidzapeza pamene Izo zinalembedwa.

76 Kenako, ziweruzo zonse za awa ochita zoyipa! Tsopano, penyani, kutsika kudutsa mmibadwo ya Zisindikizo izi, zakhala zikumatulidwa, kufikira tsopano Chisindikizo chotsiriza chikumatulidwa. Ndipo tsopano monga iwo—monga iwo akhala akuyang'anira pa Zisindikizo izi ndipo nkumangopenekera basi, kupenekera zomwe iwo anali kuchita. Tsopano, pamapeto a mibadwo, a mibadwo ya mpingo, onse awa ochita zoipa adzatenga malo ndipo adzalunjika mu Chisautso; onse ochita zoipa awa a Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, amene akhala akuchita mwachinsinsi mu mpingo.

77 Ndipo ife tipeza, mu miniti, kuti izo zimagwira ntchito ngakhale mu dzina la mpingo. Iwo amadzitcha okha, "Mpingo." Ndipo inu mungoona ngati izo siziri zolondola. Nzosadabwitsa kuti ine ndakhala ndiri wotsutsa chipembedzo kwambiri, osadziwa chifukwa chake. Mukuona? Mukuona?

78 Iwo akutsirizira. Tsopano, izo zikuyambira mmbuyo apa mwa mawonekedwe opanda mphamvu, ndipo zikungopitirira kuyipira yipirabe, mpaka mmusi kufikira. . . Ndipo anthu analowa mpaka mu izo, kumati, "Oh, inde, *izi* ziri bwino basi." Koma mmasiku otsiriza, zinthu izi zikupangidwa kudziwika. Ndipo iwo potsiriza akupita moyipa kwambiri mpaka iwo akukalowa mpaka mu nthawi ya Chisautso.

79 Ndipo munthu anganene bwanji kuti Mkwatibwi wa Khristu akupita mu Chisautso? Ine sindingamvetse zimenezo. Mukuona? Iye wachotsedwa ku Chisautso. Ngati—ngati Mpingo waweruzidwa, ndipo iwo adziweruza okha ndipo avomereza Magazi, ndiye Mulungu angamuweruze bwanji munthu yemwe ali mwangwiro, mwathunthu wopanda tchimo?

Inu mukuti, "Palibe munthu woteroyo."

80 Wokhulupirira aliyense wobadwa-mwatsopano, wokhulupirira woona, amakhala wangwiro, mwamtheradi wopanda tchimo pamaso pa Mulungu. Iye samadalira mu ntchito zake; mu Magazi a Yesu, mmene kuvomereza kwake kwagwetsedweramo. Baibulo limanena chomwecho. Mukuona? "Iye amene—amene wabadwa mwa Mulungu samachimwa, pakuti iye sangakhoze kuchimwa." Inu mungamupange bwanji munthu kukhala wochimwa pamene bulitchi ya Magazi a Yesu Khristu ili pakati pa iye ndi Mulungu? Iyo ingakhoze kumwaza tchimo mpaka sipangakhale kanthu kotsalira ka ilo. Mukuona? Magazi angwiro awo a Khristu angalole bwanji tchimo kudutsa pamenepo? Iye sangatero.

81 Yesu anati, "Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu a Kumwamba ali angwiro." Ndipo ife tingaliyambe bwanji nkomwe lingaliro la kukhala angwiro? Koma Yesu

anawufuna iwo. Ndipo ngati Yesu anawufuna iwo, Iye ayenera kukonza njira ya iwo. Ndipo Iye anatero; Magazi Ake Omwe!

82 Tsopano, zonse, akuwulula zinsinsi zonse zomwe zapita kale mmbuyomo. Tsopano, lingalirolo liri, apa pa nthawi yotsiriza, kuti zinsinsi zomwe zinayambira mmbuyo kale uko ndipo zabwera kudutsa mmibadwo ya mpingo, ziri zoti ziwululidwe apa pa kumatulidwa kwa Zisindikizo, kuno mmasiku otsiriza, nthawi ya kupembedzera itangotsala pang'ono kuti ithe, pa nthawi imeneyo.

83 Ndiye, ziweruzo zikuyembekezera iwo amene ali mmbuyo. Iwo akupitirira kukalowa mu zimenezo. Izo zidzachitika Mkwatibwi akadzati wachotsedwa powonekera.

84 Oh, tiyeni tingowerenga Lemba. Inu nonse mumakonda kulemba ena a Malemba? Tiyeni titenge Atesalonika Wachiwiri, mphindi yokha, ndipo tiyang'ane apa miniti yokha. Icho—icho ndi chithunzi chokongola chotero apa! Ine ndimachikonda icho. Ndipo tiyeni tiwone. Inde, Atesalonika Wachiwiri. Ndipo ine ndikufuna mutu wa 2 wa Atesalonika Wachiwiri, ndipo ya—ndime ya 7. Tiyeni tiwone. Atesalonika Wachiwiri 2:7. Ine ndikuganiza uko nkulondola, tsopano. Ine ndimalemba izi, ndikunjenjemera ndi kumagwedezeka.

> *. . .chinsinsi cha kusaeruzika chayamba kale kugwira ntchito: iye yekha amene. . .amaloleza adzamulola, mpaka iye adzachotsedwe pa njirayo.*

85 Ndani? "Iye amene amaloleza." Mukuona? Mwaona, chinsinsi, "chinsinsi cha kusaeruzika," kumbuyo komwe uko mu m'badwo wa mpingo woyamba womwe apa. Apa pali Paulo akulemba, akunena kuti, "Chinsinsi cha kusaeruzika." Kusaeruzika ndi chiyani? Kusaeruzika, ndi chinachake chimene iwe umadziwa kuti suyenera kuchita, ndipo iwe nkuchichita icho mulimonse. Ndipo Paulo anati alipo oterowo mu dziko lapansi lero, ochita kusaeruzika. Oh, ngati inu. . .Ife tifika ku. . .Tiyeni tingowerenga chidutswa chimenecho, miniti chabe. Tiyambire patali pang'ono, ndime ya 3.

> *Musalole kuti munthu aliyense akunyengeni inu mwa njira iliyonse: pakuti tsiku limenelo silidzabwera, pokha pokha patadzabwera kugwa poyamba, ndipo uyo* (m-u-n-t-h-u) *munthu wa tchimo adzaululidwe, mwana wa chitayiko;* (uko nkulondola)
>
> *Amene* amatsutsa *ndi* kudzikuza *yekha pamwamba pa zonse zotchedwa Mulungu, kapena amene akupembedzedwa; kotero kuti iye monga Mulungu akukhala mu kachisi wa Mulungu,* kumadziwonetsera *yekha kuti iye ali Mulungu,* kumakhululukira machimo.
>
> *Simukukumbukira inu kodi, kuti, ine pamene ndinali ndi inu, ine ndinakuuzani inu zinthu izi?*

86 Ine ndikanakonda nditakhala pansi pa kuphunzitsa kwake kwina. Simukanakonda inu?

> *Ndipo tsopano* inu *mukudziwa chimene chikulepheretsa kuti iye akhoze kuwululidwa mu nthawi yake.*

87 Osati nthawi imeneyo, mwaona, osati nthawi imeneyo; koma, "mu nthawi yake," mukuona, pa kumatula kwa Chisindikizo chimenecho. Ife tikanazadziwa ndendende chimene icho chinali. Ndi ndani munthu wa kusaeruzika uyu? Ndi ndani munthu wa tchimo uyu, munthu uyu amene akuchita kusaeruzika? "Koma iye adzaululidwa mu nthawi yake."

> *Pakuti chinsinsi cha kusaeruzika chikugwira kale ntchito* (onyenga, mukuona, kuwanyenga anthu kuwasocheretsera mu chinachake, mwaona): *iye yekha* (Mulungu) amene *amaloleza adzamulola, mpaka iye* (Mpingo, Khristu, Mkwatibwi) *atachotsedwa pa njirayo.*
>
> *Ndipo zikadzatero Wochimwa* uyo *adzawululidwa,. . .*

88 Pa kumatula kwa Chisindikizo, "pa nthawi yake." Paulo anati, "Osati mu nthawi yanga, koma mu nthawi imene iye ati adzawululidwe." Mukuona?

> *. . .amene Ambuye ati adzamuwononge ndi mzimu wa pakamwa pake,. . .*

89 Ife tifika ku zimenezo pakapita kanthawi, "mzimu wa pakamwa pake." Muwone chomwe icho chiri.

> *. . .ndipo adzamuwononga nako kuwala kwa kudza kwake:*
>
> *Ngakhale iye, amene kudza kwake kuli monga mwa machitidwe a Satana. . .*

90 Iye, "iye," munthu amene machitidwe ake ali onga machitidwe a Satana.

> *. . .ali ndi mphamvu zonse ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zabodza,*
>
> *Ndipo ndi chinyengo chonse cha chosalungama,* kumawanyenga anthu ndi kusalungama, *mwa iwo amene akuwononge ka* (osati Mkwatibwi uyu), mwa iwo amene akuyang'anira chinthu chotere; *chifukwa iwo sanalandire chikondi cha choonadi,. . .*

91 Ndipo Khristu ali Choonadi, ndipo Khristu ndi Mawu; koma iwo amasankha kukhala ndi kachikhulupiriro. Huh! Mukuona?

> *. . .kuti iwo akhoze kupulumutsidwa.*
>
> *Ndipo chifukwa cha ichi Mulungu* watumiza *kwa iwo* zosocheretsa *zaukali, kuti iwo akhulupirire a—bodza:*

92 Izo ziyenera kutanthauziridwa pamenepo, momwe ine ndinawonera mu lexicon, "chi bodza," osati "ka bodza." "Chi bodza," lomwelo limene iye anamuwuza Eva.

> *Kuti iwo . . . akhoze kuwonongeka amene sanakhulupirire choonadi, koma anali ndi chisangalatso mu kusalungama.*

93 Ndi maneno otani! Mai! Mkwatibwi akadzachotsedwa, ndiye munthu wa tchimo uyu adzadziwulula yekha.

94 Iye, Mkwatibwi woona wa Khristu, wasankhidwa kuchokera mu m'badwo wa mpingo uliwonse.

95 Tsopano, tsiku lina ine ndinapanga neno, "Mkwatibwi akhoza kupita Kwawo ndipo inu simudzadziwa kanthu za icho." Izo ndi zoona.

96 Winawake anati, "Chabwino, M'bale Branham, ilo lidzakhala gulu laling'ono lamphamvu."

97 Yesu anati, "Monga zinakhalira mmasiku a Nowa," tsopano inu muyankhule naye Iye za zimenezo, mwaona, "mmene miyoyo eyiti inapulumutsidwa ndi madzi, momwemonso zidzakhala mu Kudza kwa Mwana wa munthu." Ngati atakhalapo eyiti handiredi atapita mu Mkwatulo usikuuno, inu simungadzamve zonena za izo mawa, kapena tsiku lotsatira, kapena nthawi iliyonse. Iwo angakhale atapita ndipo inu simungadziwe kanthu za izo. Mwaona, chingakhale chinthu chomwecho basi.

98 Kodi ine ndikuyesera kunena chiyani? Ine sindikuyesera kuti ndikuwopsyezeni inu, kukudandaulitsani inu. Ine—ine ndikufuna kuti inu mukhale mutayima ndi zala zanu. Mukhale okonzeka, mukuyang'anira, miniti iliyonse. Siyani zamkutu zanu. Mungokhala pa ntchito ndi Mulungu, chifukwa ndi mochedwa kuposa mmene inu mukuganizira.

Tsopano, inu muzikumbukira, Mkwatibwi woona!

99 Tsopano, alipo mkwatibwi wabodza. Ife tizipeza zimenezo mu Chivumbulutso 17. Iye anati, "Ine ndine mkazi wamasiye, ndipo sindisowa kanthu," mukuona, atakhala pa chirombo cha mtundu wofiira ichi, ndi zina zotero, chirombo, kani.

100 Tsopano, koma Mkwatibwi woona adzapangidwa mwa masauzande kuchulukitsa ndi masauzande a anthu, koma adzakhala Osankhidwa ochokera mu m'badwo wa mpingo uliwonse. Nthawi iliyonse imene uthenga uperekedwa, ndipo anthu nkuwukhulupirira iwo nawulandira iwo mu Kuwala kwake konse, pamene iwo anasindikizidwa kufikira Tsiku lija la Chiwombolo.

101 Kodi Yesu sanaphunzitse chinthu chomwecho, pamene Iye anati, "A—mfuu unamveka mu—ulonda wachisanu ndi chiwiri"? Ndiwo m'badwo wa mpingo wotsiriza. Mukuona? Ndipo anati, "Taonani, Mkwati akudza; tulukani mukakumane naye Iye."

102 Ndiye kenako namwali wogona anadza, anapukuta maso ake, ndipo anati, "Ndikuganiza kuti ine ndiyenera kukhala nawo ena a Mafuta amenewo, nanenso, kotero mwinamwake inu mungakhale nawo ena."

103 Ndipo Mkwatibwi weniweni, woona atayima pamenepo, anati, "Ife tangotsala nawo otikwanira tokha. Uh-huh. Ife tangotsala nawo okwanira kuti tilowemo, ifeeni. Ife sitingakupatseni inu kalikonse. Ngati inu mukufuna ena, inu pitani mukapemphere."

104 Ndipo pamene iye anali atapita, Mkwati anabwera, ndipo Mkwatibwiyo analowa mkati. Ndiyeno otsalirawo pamenepo, iwo amene anali amakhalidwe abwino mwamtheradi, mpingo, anasiyidwa kunja. Ndipo Iye anati, "Uko kudzakhala kulira, ndi kubuula, ndi kukukuta kwa mano."

105 Mwaona, tsopano, amenewo ndi Osankhidwa. Ndipo pamene mfuu unamveka, "Mkwati akubwera," ndiye mmodzi aliyense wa iwo amene anagona kudutsa mmibadwo iyo, anawuka, aliyense. Mwaona, izo si Mulungu, monga ife tingaganizire, kungopita kukamusakira Iye anthu sauzande apang'ono a m'badwo uno ndipo nkuwatenga iwo. Ndi Osankhidwa omwe kuchokera mu m'badwo uliwonse. Ndipo ndicho chifukwa chake Khristu ayenera kukhala pa mpando wa umkhalapakati kumbuyo kuno, monga Wopembedzera, kufikira mmodzi wotsiriza uyo atadzalowamo pa m'badwo wotsiriza. Ndipo mavumbulutso awa ndiye, a zomwe zakhala ziri, akumatukira pa anthu, ndipo iwo akuwona zomwe zinachitika. Mukuona? Inu mukumvetsa izo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino.

106 Zindikirani, "Ena onse akufa," mamembala a mpingo, "sanakhalenso moyo kufikira zaka wani sauzande zitatha." Mamembala a mpingo, a—Akhristu, mpingo, sunakhalenso moyo mpaka kumapeto kwa zaka sauzande. Ndipo kenako iwo anadzatulukira kuti adzaime pamaso pa Mkwatibwi, ndiko kulondola, kudzaima pamaso pa Mfumu ndi Mfumukazi. Ulemelero!

Mpingo wina lero umadzitcha wokha, "Mfumukazi ya Kumwamba."

107 Mfumukazi ya Kumwamba ndi Mkwatibwi wosankhidwa wa Khristu, ndipo Iye akubwera limodzi ndi Iye. Daniele anawona zimenezo, ndipo anati, "Ma teni sauzande kuchulukitsa ndi ma teni sauzande anatumikira kwa Iye." Tsopano ngati inu mungaliyang'ane Lembalo pamenepo, mu Daniele, "chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo mabuku anatsegulidwa." Tsopano kumbukirani, pamene Iye anadza, Iye anadza naye Mkwatibwi Wake. Mkazi amatumikira kwa mwamuna wake. "Ndipo ma teni sauzande kuchulukitsa ndi ma teni sauzande a masauzande anatumikira kwa Iye. Chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo

mabuku anatsegulidwa." "Ndipo bukhu lina linatsegulidwa, limene liri bukhu la Moyo," osati Mkwatibwi, nkomwe. Iye wapita kale mmwamba ndipo wabweranso, ndipo akuyima pamenepo mu chiweruzo cha mibadwo imeneyo imene inakana Uthenga Wabwino.

108 Kodi Yesu sanati? "Mfumukazi ya Kummwera idzawuka nawo m'badwo uno mmasiku ake, a Chiweruzo, ndipo idzawutsutsa m'badwo uno; pakuti iye anachokera ku malo akutali a dziko lapansi, kudzamvera nzeru za Solomoni, ndipo woposa Solomoni ali pano." Apo panayima—chiweruzo, mfumukazi ya—ya ku Sheba, ya Kummwera, inayima pamenepo mu Chiweruzo, ndi umboni wake womwe.

109 Panalibe ngakhale Myuda amene anawuka nawo m'badwo umenewo amene anali Ayuda. Ndipo iwo anali akhungu, ndipo anamuphonya Iye. Chifukwa, iwo anali akumuyembekezera Iye, koma Iye anabwera mophweka kwambiri mwakuti iwo anapita pamwamba pomwe pa izo, monga chomwecho.

110 Ndipo, uko, mfumukazi yaikulu ija inadzichepetsa yokha, ndipo inadza ndi kudzavomereza uthenga. "Ndipo iye adzayima mu Chiweruzo," Iye anatero, "ndi kudzawutsutsa m'badwo umenewo."

111 Tsopano inu mukuona magulu atatuwo, nthawizonse. Bukhu, akufa anaweruzidwa; bukhu lina, bukhu la Moyo, iwo amene anali nawo maina awo mu bukhu la Moyo.

112 Iwo amati, "Ngati dzina lako liri mu bukhu la Moyo, izo ziri bwino, uh?" Ayi, bwana!

113 Taonani, Yudasi Iskarioti anali nalo dzina lake mu bukhu la Moyo. Tsopano mukuti uko ndi kulakwitsa? Yesu, mu Mateyu 10, anawapatsa iwo mphamvu yokatulutsa ziwanda, ndipo anawatuma iwo kuti akachiritse odwala, ndi kukawayeretsa akhate, ndi kukawukitsa akufa. Ndipo iwo anapita kumeneko, ndipo anabwererako, Yudasi ali limodzi nawo. Ndipo iwo anakatulutsa ziwanda, ndipo anakachita mitundu yonse ya zozizwitsa. Ndipo anabwererako, ndipo anati, "Ngakhale ziwanda zimatimvera ife."

114 Yesu anati, "Musasangalale kuti ziwanda zimakumverani inu, koma musangalale chifukwa maina anu analembedwa Kumwamba." Ndipo Yudasi anali nawo iwo. Koma chinachitika ndi chiyani? Pamene zinafika kwa gulu Losankhidwalo, kuti apite kumeneko pa Pentekoste ndi kukalandira kwenikweni Mzimu Woyera, Yudasi anawonetsera mawanga ake. Iye adzakakhala kumeneko mu Chiweruzo.

115 Kotero mabuku anatsegulidwa; ndipo bukhu, la Moyo, linatsegulidwa; ndipo munthu aliyense anaweruzidwa chomwecho. Tsopano, Mkwatibwi akuyima apo limodzi ndi Khristu, kuti aliweruze dziko lapansi. Kodi a . . . Paulo akuti, "Musayesere inu," akuyankhula kwa Mkwatibwi, "mukakhala

nawo mtundu uliwonse wa dandaulo kwa wina ndi mzake, kuti inu mumapita ku mabwalo osalungama. Kodi inu simukudziwa kuti oyera adzaweruza dziko lapansi?" Mukuona? Ndi zimenezotu pamenepo. Oyera adzaweruza dziko lapansi ndipo adzalitenga ilo. Uko nkulondola.

116 Mukuti, "Zidzakhala motani mdziko ndi kagulu kakang'ono monga kameneko?" Ine sindikudziwa momwe izo zidzachitikire. Koma Iye anati izo zidzachitika, kotero izo zikungokhazikitsa zimenezo, monga momwe ine ndikudziwira.

117 Tsopano taonani. Tsopano zindikirani. "Ena onse akufa," mamembala a mpingo, mamembala akufa a mpingo, "sanakhalenso ndi moyo kufikira zaka sauzande zitatha." Ndiyeno pa kutha kwa zaka sauzande, iwo anasonkhanitsidwa; chiukitsiro china chinabwera, chomwe chiri chiukitsiro chachiwiri, ndipo iwo anasonkhanitsidwa. Ndipo Khristu ndi Mpingo, Mkwatibwi, osati mpingo; Mkwatibwi, Khristu ndi Mfumukazi, osati mpingo. Mping-. . . Khristu ndi Mkwatibwi anayima pamenepo.

118 Ndipo iwo analekanitsidwa, monga nkhosa kwa mbuzi. Uko nkulondola. Pamenepo ndi pamene mamembala a mpingo akudzabwera. Ndipo ngati iwo anamva Choonadi ndikuchikana Choonadicho, ndiye ndi chiti chidzayankhulidwe pamene chinthu chachikulucho chidzawonetseredwe poyera, pamene ngakhale malingaliro anu omwe adzakhala ali pamenepo, zomwe inu munkalingalira za Icho? Inu mudzazithawa bwanji izo, ndipo izo ziri pomwepo pa chinsalu cha mumlengalenga, ndipo televizioni yaikulu ya Mulungu ili pamenepo. Ndi malingaliro anu omwe akukuwukirani. Malingaliro anu omwe adzayankhula mokutsutsani inu mu ora limenelo.

119 Kotero ngati mumayankhula chinthu chimodzi, ndi kuganiza china, kulibwino inu musiye zimenezo. Muziyika malingaliro anu pa Mulungu. Muziwasunga iwo mwangwiro, ndipo muzikhala pomwepo ndi iwo, ndipo muziyankhula chinthu chomwecho nthawi zonse. Mukuona? Osati muziti, "Chabwino, ine ndinena kuti ndikukhulupirira Izo, koma ine ndipita ndikafufuze." Inu mukhulupirire Izo! Ameni.

120 Zindikirani, zoimira izi, chifukwa chimene iwo akufa, iwo akudutsa mu kuyeretsa kwa yesero la Chisautso chifukwa iwo siali kwenikweni pansi pa Magazi. Iwo amadzinenera kuti ali, koma iwo siali. Iwo angadutse bwanji mu yesero, kuti liwayeretse iwo, pamene apo pali (bulitchi) Magazi a Yesu Khristu amene amachotsa chisonyezo chirichonse cha tchimo ndi zinthu kuzichotsa kwa inu? "Ndipo ndinu akufa kale, ndipo moyo wanu wabisidwa mwa Iye, kupyolera mwa Mulungu, ndipo mwasindikizidwira mmenemo ndi Mzimu Woyera." Inu mukaweruzidwa chifukwa chiyani? Inu mukachitenga kuti chiyeretso chanu? Inu musowa kuyeretsedwa kuchokera ku

chiyani, pamene ndinu wangwiro mwa Khristu, wopanda tchimo? Motani. . . Chiweruzocho ndi cha chiyani? Koma ndi gulu logonalo, limene anthu amenewo sangakhoze kukwanitsa.

121 Tsopano, iwo sanachite izo kwa zaka, mukuona, koma ili ndi ora la vumbulutso, mwaona, mwaona, zikuwululidwa chabe pa kudza kwa Mkwatibwi; kutsirizitsa komaliza, zinthu zotsiriza zikubwera. Izo zikufika kumathero, mzanga, ine ndikukhulupirira. Liti? Ine sindikudziwa. Ine—ine sindingakhoze kukuuzani inu. Koma chirichonse. . . Ine ndikufuna kumakhala moyo usikuuno ngati kuti unali usikuuno, ine ndikhale wokonzeka. Mukuona? Iye akhoza kubwera usikuuno, apobe, ndipo Iye mwinamwake akhoza kusabwera kwa zaka twente. Ine sindikudziwa nthawi imene Iye ati adzabwere. Koma kaya ndi liti,. . . Ndipo moyo wanga ukhoza kutha, usikuuno; ndipo, ndiye, chirichonse chimene ine ndachita kuno chidzatsirizika pa ora limenelo. Ine—ine ndiyenera kudzakomana naye Iye mu chiweruzo, momwe ine ndayendera pansi pano. "Komwe mtengo wapendekera, ndi kumene iwo umakagwera."

122 Kumbukirani, pamene iwo anapita kukagula Mafuta, iwo. . . "Oh," inu mukuti, "tsopano dikirani miniti, M'bale Branham. Ine sindikudziwa za zimenezo." Pamene iwo anapita kukagula Mafuta, pamene iwo anabwerera, Mkwatibwi anali atapita kale ndipo chitseko chinali chitatsekedwa. Ndipo iwo anagogoda, ndipo anati, "Tiloreni ife tilowe! Tiloreni ife tilowe!" [M'bale Branham anagogoda pa guwa kangapo—Mkonzi]. Koma iwo anali kunja ku mdima wakunja.

123 Tsopano, ngati inu mukufuna choyimira cha zimenezo, tsopano onani. "Mu nthawi ya Nowa," Yesu anati, anafanizira kwa iyo. Tsopano, mu nthawi ya Nowa, iwo analowa mu chombo. Koma iwo anatengedwa kudutsa umo. . . mu nthawi ya chiweruzo, koma icho—icho sichinaimire Mkwatibwi wa Khristu.

124 Enoki anaimira Mkwatibwi. Enoki! Nowa anatengedwera umo, kudutsa mwa Mkwatibwi. . . anatengedwera, kudutsa mu nthawi ya chisautso, ndipo anazunzika, ndipo anadzakhala chidakhwa, ndipo anafa. Koma Enoki anayenda pamaso pa Mulungu, kwa zaka faivi handiredi, ndipo anali nawo umboni, "iye anamukondweretsa Mulungu," ndi chikhulupiriro chokwatulitsa; ndipo anangoyamba kuyenda kumeneko, ndipo anakwera mmwamba kudutsa mu mlengalenga, ndipo anapita Kwawo wopanda ngakhale kulawa imfa; sanafe konse, nkomwe.

125 Ndiwo mtundu wa, "Ife amene tiri ndi moyo ndipo tatsalira, sitidzawalepheretsa, kapena kuwatsekereza, anthu a mtundu womwewo awo amene akugona," amene anagona tulo chifukwa cha usinkhu wa umunthu, mu—mu chikhalidwe cha usinku wa munthu. Iwo anafa kumbuyo uko, koma iwo sikuti anafa.

Iwo akugona. Ameni. Iwo ali mtulo, sikuti akufa. Ndipo chinthu chokhacho chimene chikusowekera ndi kuti Mkwati awadzutse iwo. Inde. "Ndipo ife amene tiri moyo ndipo tatsalira, sitidzawatsekereza iwo amene anagona kale tulo. Pakuti lipenga la Mulungu lidzawomba, ndipo akufa mwa Khristu adzawuka poyamba; ndiye ife amene tiri moyo ndipo tatsalira tidzakwatulidwa limodzi ndi iwo, ndipo tidzakakomana naye Ambuye mu mlengalenga."

126 "Ndipo ena onse akufa sanakhale ndi moyo kwa zaka sauzande." Ndi zimenezotu, iwo anadutsa mu nthawi ya Chisautso.

127 Chinali chiyani chimenecho? Monga Enoki. Inu mukudziwa, Nowa ankamuyang'ana Enoki. Pakuti, pamene Enoki anafika posowa, iye anadziwa kuti chiweruzo chinali pafupi. Iye anayamba kumakhala pafupi ndi chombo.

128 Koma Nowa sanakwere mmwamba. Iye anangokwezedwa mmwamba pang'ono, ndipo anakwera kudutsa pamwamba pa zisautso. Iye ananyamulidwa kudutsa mu nthawi ya chisautso, kuti afe imfa. Mukuona? Koma Nowa anatengedwera kudutsa mmenemo.

129 Enoki anasamutsidwa, popanda kufa, choyimira cha Mpingo ukukwatulidwa nawo iwo amene akugona, kukakomana naye Ambuye mu mlengalenga, ndipo mpingo wonse wotsalawo ukutengedwera mu nthawi ya Chisautso. Sindingapange chinthu chinanso kuchokera kwa izo, inemwini. Enoki, kukwatulidwa, popanda imfa.

130 Tsopano tiyeni tiyambe kuwerenga pang'ono tsopano, tifike ku phunziro lathu. Ine ndikamangopitirira pa zimenezo, ife sitilowa konse mu izi, Chisindikizo ichi. Tsopano zindikirani. Tiyeni titenge tsopano, chifukwa tidzakhala nazo, momwemu, mwinamwake mawa usiku kapena usiku wotsatirawo, tidzagunda Lipenga, nthawi ndi nthawi, chifukwa Lipenga likuwomba nthawi yomweyo ya Zisindikizo. Icho ndi chinthu chomwecho basi. M'badwo wa mpingo ukutseguka, a . . . chinthu chomwecho basi. Mukuona?

131 Tsopano, lipenga nthawizonse limafotokoza za nkhondo kapena, mwanjira ina, kusokoneza kwa ndale, lipenga limatero, kusokoneza kwa ndale, ndipo izo zimayambitsa nkhondo. Pamene inu mufika posokonezeka mu ndale, ndi kuzisokoneza izo zonse, monga ife tazifikitsira izo tsopano, mudzapenyetsetse, nkhondo ili pafupi. Koma, mukuona, ufumu ukadali wa Satana. Iye akadali nalo gawo ili mdzanja lake.

132 Chifukwa chiyani? Ilo linawomboledwa ndi Khristu, koma Iye akuchita gawo la Muwomboli Wachibale, akutenga omumvera Ake, mpaka lotsirizalo (dzina) litalembedwa pa Bukhu limenelo, walilandira kale Ilo ndipo wasindikizidwira

kutali. Tsopano kodi mwamvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

133 Kenako Iye akubwera kuchokera ku Mpandowachifumu Wake, Mpandowachifumu wa Atate Ake, akupita patsogolo, akudzatenga Bukhulo kuchokera mdzanja la Mulungu, kuchokera ku Mpandowachifumu, ndipo akudzatenga ufulu Wake. Chinthu choyamba chimene Iye akuchita ndi kuyitana Mkwatibwi Wake. Ameni! Kenako Iye akutenga chiyani? Iye akumutenga mdani Wake, Satana, ndipo akumumanga iye, ndipo akumuponyera iye mmoto kunja uko, limodzi ndi onse omwe ankamutsatira iye.

134 Tsopano, kumbukirani, uyo sanali Russia. Ayi. Wotsutsakhristu ndi munthu wothyathyalika. Tangoyang'anani momwe iye aliri wothyathyalika. Iye ndi wanzeru, tsopano. Inde, bwana. Zimangotengera Mzimu Woyera; chinthu chokhacho chimene chingamugonjetse iye.

135 Zindikirani, Malipenga amatanthauza kusokoneza kwa ndale, nkhondo. Mateyu 24, Yesu anayankhula za izo. Iye anati, "Inu mudzamva za nkhondo ndi mphekesera za nkhondo, mwaona, njira yonse mpaka mmusi." Inu mukukumbukira . . . Yesu akuyankhula zimenezo, "Nkhondo, mphekesera ndi nkhondo, ndi mphekesera ndi nkhondo, ndipo mpaka mmusi mpaka ku mapeto." Tsopano, amenewo ndi Malipenga akuwomba.

136 Tsopano, pamene tidzafike pa Malipenga, ife tidzabwerera mmbuyo uko ndi kukatenga iliyonse ya nkhondo zimenezo, ndi kudzakuwonetsani inu kuti izo zinkatsatira mipingo imeneyo, kukuwonetsani inu kuti izo zikutsatira Zisindikizo izi. "Nkhondo ndi mphekesera za nkhondo." Koma, Lipenga, limatanthauza kusokonekera kwa ndale.

137 Pamene, Zisindikizo zimachita ndi kusokonekera kwa zipembedzo. Mukuona? Chisindikizo chikatsegulidwa, Uthenga umaperekedwa. Ndiyeno mpingo nthawizonse umakhala utakhazikika kwambiri mu njira zake za ndale, ndi china chirichonsecho, ndi nthumwi zake zonse zolemekezeka. Ndiye pamene Uthenga weniweniwo ugwera pansi, mtumikiyo amapita kumeneko ndipo amakawagwedeza iwo mzidutswa. Uko nkulondola. Pamakhala chisokonezo cha zipembedzo pamene Chisindikizo chatsegulidwa. Izo ndi zomwe zinkachitika. Eya. Inde.

138 Iwo onse amakhala molekerera mu Zioni. Mpingo wonse umafika pokhazikika, ndipo, "Ife tazipanga zonsezo." Chimodzimodzi monga mpingo wa ku England, iwo onse anafika pokhazikika. Mpingo wa Katolika, onse anakhazikika, ndipo kenako panadzabwera Luther. Apo panali kusokonezeka kwa zipembedzo. Inde, bwana! Ndithudi zinatero! Chabwino, mpingo unapitirira kutayika, ndi Zwingli. Ndipo kuchokera kwa

Zwingli, panadzabwera mmusimo osiyanasiyana, ndipo mpaka kwa Calvin. Ndipo patapita kanthawi, mpingo wa Anglican unadzakhazikika, ndipo iwo unangokhala molekerera, ndipo popitirira panadzabwera Wesley. Apo panali kusokonezeka kwa zipembedzo. Uko nkulondola. Mwaona, izo nthawizonse zimasonyeza kusokonezeka kwa zipembedzo.

139 Tsopano, Chisindikizo. Tiyeni tingowerenga Icho pang'ono pokha tsopano. Ine ndikufuna kuti—kuti nditenge izi, ife tingowerenga Icho. Ine ndikayamba kuyankhula. Ine . . .

> *Ndipo ine ndinawona pamene Mwanawankhosayo anatsegula chimodzi cha zisindikizo,* (chinachitika ndi chiyani?) *ndipo ine ndinamva, ngati kuti linali phokoso la bingu, . . .*

140 Oh, momwe ine ndikanafunira kukhazikika pa icho maminiti ochepa okha! Ndipo ine ndikuyembekeza tsopano kuti anthu onse amene akuzidziwa zinthu izi ndipo akuyembekezera chitonthozo cha Ambuye, tsopano aphunzira mwatcheru kwenikweni; ndi pa matepi, naponso, kuti inu muganizira za izi.

141 Chinthu choyamba chimene chinachitika, pamene Mwanawankhosa uja anamatula Chisindikizo Choyamba chija, Bingu linabangula. Tsopano, icho chinali ndi kufunikira. Chiri ndi . . . Ndi chofunikira. Chiri ndi tanthauzo. Icho ndi tanthauzo. Palibe chimene chimachitika popanda tanthauzo. Chabwino, Bingu, Bingu linabangula. Mukudabwa chomwe Bingu ilo linali?

142 Tsopano tiyeni tiwerenge pang'ono pokha. Tiyeni titsegule ku Mateyu . . . Ayi, tiyeni titenge Yohane Woyera, poyamba. Yohane Woyera, mutu wa 12, ndipo mungogwira kwa miniti. Yohane Woyera, mutu wa 12. Ndipo tsopano tiyeni tiyambire pa ndime ya 23 ya Yohane Woyera 12. Tsopano mvetserani apa, tsopano, mwatcheru kwenikweni, ndiye inu simusowa kudabwanso chimene icho chiri.

> *Ndipo Yesu* powayankha *iwo, anati, Ora lafika, kuti Mwana wa munthu alemekezedwe.*

143 Mwaona, inu muli pa mathero a m'badwo, pamenepo. Utumiki wake ukutha. Mukuona? "Ora lafika, lakuti Mwana wa munthu alemekezedwe."

144 Nanga bwanji, "Ora lafika lakuti Mkwatibwi Wake atengedwepo"? Chiyani? Ora lafika, lakuti, "Nthawi siyidzakhalaponso." Mngeloyo wakonzeka kuti ayike phazi limodzi pa mtunda, ndi linalo pa nyanja, ali ndi utawaleza pamutu Pake, mapazi Ake, ndi kunena kuti, "Nthawi yatha." Ndipo pambali pa zimenezo, Iye anakweza mmwamba dzanja Lake ndipo analumbira kuti "nthawi siyidzakhalaponso," pamene ichi chidzachitike. Motani—ndi zangwiro motani, chikalata cha lumbiriro kwa Mpingo!

. . . Ora lafika, lakuti Mwana wa munthu alemekezedwe.

Indetu, indetu, Ine ndinena kwa inu, Pokhapokha njere ya tirigu itagwera *mu nthaka ndi* kufa, *iyo* imakhala *yokha: koma ngati iyo ifa, iyo imabala zipatso zambiri.*

Iye amene akonda moyo wake adzawutaya iwo; . . . iye amene adana nawo moyo wake mdziko lino adzawusungira iwo kwa moyo wamuyaya.

Ngati munthu wina aliyense anditumikira ine, muloleni iye anditsate ine; ndipo kumene ine ndiri, kumeneko . . . wantchito wanganso adzakakhalako: ngati munthu aliyense anditumikira ine, iyeyo Atate anga adzamchitira ulemu.

Tsopano moyo wanga wasautsika; . . .

145 Inu mukuti, "Chabwino, Iye, kufika kumathero a ulendo, ndipo nkukhala ndi vuto?" Kodi chimakupangitsani inu kuganiza ndi chiyani pamene chinthu china chopambana chauzimu chichitika, chimene chimakusautsani inu? Oh, mai! Uh-huh!

Tsopano mu *moyo mwanga ndasautsika; ndipo kodi ine ndidzanena chiyani? Atate, ndipulumutseni ine ku ora ili: koma kwa cholinga ichi ine ndinadza ku* dziko *ili, kwa ora ili.*

Atate, lemekezani dzina lanu. Ndiye panadza apo liwu lochokera kumwamba, likuti, ine ndalilemekeza ilo, ndipo ndililemekeza ilo kachiwiri.

Anthuwo anati, *amene anayima pafupi,* amene *analimva ilo,* iwo anati . . . *kunamveka bingu:* . . .

146 Ndiye, pamene Mwanawankhosa anatenga Bukhulo ndi kumatula Chisindikizo Choyambacho, Mulungu anayankhula kuchokera ku Mpandowachifumu Wake Wamuyaya, kuti anene chomwe Chisindikizo icho chinali, kuti chiwululidwe. Koma pamene Icho chinayikidwa pamaso pa Yohane, Icho chinali mophiphiritsa. Pamene Yohane anachiwona Icho, Icho chinali chikadali chinsinsi. Chifukwa chiyani? Icho chinali chisanaululidwe nkomwe panthawiyo. Icho sichingaululidwe kufikira chimene Iye ananena apa, "pa nthawi yotsiriza." Koma icho chinabwera mophiphiritsa.

147 Pamene, "kunamveka bingu." Kumbukirani, phokoso logunda lalikulu la Bingu ndi Liwu la Mulungu. Ndicho chimene Baibulo limanena, mwaona, "kugunda kwa Bingu." Iwo ankaganiza kuti ilo linali bingu, koma Ilo linali Mulungu. Iye analimvetsa Ilo, pakuti Ilo linawululidwa kwa Iye. Mukuona? Ilo linali Bingu.

148 Ndipo, zindikirani, Chisindikizo Choyamba chinatsegulidwa. Chisindikizo Choyamba, pamene Icho chinatsegulidwa mmawonekedwe ophiphiritsa, kunamveka bingu. Tsopano kuli bwanji pamene Icho chizitsegulidwa mmawonekedwe Ake enieni? Mai . . . Kunamveka bingu mwamsanga pamene Mwanawankhosayo anakanthira mmbuyo Chisindikizocho. Ndipo kodi Icho chinaulula chiyani? Osati zonse za Icho. Poyamba, Icho chiri ndi Mulungu; chotsatira, Icho chiri mophiphiritsa; kenako, Icho chikuululidwa. Zinthu zitatu. Mukuona? Icho chikubwera kuchokera ku Mpandowachifumu.

149 Poyamba, Icho sichingawoneke, kumvedwa, kapena chirichonse. Icho ndi chosindikizidwa. Magazi a Mwanawankhosa analipira mtengo wake.

150 Panamveka bingu pamene Iye anachiyankhula Icho. Ndipo pamene Iye anatero, wokwera pakavalo-woyera anayamba kutulukira, ndipo Icho chinali chikadali chophiphiritsa. Tsopano penyani, Iye anati Icho chidzadziwika mu tsiku lotsiriza. Koma Icho chikubwera mwa chophiphiritsa cha mpingo. Kodi inu mukumvetsa zimenezo, mpingo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Icho chikubwera mwa—mwa chophiphiritsa cha mpingo, kuti iwo adziwe kuti pali Chisindikizo. Koma basi chomwe Icho chiri, komabe, iwo sakudziwa, chifukwa Icho chiri wokwera pakavalo-woyera.

151 Ndipo icho chiri choti chidzaululidwe kokha pa tsiku lotsiriza, pamene Chisindikizo chenicheni ichi chikumatulidwa. Kumatulidwira kwa ndani? Osati kwa Khristu, koma kwa Mpingo. Zindikirani, tsopano. Oh, mai, izo zikungondipangitsa ine kunjenjemera! Ine—ine—ine ndikuyembekeza kuti Mpingo ukuchimvetsa Icho moona, chimene ine ndikutanthauza, anthu inu. Ine ndikutchani inu Mkwatibwi, mwaona, kuti Inu muchimvetse Icho.

152 Liwulo ndi Bingu. Liwulo linabwera kuchokera kuti? Kuchokera ku Mpandowachifumu kumene Mwanawankhosa anali atangochokako kumene, monga Wopembedzera. Tsopano Iye akuyima apa kuti atenge malo Ake ndi zomwe ziri Zake. Koma Bingulo linabwera kuchokera mkati mwa Mpandowachifumu, linagunda momveka. Ndipo Mwanawankhosayo anali atayima panja apa. Bingu, kumene Mwanawankhosa anali atachokako. Anachoka ku Mpandowachifumu wa Atate, kuti apite kukatenga Mpandowachifumu Wake Womwe. Ulemelero! Tsopano, tsopano musaphonye izi, amzanga.

153 Ife tonse tikudziwa, ngati Akhristu, kuti Mulungu analumbira kwa Davide kuti Iye akanadzadzutsa Khristu kuti adzakhale pa Mpandowachifumu wake, ndi kumupatsa Iye ufumu wosatha pano pa dziko lapansi. Iye anachita zimenezo.

154 Ndipo Yesu anati, “Iye amene agonjetsa wotsutsakhristu ndi zinthu zonse za mdziko, adzakhala ndi Ine pa Mpandowachifumu Wanga, monga Inenso ndagonjetsa ndipo ndakhala pansi pa Mpandowachifumu wa Atate Anga.” Mukuona?

155 Tsopano, tsiku lina Iye adzadzuka kuchokera ku Mpandowachifumu wa Atate, ndipo adzapita kukatenga Mpandowachifumu Wake Womwe.

156 Tsopano Iye akubwera kudzayitana omumvera Ake. Iye adzawatenga chotani iwo? Iye ali nalo kale Bukhu la Chiwombolo mdzanja Lake. Ulemelero! Oh, ine ndikumverera ngati ndiyimbe nyimbo.

Posachedwa Mwanawankhosa adzatenga
Mkwatibwi Wake kukakhala nthawizonse
pa mbali Pake,
Khamu lonse la Kumwamba lidzasonkhana
(kudzawonera izo);
Oh, iwo adzakhala mawonekedwe aulemelero,
oyera onse atavala zoyera zopanda banga;
Ndipo ndi Yesu ife tidzachita phwando
Kwamuyaya.

157 Oh, mai! Kukamba za “kukhala tsopano mmalo Ammwambamwamba”? Zidzakhala zotani izo! Ngati ife tikukhoza kumverera mwa njira iyi, titakhala pano pa dziko lapansi, Mkwatulo usanafike, mu chikhalidwe ichi chimene ife tirimo tsopano; ndipo tikukhoza kusangalala, ndi kuimirira mozungulira makoma, ndi kuyima mu mvula, kuti tingomvetsera Izi; zidzakhala motani pamene ife tidzamuwona Iye atakhala pamenepo! Oh, mai! Oh, idzakhala nthawi yaulemelero.

158 Anasiya Mpandowachifumu wa Atate, anadza ku. . . Mwana Wake, kuti adzakhale. . . Iye ndi Mwana wa Davide. Icho ndi chimene Israeli ankaganiza kuti Iye akudzachita nthawi imeneyo. Kumbukirani mkazi wa Chisurofonika, anati, “Inu Mwana wa Davide!” Kumbukirani Bartimeyo wakhungu, “Inu Mwana wa Davide!” Uh-huh! Ndipo Yesu, podziwa chomwe dongosololo linali, komabe iwo sankadziwa ichi. Iwo anayesetsa kumukakamiza Iye ndi kumupangitsa Iye kutenga mpandowachifumuwo. Ndipo ngakhale Pilato anamfunsa Iye.

159 Koma Iye anati, “Ngati ufumu Wanga ukanakhala wa dziko lino, ndiye ondimvera Anga akanamenyera. Ufumu wanga uli Kumwamba.” Koma Iye anati, “Pamene inu mupemphera, pempherani, ‘Ufumu Wanu udze. Chifuniro Chanu chichitike mdziko lapansi lino, monga ziriri Kumwamba.’” Ameni. Uh-huh! Ndi chaulemelero bwanji chinthu chopambana ichi!

160 Anasiya Mpandowachifumu wa Atate, kuti akatenge Mpandowachifumu Wake Womwe. Iye tsopano wabwera kuchokera ku ntchito Yake yopembedzera, kudzatenga

Mpandowachifumu Wake Womwe, omumvera Ake owomboledwa. Icho ndi chimene Iye anadzera kuchokera ku Mpandowachifumu kuti adzachite. Apo ndi pamene Chamoyo chonga mkango chinati kwa Yohane, "Bwera, udzawone." Penyani. Kodi inu mukuwerenga zimenezo?

> . . .*chimodzi cha zisindikizo, ndipo* icho. . .*monga* ngati *liwu la bingu,* ndipo *chimodzi cha zamoyo zinayi*. . .

161 Inu mukudziwa chimene Zamoyozo zinali. Ife tinazitenga izo. "Chimodzi chonga mkango; china chonga ng'ombe; ndi china chonga munthu; ndi china chonga mphungu." Tsopano, Chamoyo choyamba ichi chinati. . .Penyani, nthawi iliyonse pakumakhala Chamoyo chosiyana, mpaka okwera pakavalo anayi amenewo atadutsa. Pali Zamoyo zinayi, ndipo pali okwera pakavalo anayi.

162 Zindikirani, chirichonse cha Zamoyo izo chikulengeza. Mateyu, Marko—Marko, Luka, ndi Yohane. Ife tibwereramo umo ndi kudzatsimikizira kuti ndi chiti chiri, Mateyu, Marko, ndi chiti chiri Marko—Marko, ndi chiti chinali Yohane, chirichonse pamene izo zinkapita!. . .?. . .

> . . .*chimodzi cha. . .zamoyo chinati, Bwera. . . udzawone.*

163 Iye anamva phokoso la bingu. Ndipo chimodzi cha Zamoyo chinati, "Tsopano bwera, udzawone."

164 Mwa kuyankhula kwina, tsopano, *apa* payima Mwanawankhosa, ndipo Yohane ataimirira kunja uko akuyang'ana izo zikuchitika. Mwanawankhosa anabwera kuchokera pa Mpandowachifumu, ngati kuti Iye anali ataphedwa, Magazi ali paliponse pa Iye. Iye anali Mmodziyo yemwe anapezeka woyenera. Ndipo pamene Iye anafikirako natenga Bukhulo, ndiye chirichonse chinayamba kufuula, ndi kukuwa, ndi kumapitirira, inu mukuona, chifukwa iwo amadziwa kuti chiwombolo chinali chitalipiridwa.

165 Tsopano Iye wabwera kudzatenga Ake Omwe. Kotero, Iye akulitenga Bukhulo, akuyima pamenepo pamaso pa Yohane, ndipo Iye akuchisolola Icho ndipo akumatula Chisindikizocho. Akusolola Chisindikizocho! Ndipo pamene Iye akusolola Chisindikizocho, Bingu linagunda kudzadutsa pa malopo. Ndipo pamene Bingu linagunda, mosakaika Yohane ayenera kuti analumpha mmwamba mmalere, pamene Bingulo linabangula.

166 Ndiyeno chimodzi cha Zamoyo zinayizo chinati, "Tsopano bwera, udzawone chimene Icho chiri, chimene chawululidwa pansi apa." Oh, mai! "Yohane, lemba zomwe iwe waziwona." Kotero Yohane akupita kukawona, kukawona chimene Icho chinali. Yohane akupita kukawona chimene Bingulo linanena. Ndi pamene Chamoyo ichi chinamuuza Yohane, "Bwera, udzawone chimene chinsinsicho chiri pansi pa Chisindikizo

Choyamba." Bingu, Liwu la Mlengi lanena Icho. Tsopano, Iye amayenera kudziwa chimene chinali Mmenemo. Mukuona? Oh, mai! Koma, taganizani tsopano, iye analemba Ichi.

167 Koma pamene iye anayamba kulemba zina zimenezo, Mabingu Asanu Ndi Awiri, Iye anati, "Usalembe Zimenezo." Iye anali atatumidwa kuti alembe chirichonse chimene iye anachiwona. Koma pamene Mabingu Asanu Ndi Awiri awa, uko mu Chivumbulutso 10, anayankhula, Iye anati, "Usalembe Izo, nkomwe." Izo ndi zinsinsi. Ife sitikudziwa chomwe izo ziri mpaka pano. Koma, lingaliro langa, izo ziwululidwa pomwe pano. Ndipo pamene izo zidzatero, zidzapereka chikhulupiriro kwa chisomo chokwatulitsa icho, kuti Mpingo uwo uchokepo. Mukuona?

168 Ife tangodutsamo kumene mu chirichonse chimene ife timachidziwa, kudutsa mu nyengo zonse. Ife tachipenya chirichonse. Ife taziwona zinsinsi za Mulungu. Ife tawona kuwonekera kwa—kwa kusonkhana limodzi kwakukulu kwa Mkwatibwi mmasiku otsiriza. Koma, apobe, pali chinachake mkati Umo chimene ife sitingadziwalitse nacho tokha. Muli chinachake chimzake.

169 Koma ine ndikulingalira, pamene zinsinsi zimenezo zinayamba kubwerapo, Mulungu anati, "Zisiye kaye Izo tsopano. Dikira kwa miniti. Ine ndidzaziwulula Izo mu tsiku ilo. Usazilembe Izo, nkomwe, Yohane, chifukwa iwo adzadzandima pa Izo. Basi—ungozilola izo zizipita, mwaona. Koma Ine ndidzaziwulula Izo mu tsiku limenelo pamene zidzafunikire kuti zitero."

170 Iwo sanangoyankhula kwa chabe. Kumbukirani, monga dontho laling'ono la inki, chirichonse chimakhala nacho cholinga. Chirichonse chimakhala ndi cholinga. Koma, zindikirani, Mlengiyo anayankhula. Ndipo iye—iye analimva Liwu ili, ndipo iye anapita kuti akawone.

171 Koma tsopano Mwanawankhosa akumusonyeza Yohane, mu chiphiphiritso cha . . . cha—cha lemba la mpingo, monga, kuti mpingo udziwe. Choti alembe, Iye anangomusonyeza iye. Anati, "Tsopano, usati—usanene ichi, basi chomwe icho chiri. Usapite kumeneko, Yohane, ndi kukati, 'Tsopano, ichi chiri basi chimene ichi chiri, cha zomwe ziri pansi pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi.' Usatero, usapite uko ndi kumakanena zimenezo. Pakuti, ngati Ine ndingamuuze Yohane zimenezo, ndiye zonse kudutsa mu m'badwo, dongosolo lonse lisweka. Icho ndi chinsinsi." Mukuona? Iye akungofuna . . . Kudza Kwake! Iye anati, tsopano, "Ndipo palibe amene ati adzadziwe nthawi imene Ine ndikubwera. Ine ndikungobwera basi." Mukuona? Mukuona? Ndizo zonse. Si ntchito yanga kudziwa kuti ndi liti. Ine ndingokhala wokonzeka, inu mukuona. Kotero ndiye iye anati . . .

Tsopano Yohane anapita pamenepo, iye anaganiza, “Ine ndikawona Icho tsopano.”

172 Ndipo kodi iye anachita chiyani, pamene Yohane anapita pamenepo? Iye, tsopano, kodi iye akukachita chiyani? Tsopano iye ayenera kulembera izi kwa m’badwo wa mpingo. Ndicho chimene iye akuyenera kuchita, kulembera izo kwa mibadwo ya mpingo. “Lemba zimene iwe ukuziwona pa Zoyikapo nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide, poyambirira. Ulembere kwa mpingo uwu ndipo uwauze iwo.” Chabwino.

173 Ndipo Bingu linabangula. Yohane anadziwa kuti ilo linali Liwu la Mulungu. Ndiyeno cha—Chamoyo chonga mkango chinati, “Bwera, udzawone chimene icho chinali.” Ndipo Yohane anapita tsopano, ali nacho cholembera chake, kuti akalembe zomwe iye akanati akawone.

174 Tsopano, iye sanawone ndendende chomwe icho chinali. Iye sanachimvetse icho. Koma zomwe iye anaziwona zinali zomwe Mulungu anali kutumiza ku mpingo kwa “kanthawi.” Tsopano Iye ali nazo . . . Iye adzatero; Iye nthawizonse amatero; Iye amazipanga izo kumveka bwino pamene nthawi yake yakwana yozipanga izo kumveka bwino. Koma Iye sanazipange izo kumveka bwino pa nthawiyo. Chifukwa chiyani? Chifukwa, Iye anali woti azisunge izo mwachinsinsi kufikira m’badwo wotsiriza. Ndipo kuwomba kwa Uthenga wa mngelo wotsiriza kunali kwakuti kudzasonkhanitse zinsinsi izi. Mukuona?

175 Sanazipangitse izo kumveka. Koma chimene Yohane anawona, iye anangowona, “Kavalo woyera akutulukira, ali naye womkwera pa iye,” kotero ndicho chimene iye analemba, mwaona, pamene iye anatero.

Ndicho chimene iye anati, “Bwera, udzawone.”

176 Chotero Yohane anapita kukawona zomwe iye akanakhoza kuwona, kuti alembere kwa mpingo. Ndipo pamene iye anatero, iye anawona, “Kavalo woyera, ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo uta; ndipo iye anapita akugonjetsa, ndi kugonjetsa; ndipo kunapatsidwa kwa iye korona.” Ndipo, tsopano, ndizo zonse zomwe Yohane anawona, kotero iye anangolemba, anazilemba zonse zimenezo. Tsopano, mwaona, izo ziri mu chophiphiritsa. Umo ndi momwe mpingo wazilandirira Izo.

177 Koma, ndi lonjezo, ndipo pa tsiku lotsiriza kuti Iye akanadzawulula Izo, kuwonetsera chomwe Icho chiri. Mulungu, atithandize ife kuti timvetse. Mibadwo ya Mpingo, koma izo sizinapangidwe kudziwika kwathunthu kufikira Uthenga wachisanu ndi chiwiri, wa m’badwo wa mpingo wotsiriza uwu. Zindikirani, iye akuyamba . . .

178 Mtumiki uyu wa m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, ngati inu mungazindikire zimenezo, iye sakuyambitsa chipembedzo, monga ena onse a iwo anachitira. Kumbukirani, ngati iye sakuyambitsa . . . Ayi. Ngati inu mungapeze, iye

akuchitsutsa icho. Kodi Eliya, kodi Eliya ankachitsutsa icho? Zedi, iye ankatero. Kodi Yohane ankachitsutsa icho, ali nawo Mzimu wa Eliya?

179 Unali mtundu wanji wa Mzimu umene Eliya anali nawo pa iye? Iye anali . . . Palibe amene akudziwa zambiri za iye. Iye anali munthu wamba, koma iye anali mneneri. Iye anali wodedwa. Mai! Ndipo kodi iye anadzuka mu nthawi yanji? Mu nthawi kumene ya kutchuka kwa Israeli, pamene iwo onse analowerera mwachidziko. Ndipo iye anawupeza iwo kumeneko, ndipo iye anali "wodana ndi akazi." Uh-huh. Inde, bwana. Zedi anali. Ndipo iye ankakonda chipululu. Ilo linali khalidwe lake.

180 Ndiye, anthu amenewo akanayenera kudziwa pamene munthu uyu anabwera kumeneko ali nawo Mzimu womwewo pa iye, atatulukira kumeneko, Yohane uyu. Osati atavala monga wotchuka, monga ine ndinanenera usiku wathawu; iwo amapsyopsyona makanda, ndi kukwatitsa, ndi kuyika maliro, ndi zina zotero. Koma munthu uyu anatulukira monga munthu wa mchipululu. Kodi iye anali chiyani? Iye ankakonda chipululu. Chinthu china chimene iye ankachita, iye ankadana nacho chipembedzo. Iye anati, "Tsopano, musayambe kunena, 'Ife tiri a *ichi* kapena *icho*,' pakuti ine ndikuwuzani inu, Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi, kudzutsa ana kwa Abrahamu."

181 Iye sanali wonyengerera. Iwo sakanakhoza . . . Anati, "Kodi inu munapita kuti mukawone bango logwedezeka ndi mphepo? Osati Yohane." Ayi, bwana.

182 Kodi iye anachita chiyani, nayenso? Basi monga Eliya amene anamuuza Yezebeli, iye anamuuza Herodiya. Anayenda mpaka pamaso pa Herode, ndipo anati, "Sikuli kololedwa kuti inu mumutenge iye." Iye anadula mutu wake, chifukwa cha icho. Mukuona? Iye anayesetsa kumutenga Elisha. Mzimu womwewo, umene unali mwa Yezebeli, unali mwa mkazi ameneyo.

183 Ndipo chinthu chomwecho chiri mu mpingo wa Chiyezebeli lero, chinthu chomwecho. Tsopano zindikirani ichi. Ndi phunziro lopambana bwanji limene ife tikulipeza apa!

184 Ndipo, tsopano, zikuwoneka ngati anthu amenewo akanakhoza kudziwa. Yohane anayamba kuwazazira anthu amenewo, ndipo anayima pamenepo, zinkawoneka ngati iwo akanakhoza kudziwa kuti umenewo unali Mzimu wa Elisha. Iwo ankayenera kumvetsa zimenezo. Ndicho chimene iye anali.

185 Tsopano, ndipo ife tikupeza kuti, ndipo tatero kudutsa m'mibadwo ya mpingo, molingana ndi Lemba, kuti ife talonjezedwa kubwereranso kwa Mzimu umenewo, isanafike basi nthawi yotsiriza. Izo nzoona?

186 Tsopano, ndipo zindikirani, inu mudzazindikira khalidwe la iwo. Tsopano, iye sadzayambitsa m'badwo wina wa mpingo, monga Luther, ndi Wesley, ndi momwe ena onsewo anachitira. Iye sadzayambitsa mpingo wina, chifukwa kulibenso mibadwo

ina ya mpingo yoti iyambidwe. Mukuona? Sikudzakhalanso ina. Kotero iye ayenera kukhala wotsutsa iyo, chifukwa Mzimu wake udzakhala chimodzimodzi basi monga iwo anali mmbuyomo, Mzimu womwewo.

187 Monga ine ndinanenera usiku watha, icho chinamukomera Mulungu kuti awugwiritse ntchito Iwo nthawi zitatu zosiyanasiyana. Ndiyo nambala Yake, katatu, osati kawiri; katatu. Wawugwiritsa ntchito kale Iwo kawiri, tsopano Iye awugwiritsanso ntchito Iwo kenanso. Iye ananena chomwecho, analonjeza izo. Tsopano zindikirani, iye . . .

188 Zindikirani tsopano, pamene Iye anatero. Iye sadzayambitsa chipembedzo, chifukwa M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya ndi m'badwo wotsiriza. Ndipo wamthenga, wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, yemwe wamthenga wachisanu ndi chiwiri, kwa m'badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, ndi munthu yemwe ati adzawulule, mwa Mzimu Woyera, zinthu zonse zachinsinsi izi. Zomwe ziti . . . Ndi angati anali muno usiku wathawu? Tiyeni tiwone dzanja lanu. Ine ndikuganiza ine sindikusowanso kuwerenga Izo mobwereza, ndiye. Inu mukudziwa pamene izo ziri, a—mutu wa 10, mwaona. Chabwino. Chabwino.

189 Okonzanso ankabwera kudzakonzanso m'badwo wa mpingo wakugwa wotsiriza wammbuyo mwawo. Ndiyeno, okonzansowo akati abwera nadzakonzanso a—m'badwo wa mpingo kuchokera pamene iwo unali, ndipo nkubwereranso mu dziko, ndiye iwo ankayamba m'badwo wa mpingo watsopano. Iwo nthawizonse ankachita zimenezo, nthawizonse. Tsopano, ife tinadutsa zimenezo. Mukuona?

190 Mwa kuyankhula kwina, *apa* panakhala pali m'badwo wa mpingo wa Chikatolika, wa mpingo wa Roma Katolika. Motsatira panadzabwera Luther, wokonzanso. Iye akutchedwa wokonzanso. Ndipo iye akudzachita chiyani? Iye akuyambira pomwepo, kukhomerera. Ndipo, pamene iye akutero, iye akuwuwukira mpingo. Ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iye akuchita chiyani? Iye akudzamanga chinthu chomwecho chimene iye anabwera kudzatulutsa mwa icho, mpingo wina.

191 Ndiye iwo ankakhala ndi m'badwo wina wa mpingo. Kenako, chinthu choyamba inu mukudziwa, apa panabwera . . . M'badwo wa mpingo unkakhala mu chisokonezeko chotero. Kenako panadzabwera John Wesley, wokonzanso wina. Mwaona, akudzamanga m'badwo wa mpingo wina. Mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza? M'badwo wa mpingo wina ukumangidwa. Iwo onse ndi okonzanso.

192 Zindikirani, Mtumiki wotsiriza uyu, wa m'badwo wa mpingo wotsiriza, si wokonzanso. Iye ndi mneneri, osati wokonzanso. Ndiwonetseni ine pamene mneneri mmodzi anayambitsapo m'badwo wa mpingo. Iye si wokonzanso. Iye ndi mneneri.

193 Enawo anali okonzanso, koma osati aneneri. Ngati iwo akanakhala anali, Mawu a Ambuye amadza kwa mneneri. Ndi chifukwa chake iwo ankapitirirabe mu ubatizo wa "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," zinthu zina zonse izi, chifukwa iwo anali okonzanso, ndipo osati aneneri. Ndipo komabe iwo anali amuna opambana a Mulungu, ndipo anawona chosowekera cha tsiku limene iwo ankakhalamo. Ndipo Mulungu anawadzoza iwo, ndipo iwo anatumidwa kunja uko ndipo anakang'amba zinthu zimenezo mzidutswa. Koma Mawu athunthu a Mulungu sanabwere kwa iwo, chifukwa iwo sanali aneneri. Iwo anali okonzanso.

194 Koma mmasiku otsiriza, iye adzayenera kukhala mneneri, kuti adzatenge zinsinsi za Mulungu, kuti adzazibweretsenso izo, chifukwa zinsinsi zinkadziwika kokha ndi aneneri. Kotero, ayenera kukhala munthu uyu amene akubwera. Mukuona chimene ine ndikutanthauza tsopano? Iye sangakhoze kukhala wokonzanso. Iye ayenera kukhala mneneri, chifukwa ayenera kukhala winawake amene ali nayo mphatso ndipo anayikidwa pamenepo, amene angagwire Mawu.

195 Tsopano, okonzanso amenewo ankadziwa kuti panali chinachake cholakwika. Luther ankadziwa zimenezo, kuti mkate umenewo sunali thupi la Khristu. Ndipo kotero iye analalikira, "Olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro," ndipo umenewo unali uthenga wake. Ndipo pamene John Wesley anadzabwera kenako, iye anawona kuti panali kuyeretsedwa, kotero iye analalikira kuyeretsedwa. Umenewo unali uthenga wake. Mukuona? Achipentekoste anabweretsamo uthenga wa Mzimu Woyera, ndi zina zotero.

196 Koma mmasiku otsiriza, mu m'badwo wotsiriza uno, mtumikiyu si woti adzayambitse kukonzanso kulikonse, koma ndi woti adzatenge zinsinsi zonse zimene okonzanso awo anazisiya, ndipo adzadzisonkhanitsa izo pamodzi ndi kudzazilongosola izo kwa anthu. Ndiroleni ine ndingowerenga Izo kachiwiri. Izo zikumveka bwino kwambiri kwa ine! Ine—ine ndimakonda kuwerenga Izo.

> *. . .Ine ndinawona mngelo wina wamphamvu akutsika kuchokera kumwamba, wovala mtambo:. . . utawaleza. . .pamutu pake, ndipo nkhope yake inali. . . dzuwa, ndi mapazi ake ngati mizati yamoto:*

197 Tsopano, ife tawona chinthu chomwecho, chimene chinali Khristu. Ndipo ife tikudziwa kuti Khristu nthawizonse amakhala Mtumiki kwa Mpingo. Chabwino. Iye amatchedwa Lawi la Moto, Mngelo wa Pangano, ndi zina zotero.

> *Ndipo iye anali nalo mdzanja lake bukhu laling'ono* lotsegulidwa:. . .

198 Tsopano, Zisindikizo zinali zitamatulidwa kale, apa. Ife tikuzimatula izo tsopano. Koma, ichi, Chinthucho chatsegulidwa.

> *. . .ndipo iye anapondetsa phazi lake lamanja* pa *nyanja, ndi lake lamanzere. . .pa mtunda,*
>
> *Ndipo* iye *anafuula. . .ndi mawu aakulu, monga pamene mkango ubangula: ndipo pamene iye. . . anafuula, mabingu asanu ndi awiri anayankhula maliwu awo.* (Mai! Kwathunthu!)
>
> *Ndipo pamene mabingu asanu ndi awiriwo anayankhula maliwu awo, ine* Yohane *ndinali pafupi kuti ndilembe* (kulemba chiyani?) zimene iwo ananena: *ndipo ine ndinamva liwu lochokera kumwamba* (Mulungu) *likunena kwa ine, Sindikiza zinthu izo zimene mabingu asanu ndi awiriwo ayankhula, ndipo usazilembe izo.* Usazilembe izo. (Mukuona?)
>
> *Ndipo mngelo amene ndinamuwona ataimirira panyanja. . .anakweza* manja *ake mmwamba,*
>
> *Ndipo analumbira pa iye amene* akukhala moyo *kwa nthawi za nthawi, amene analenga* miyamba, *ndi zinthu ziri* momwemo, *ndi dziko lapansi, ndi zinthu* zimene *ziri* momwemo, *ndi nyanja, ndi zinthu zomwe ziri momwemo, kuti pasakhalenso nthawi yopitirira:*

199 Penyani! Musaiwale ichi tsopano, pamene ife tikupitirira.

> *Koma mmasiku* (masiku) *a liwu la mngelo wachisanu ndi chiwiri, . . .*

200 Mngelo wotsirizayo, mngelo wapadziko lapansi. Mngelo *uyu* anabwera pansi kuchokera Kumwamba. Sanali Iyeyo; Iye anabwera kuchokera Kumwamba. Koma Iye akuyankhula apa za liwu la mngelo wachisanu ndi chiwiri, amene ali a. . . *Mngelo* amatanthauza "mtumiki," aliyense akudziwa zimenezo, ndi mtumiki kwa m'badwo wa mpingo.

> *. . .mmasiku a liwu la mngelo wachisanu ndi chiwiri, pamene iye adzayamba kuwomba, chinsinsi* (Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, zonsezo, chinsinsi chonsecho) *cha Mulungu chiyenera kutsirizika, monga iye wanenera kwa antchito ake aneneri.*

201 Chinsinsi chonsecho chikufutukulidwa. Ndiwo utumiki wa mngelo ameneyo. Mukuona? Zidzakhala zophweka kwambiri, anthu amangogwera pamwamba pa izo. Ndipo, komabe, izo zidzatsimikiziridwa mwangwiro. Izo basi zidzadziwika mwangwiro. Mukuona? Aliyense amene akufuna kuziwona izo akhoza kuziwona izo. Mukuona? Uko nkulondola. Koma iwo. . .

202 Yesu ananena, monga Iye ananenera pamene Iye anabwera, anati, "Inu muli nawo maso, ndipo simukukhoza kupenya. Yesaya anati inu munatero. Mukuona? Ndipo inu muli nawo

makutu, ndipo inu simukukhoza kumva." Tsopano, chotero ife tikupeza kuti . . .

203 Iyo inandiwopsyeza ine. Ine ndinayang'ana mmbuyo uko pa koloko iyo ndipo ine ndimaganiza kuti iyo inali teni koloko. Koma, ndi, ine—ine ndiri . . . Iyo siinakwane nkomwe naini, panobe, mwaona. Chabwino. Oh, mai! Tiyeni titenge icho tsopano. Zindikirani. Ine ndikuzikonda izi.

204 Enawo, okonzanso, koma, pokhala amuna opambana a Mulungu, anawona chosowekera cha tsikulo, ndipo anabweretsa kukonzanso.

205 Koma Chivumbulutso 10 anati Uthenga wake unali woti udzawulule, osati kudzakonzanso; kudzaulula zinsinsi. Kuwulula zinsinsi! Ndi Mawu mwa munthu. Ahebri 4 ananena, kuti, "Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, kupyoza ngakhale mogawanika mwa fupa, ndi Woulula zinsinsi za mu mtima." Mukuona? Munthu uyu si wokonzanso. Iye ndi woulula, woulula wa (chiyani?) zinsinsi za Mulungu. Pamene mipingo yachimangiriza Icho chonse ndi chirichonse, iye ali woti abwere ndi Mawu a Mulungu ndi kudzachiwulula chinthucho.

206 Chifukwa, iye ali woti "adzabwezeretse Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa makolo." Chikhulupiriro chapachiyambi cha Baibulo chiri choti chibwezeretsedwe ndi mngelo wachisanu ndi chiwiri. Tsopano, oh, momwe ine ndimazikondera izi! Zinsinsi zonse za Zisindikizo, zomwe okonzansowo samazimvetsetsa kwathunthu! Mukuona? Tsopano tayang'anani pa Malaki 4, miniti yokha. Chabwino, inu mungozilemba izo. Iye ndi mneneri, ndipo, "akubwezeretsa Chikhulupiriro choyambirira cha makolo." Tsopano ife tikumuyembekezera munthu ameneyo kuti awonekere poyera. Iye adzakhala wodzichepetsa kwambiri mwakuti mamillioni teni kuchulukitsa ndi mamillioni teni adza . . . Chabwino, padzakhala kagulu kakang'ono kamene kati kadzamvetse Izo.

207 Pamene, inu mukukumbukira tsiku lina, pamene Yohane ankayenera kudza, kunaloseredwa, mtumiki Khristu asanadze, "liwu la mmodzi wofuula mchipululu." Malaki anamuwona iye. Taonani, mutu wa 3 wa Malaki ndiko kudza kwa Eliya amene ankayenera kudza nadzatsogolera kudza kwa Khristu.

208 Inu mukuti, "Oh, ayi, ayi, M'bale Branham. Ndi mutu wa 4." Ine ndikupempha kukhululukira kwanu.

209 Yesu anati iwo unali mutu wa 3. Tsopano mutenge Woyera . . . Inu mutenge Mateyu Woyera, a—mutu wa 11 ndi ndime ya 6, Iye adza—Iye adzanena ichi. Wa 11—mutu wa 11, ine ndikukhulupirira iyo ndi ndime ya 6; ya 4, ya 5, kapena ya 6, cha pamenepo. Iye anati, "Ngati inu mungazilandire izo," pamene Iye ankanena za Yohane, "uyu ndi iye amene ananenedwa, 'Ine ndidzatuma wamthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga.'"

Tsopano muwerenge Malaki 3. Ena a iwo amayesera kuziyika izo ku Malaki 4. Ayi, bwana, sindizo ayi.

210 Zindikirani Malaki 4, mwamsanga pamene wamthenga ameneyo akupita, dziko likuwotchedwa kwathunthu, ndipo olungama akuyenda mu Zakachikwi, pa mapulusa a iwo. Kotero, inu mukuona, ngati mukaziyika izo kukhala iye kumbuyo uko, ndiye—ndiye kuti Baibulo linanena chinachake chimene sichinali chomwecho. Ife takhala nazo zaka thuu sauzande, ndipo dziko silinawotchedwebe, ndipo olungama akukhala mmenemo. Kotero izo ziyenera kukhala mtsogolo. Oh, mai!

211 Ngati mudzafike apa mu Chivumbulutso, ndi kuwona chimene wamthenga ameneyo pa mapeto a m'badwo uno akuyenera kudzachita, ndiye inu mudzawona chimene icho chiri. Iye ayenera kukhala mneneri. Iye ayenera kudzatenga mapeto awa omwe okonzanso awa sanakhoze kuwaona, ndi kuziyika Izo mkati umo.

212 Kodi Mateyu 28:19 angafanizidwe bwanji ndi Machitidwe 2:38, popanda vumbulutso lauzimu la Mulungu? Anthu awa anganene bwanji kuti masiku a zozizwitsa anapita, ndi zina zotero monga choncho, ndipo (huh!) popanda vumbulutso la Mulungu? Njira yokhayo yomwe iwo angadzadziwire konse izo, kudziwa ngati ziri zolondola kapena zolakwika! Mukuona? Koma iwo adutsira mmaseminare. Ine ndikuyembekeza kuti ife tiri nayo nthawi kuti tilowe mu zimenezo.

213 Ine ndikufuna kuti ndifulumire, chifukwa ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu muno kupitirira sabata, inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, izi, kutsegula Zisindikizo izi. Ine ndiri ndi tsiku limodzi, ndipo ine ndikufuna ndidzakhale ndi pemphero la odwala pa tsiku limenelo, ngati ine ndingathe.

214 Tsopano taonani, Malaki 4, iye ndi mneneri, ndipo "akubwezeretsa Chikhulupiriro chapachiyambi cha makolo."

215 Pa nthawi yotsiriza, pamene nthawi ya Chisautso idzabwera . . . Tsopano apa pali kanthu kakang'ono kamene ife tikabwezere mmbuyo, kwa miniti, pamene zaka zitatu ndi theka, kapena, masabata sevente a Daniele, theka lotsiriza la masabata sevente a Daniele, zimene ziri zaka zitatu ndi theka. Tsopano, ife . . . Ndi angati akukumbukira zimenezo, kuchokera mmibadwo ya mpingo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mukuona? "Pali masabata sevente olonjezedwa." Yang'anani mmene izo zinaliri zangwiro. Anati, "Mesiya adzabwera, ndipo Iye adzadulidwa, chifukwa cha nsembe, pakati pa sabata, ndipo chilamulocho chidzasiya." Kenako, zikadalipobe zaka zitatu ndi theka zomwe zikuyembekezeredwa, za Chiphunzitso cha Umesiya kwa Ayuda.

216 Ndipo Mulungu samachita ndi Ayuda ndi Amitundu pa nthawi yomweyo. Iye amachita naye Israeli monga fuko, Amitundu monga munthu payekha. Iye sanatenge konse

Amitundu kukhala Mkwatibwi Wake; Iye akutenga anthu kuchokera mwa Amitundu. Mukuona? Tsopano Iye amachita ndi Israeli ngati fuko. Ndipo tsopano ndi uyo wakhala ukoyo, komwe uko tsopano, monga fuko.

217 Ine ndalandira kalata kuchokera kwa Paul lero, Paul Boyd. Ndipo iye anali kundiuza ine, anati, "M'bale Branham, ndi zoona bwanji! Ayuda awa akadali nako kumverera kwachirendo pa Amitundu, ziribe kanthu zomwe zachitika." Zedi, iwo adzatero. Iwo ayenera kutero.

218 Pamene Martin Luther anapanga kulengeza, kuti, "Ayuda onse ayenera kuthamangitsidwa, ndipo nyumba zawo ziwotchedwe, chifukwa iwo anali otsutsakhristu." Mukuona? Martin Luther anapanga neno limenelo, iyemwini, mu kulemba kwake. Tsopano, Hitler anangokwaniritsa zomwe Martin Luther ananena. Ndi chifukwa chiyani Martin Luther ananena zimenezo? Chifukwa iye anali wokonzanso, osati mneneri.

219 Mulungu, anati, "Mneneri wanga anamudalitsa Israeli, iye anati, 'Aliyense amene adalitsa iwe adzakhala wodalitsidwa, ndipo amene atemberera iwe adzakhala wotembereredwa.'" Angakhoze bwanji mneneri mmodzi kuyima ndi kukana chimene mneneri wina ananena? Iye sangakhoze kuchita zimenezo. Izo ziyenera kukhala mogwirizana, mwaona.

220 Koma icho ndi chifukwa chake iwo amasankha... Mwaona, Germany anayenera kukhala fuko la Chikhristu, ndipo, iwo, momwe iwo anamuzunzira Israeli! Iwo akadali nayo ndodo paphewa lawo, ndipo inu simungawanene iwo. Koma mungokumbukira, Ayuda amene mwakhala muno, inu musadandaule, tsiku likubwera! Mulungu sangakhoze konse kuwaiwala iwo. Iwo anachititsidwa khungu chifukwa cha ife.

221 Inu mukudziwa, Iye anati kwa mneneriyo, Iye... Mneneriyo anafuula mokweza, anati, "Kodi Inu mudzaiwala Israeli?"

222 Iye anati, "Tenga ndodo yoyezera iyo; ndipo kodi kumwamba ndi kwakutali bwanji? Nyanja ndi yakuya bwanji?"

Iye anati, "Ine sindingakhoze kuyeza izo."

223 Anati, "Ine sindingakhoze konse kuiwala Israeli." Awo ndi anthu Ake, antchito Ake.

224 Ndipo Amitundu, ndi apang'ono chabe akutengedwa kuchokera kumeneko, kudzakhala Mkwatibwi Wake. Ndiko kulondola ndendende. Ndiye Mkwatibwiyo.

225 Tsopano, masabata sevente anaperekedwa, mwangwiro, monga Daniele ananena kuti Mesiya akanadzabwera ndipo akanadzadulidwa pakati pa sabata. Ndipo Yesu ananenera kwa zaka zitatu ndi theka. Tsopano, pakati pa izi, zaka zitatu ndi theka za Daniele, pakati pa izo, Iye anadulidwapo. Koma tsopano gawo lotsirizalo ndi nthawi ya Chisautso, kumene mpingo wa Amitundu uli. Oh, izi ndi zopambana! Tsopano

musaphonye. Mkwatibwi akukalowa limodzi ndi Mkwati; kenako, zikadzatha Zakachikwi, akudzayenda pa mapulusa a oyipa.

226 Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chinachake apa, basi pamene ife tiri nacho icho mmalingaliro. Ndiloleni ndingokuwonetsani inu chimene Ilo linanena, chimene Baibulo likunena. Ndipo ife sitingakhoze kuwakana Awa kukhala Mawu a Mulungu. Ngati ife tingatero, ndiye kuti ndife achikunja. Mwaona, ife tiyenera kuwakhulupirira Iwo. Inu mukuti, "Ine sindikuzimvetsa Izo." Ngakhale inenso. Koma ine ndikumuyembekezera Iye kuti awulule Izo. Yang'anani.

> *Pakuti, taonani, likudza tsiku, limene lidzayaka ngati ng'anjo; ndipo onse odzikuza* (monga Achimereka, ndi ena otero), *eya,. . . onse amene akuchita zoipa, adzakhala* ziputu: (Ilo lidzawotcha.) *ndipo tsiku liri nkudza,* limene Ine *ndidzawawotcha iwo, atero* AMBUYE *wa makamu,. . . ilo silidzawasiyira iwo ngakhale muzu* kapena *nthambi.*

227 Ndiye inu muli nayo bwanji gehena Yamuyaya mmenemo ndiye? Mwaona, ndi masiku otsiriza, pamene zinthu izi zikuwululidwa. Palibe malo mu Baibulo pamene amati gehena ndi Yamuyaya. Chotero, kuti ukhale. . . kuti ukhale mu gehena Yamuyaya, iwe udzayenera kukhala ndi Moyo Wamuyaya kuti ukakhale mmenemo. Pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo ndi umene ife tikuwuvutikira. Chirichonse, chimene chinali nacho chiyambi, chiri ndi mathero. "Gehena inalengedwera mdierekezi ndi angelo ake," ndipo idzawonongedwa ndi kudzathetsedwa. Kulondola. Mukuona? Koma pamene izi zidzachitika, "Izo sizidzawasiyira iwo ngakhale muzu kapena nthambi."

> *Koma kwa* iwo *akuwopa dzina langa Dzuwa la chirungamo* lidzawatulukira *limodzi ndi machiritso mmapiko mwake;. . . inu mudzapita,* ndi *kukula monga ana a ng'ombe okulira mu khola.*

> *Ndipo inu mudzawapondereza pansi oyipa; pakuti iwo adzakhala mapulusa pansi pa zidendene za mapazi anu mu tsiku limenelo limene Ine* ndidzac*hita izi, atero* AMBUYE *wa makamu.*

228 Kodi oyipa adzakhala ali kuti chikadzatha Chisautso? Mapulusa.

> *Kumbukirani. . .* malamulo *a Mose. . . amene ine ndinamulamulira. . . iye mu Horebu kwa Israeli yense, ndi malamulo ndi* chiweruzo.

> *Taonani, ine ndidzatumiza* kwa *inu Eliya mneneri lisanadze tsiku lalikuru* ilo *ndi lowopsya la* AMBUYE*:*

229 Ameni! Apa pali Chipangano Chakale chikutsekedwa monga choncho, ndipo apa pali Chipangano Chatsopano chikutsekedwa ndi chinthu chomwe chomwecho. Inu muzilepheretsa chotani izo? Simungakhoze. Penyani, "Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri lisanadze tsiku limenelo."

> *Ndipo iye adzatembenuzira* mitima *ya makolo kwa ana, ndi* mitima *ya ana kwa makolo, kuti ine ndisafike ndi kukantha dziko lapansi ndi themberero*. (Uh!)

230 Ndi zimenezotu pamenepo. Ndiwo Mawu a Ambuye. Iye analonjeza zimenezo. Izo ziyenera kubwera. Ndipo tsopano ngati inu mungazindikire momwe izi zikuchitikira. Ndi zokongola, momwe Mulungu amachitira izo. Mkwatibwi akupita, ali ndi Mkwati. Ndipo—ndiyeno zikadzatha zimenezo, woyipayo akuwotchedwa ndi moto wosazimitsika. Ndipo dziko likadzayeretsedwa, kudzibalanso lokha. Chirichonse chiyenera kuchita zimenezo, chiyenera kudutsa mu chochitika cha kuyeretsedwa.

231 Ziphala zamoto zidzaphulika mu nthawi yopambana yotsirizayo, ndipo dzikoli lidzaphulika, ndi kugeya, ndi kumapita; ndipo zithaphwi zonse izi za tchimo, ndi zonse ziri pa dziko lapansi, zidzasungunuka osakhala kanthu. Ilo lidzayaka ndi moto wonyeketsa chotero, mwakuti zidzakhala ngati bulitchi ija imene imatumiza—mtundu wa—wa inki kubwerera ku chirengedwe chake chapachiyambi. Momwemonso Moto wochokera kwa Mulungu udzakhala wotentha kwambiri, umene udzasintha chinthu cha uve chirichonse kubwerera ku chikhalidwe chake kachiwiri, pamene Satana ndi tchimo lonse adzawotchedwa, ndi chirichonse. Ndiyeno ilo lidzakhala lokongola monga momwe linkakhalira mmunda wa Edeni. Kulondola. Oh, ora lopambanalo lagona kutsogolo kwathu basi!

232 Mu nthawi ya Chisautso . . . Apa pali chimene ine ndikufuna kuti inu muzindikire tsopano, kanthu kakang'ono kamene ine ndakagwetseramo umu. Mu nthawi ya Chisautso iyi, Mkwatibwi atatha kuyitanidwa atuluke, ndipo mpingo ukupita kudutsa mu nthawi ya Chisautso, handiredi ndi forte foro sauzande akuyitanidwa ndi mboni ziwiri za Chivumbulutso 11. Tsopano penyani. Iwo adzanenera, masiku wani sauzande thuu handiredi ndi sikisite, atavala ziguduli.

233 Tsopano, ife tikudziwa kuti kalendala ya Chiroma iyi ili ndi . . . Ife tiri nawo masiku twente-eyiti ndipo, nthawizina, ndi sarte, ndi sarte-wani. Koma, kwenikweni, kalendala imawerenga chonchi, masiku sarte ku mwezi uliwonse. Kulondola. Ndipo mutenge handiredi . . . masiku sauzande thuu handiredi ndi sikisite, ndipo mugawe ndi sarte kwa iwo, ndipo onani chimene inu mukupeza. Zaka zitatu ndi theka, ndendende pa dontho. Ndiyo nthawi imene yaikidwa, nthawi yakuti Uthenga wa Umesiya ukalalikidwe kwa Israeli, monga

izo zinkakhalira mmbuyomo. Pamene Iye akudzabwereranso ndi kukadzizindikiritsa Yekha, mwa chophiphiritsa kuti pamene Iye akubwera . . .

234 Pamene, Yosefe anatengedwera kupita mdzikolo, ndipo anakanidwa ndi abale ake, chifukwa iye anali munthu wauzimu. Iye ankakhoza kuwona masomphenya ndi kumasulira maloto. Ndipo pamene iye anatero, iye anatengedwera kupita ku dzikolo ndipo anakagulitsidwa ndi pafupifupi zidutswa sarte za siliva. Iye ankaimira Khristu, ndendende, chifukwa iwo unali Mzimu wa Khristu mwa iye.

235 Zindikirani chimene chinadzachitika kenako. Ndipo zindikirani kuti, pamene iye anachita ichi, iye anakaikidwa mu ndende, ndipo munthu mmodzi anapulumutsidwa ndipo winayo anatayika. Ndendende Yesu, pamene Iye anali mu ndende pa mtanda, wakuba mmodzi anapulumutsidwa ndipo winayo anatayika, ndendende.

236 Anatayidwa mkati mwa manda, kuganiziridwa kuti anali wakufa, ndipo anatulutsidwamo, nakwezedwera kudzanja lamanja la Farao, mwakuti palibe amene akanakhoza kumuwona Farao popanda kumuwona Yosefe poyamba. Yesu akukhala pa dzanja lamanja la Mulungu, ndipo palibe munthu amene angakhoze kudza kwa Atate popanda kudzera mwa Mwana. Kulondola.

237 Ndipo zindikirani kuti nthawi iliyonse pamene Yosefe akudzuka, pamene Yosefe akudzuka kuchokera ku dzanja lamanja la mpando wachifumuwo. Penyani! Ulemelero! Yosefe ankakhala pamenepo, cha ku dzanja lamanja la Farao. Ndipo pamene Yosefe anali kudzuka, kuchoka pa mpando wachifumuwo, lipenga linkawomba. “Gwadani pamawondo, aliyense! Yosefe akubwera!”

238 Pamene Mwanawankhosa uyo adzachoka pa Mpandowachifumu, kutsidyako, pa masiku Ake a ntchito ya umkhalapakati, pamene Iye adzachoka pa Mpandowachifumu kumeneko, ndi kudzatenga Bukhu ilo la Chiwombolo ndi kumapita, bondo lirilonse lidzagwada. Ndi Uyo pamenepo. Zindikirani.

239 Ndipo pamene Yosefe, anakanidwa ndi abale ake, iye anapatsidwa mkazi wa Amitundu. Potifara anali atamupatsa iye. . . Kapena, Farao anampatsa iye a—mkazi wa Amitundu, ndipo iye anabala ana Amitundu, theka Wamitundu ndi theka Chiyuda. Iwo anapereka choyimira chachikulu. Pamene Yakobo anali kuwadalitsa iwo, Efremu mbali imodzi ndi Manase kumbali inayo, iye anasemphanitsa manja ake namupatsa mwana wamng’onoyo mdalitso. Ndipo ana awiriwo anawonjezeredwa kwa mafuko thwelovuwo, amene anali teni okha pa nthawiyo, ndipo iye anawadalitsa iwo mwa Yakobo mwiniwake. Ndipo Yosefe, mwana wake mneneri, atayima

pamenepo, anati, “Atate, inu mwachita molakwitsa.” Anati, “Inu mwayika dalitso la dzanja lanu lakumanja pa mwana wamng’ono, pamene ilo limayenera kupita pa wamkuluyo.”

240 Ndipo iye anati, “Ine ndikudziwa kuti manja anga asemphanitsidwa, koma Mulungu anawasemphanitsa iwo.” Chifukwa chiyani? Israeli, pokhala nawo ufulu wokhala Mkwatibwi, anakana ndipo anagulitsa maufulu awo obadwa nawo, ndipo . . . anachoka kwa mwana wamkulu, Israeli, nkupita kwa watsopano, Wamitundu. Ndipo madalitsowo anabwera kuchokera kumeneko, kudzera pa mtanda, kupita kwa Amitundu.

241 Koma zindikirani zitatha zimenezo, mwaona, kudzera apo, pamene onse . . . Iye anali atatenga mkwatibwi wake. Koma pamene anyamata awo anabwera uko kuti adzagule chakudya . . .

242 Oh, ndi chithunzi chokongola chomwecho! Ine ndachoka ku Chisindikizo, koma ine ndikungoyenera kunena izi, mwaona, chifukwa inu muchimvetsa chithunzicho bwinoko, ine ndikukhulupirira. Zindikirani.

243 Tsopano, pamene iwo anabwera kudzagula chakudya, inu mukudziwa, Yosefe anawazindikira iwo pomwepo. Ndipo Yosefe anali mwana wochita bwino. Zinalibe kanthu kumene iye ankapita, uko nthawizonse kunkachita bwino.

244 Inu muyembekeze mpaka Iye adzabwere ku dziko lapansi kachiwiri; muyembekeze mpaka Yosefe wathu adzabwere! Mukuona? “Chipululu chidzabiriwira ngati duwa, ndipo Dzuwa la Chirungamo lidzatulukira liri ndi machiritso mmapiko Ake.” Oh, mai! Akaloga onse cha ku Arizona adzafutukuka kukhala mitengo yokongola, ndipo iyo—ndipo iyo idzakhala yokongola.

245 Zindikirani, apa iye akutulukira, ndipo iye akuchita kandale pang’ono pa iwo pamenepo. Ndipo iye akutumiza, ndipo iye akuti, “Kodi abambo anga akadali moyo?” Mukuona? Iye ankafuna kudziwa ngati abambo ake a mnyamatayo anali moyo. Anati, “Inde.” Iye ankadziwa kuti ameneyo anali mchimwene wake. Koma kodi inu munazindikira pamene iye anakonzeka kuti adziwulule yekha kwa abale ake?

246 Ndipo iye anamupeza Benjamini wamng’ono, amene anabadwa chichokereni cha iye. Ndipo uyo akuimira Ayuda awa, handiredi ndi forte-foro sauzande awa amene akusonkhana kumeneko tsopano chichokereni cha Iye. Ndipo pamene Iye anabwerera, Iye anati . . . Iye anayang’ana pa Benjamini; mtima wake unali pafupi kuti usweke.

247 Ndipo, kumbukirani, iwo anali ndi . . . iye . . . Iwo sankadziwa kuti iye akanakhoza kuyankhula Chihebri. Iye amatenga wotanthauzira. Iye ankachita ngati kuti anali Wachiigupto. Mukuona? Ndiyeno pamene zinadzadziwika, iye ankafuna kudzizindikiritsa yekha, iye anakhala akuyang’anabe

pa Benjamini wamng'onoyo. Ndipo, kumbukirani, iye anamuchotsapo mkazi wake. Iye anali mnyumba yachifumu pamene iye ankadzizindikiritsa yekha kwa abale ake.

248 Ndipo Mkwatibwi wa Amitundu, Mkaziyo, Yesu atatha kukanidwa ndi anthu Ake Omwe, Iye anakamutenga Mkwatibwi wa Amitundu. Ndipo adzamutenga Iye kuchokera kuno, kupita ku Nyumba yachifumu, ku Nyumba ya Atate Ake mu Ulemelero, kukachita Phwando la Chikwati. Ndipo adzazemba kubwerera kumeneko, kuti akadzizindikiritse Yekha kwa abale Ake, handiredi ndi forte-foro sauzande . . . ? . . . nthawi imeneyo.

249 Apo iye wayima. Ndipo, kumbukirani, tayang'anani pa chiphiphiritsocho mwangwiro. Ndipo pamene iye anabwerera kumene izi zinali, iye anayang'ana pansi kwa iwo, ndipo iye anati—iye anati . . . anayamba kuyang'ana. Ndipo iwo anayamba kuyankhula. Iwo anati, "Tsopano, Rubeni, iwe ukudziwa kuti ife tiri mu zimenezo tsopano, mwaona. Chifukwa, iwe ukudziwa chimene ife tinachita. Ife tamubweretsa mwana uyu mu vuto ili. Tsopano, ife sitimayenera kumugulitsa m'bale wathu." Uyo anali m'bale wawo atayima pamenepo, kalonga wamphamvu uyo, ndipo iwo sankadziwa izo.

250 Ndi chifukwa chake Israeli sangakhoze kumumvetsa Iye lero. Sindiro ora lake panobe kuti azidziwe izo.

251 Ndiyeno, iye, iwo ankaganiza kuti iye sakanakhoza kumva Chihebri, koma iye anali akumvetsera pomwepo pa iwo. Iwo anati, "Tsopano ife tiri mu zimenezo." Ndipo Yosefe, pamene iye anayang'ana pa iwo, iye sakanakhoza kuzipirira izo mopitirira.

252 Tsopano, kumbukirani, mkazi wake ndi ana anali mnyumba yachifumu pa nthawiyo. Oyera atachokapo, mu kukhalapo.

253 Ndipo iye anati, "Ndine Yosefe, mchimwene wanu." Ndipo iye anathamangira pamenepo ndipo anakamugwira Benjamini wamng'ono, anagwera pa khosi lake, ndipo anayamba kulira. Mukuona? Ndipo iye anazidziwitsa yekha.

254 Ndiye kenako iwo anati, "Tsopano ife tikudziwa kuti tiziona, pakuti ife tinamugulitsa iye. Ife ndife amene tinamugulitsa iye. Ife tinali amene tinayesera kumupha iye, tsopano ife tikudziwa kuti iye atipha ife."

255 Iye anati, "Ayi, musadzikwiyire nokha, inu munangochita izo kuti musunge moyo. Ndi chifukwa chake Mulungu anandituma iza ine kuno."

256 Ndipo pamene Iye akuzidziwitsa Yekha, Baibulo linati . . . pamene ife tikudutsa mu izi. Pamene Iye akuzidziwitsa Yekha kwa handiredi ndi forte-foro sauzande awo kumeneko, Benjamini wamng'ono wa lero, ndi otsalira a Ayuda awo atsalira kumeneko; pamene Iye akuzidziwitsa Yekha, iwo adzanena kuti, "Kodi Inu munazitenga kuti zipsyera zimenezo? Kodi izo zikuchita chiyani mdzanja Lanulo?"

257 Iye adzati, "Oh, Ine ndinazitenga izo mnyumba ya abwenzi Anga." Mukuona? Oh, ndiye iwo adzazindikira kuti anamupha Mesiya. Koma kodi Iye adzanena chiyani? Mofanana ndi momwe Yosefe anachitira izo. "Inu munachita izo kuti mupulumutse moyo; musati . . . kupulumutsa moyo. Musadzikwiyire nokha." Chifukwa, chakuti, Amitundu sakanabweretsedwa mkati ngati Ayuda akanapanda kuchita njomba yophimba mmaso iyo. Kotero, Iye anapulumutsa moyo wa Mpingo, mwa zinthu zimene iwo anazichita. Kotero ndi zimenezotu. Ndi chifukwa chake, lero, iwo sangakhoze kumvetsa Izi; ilo sindiro ora lake.

258 Ife sitikanamvetsanso zinthu izi mpaka nthawi itafika kuti Izo zimvetsedwe. Oh, mai! Mabingu Asanu Ndi Awiri a Chivumbulutso! Mulole Iye amuwonetse Mkwatibwi momwe angakonzekerere chikhulupiriro chachikulu chosandulitsa!

259 Tsopano tiyeni tifulumire, chifukwa tiribe pafupi maminiti fifitini, twente panobe.

260 Tsopano, kodi kavalo woyera uyu akutanthauza chiyani? Ndiroleni ine ndiwerenge . . . Ine ndakhala ndiri kutali kwambiri; mundikhululukire ine chifukwa chopita kutali ndi phunziro langa. Koma, koma ine ndiwerenga ndimeyo kachiwiri, ndime ziwirizo.

> *Ndipo ine ndinawona pamene Mwanawankhosa* anali *atatsegula chimodzi mwa zisindikizozo, ndipo ine ndinamva, ngati kuti* linali *phokoso la bingu,* ndipo *chimodzi cha zamoyo zinayi chinati, Bwera . . . udzawone.*
>
> *Ndipo ndinawona, ndipo taonani kavalo woyera: . . .*

261 Tsopano ife tikupita ku ndime ya 2.

> *. . . kavalo woyera: ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo uta; ndipo korona anaperekedwa kwa* iye, (iye analibe uyo pa nthawiyo) *. . . kwa iye: ndipo iye anapita akugonjetsa, ndi kukagonjetsa.*

262 Ndizo zonse za icho. Ndicho Chisindikizocho. Tsopano tiyeni tipeze zophiphiritsazo.

263 Ife tinapeza chimene Bingu limatanthauza. Izo ziri mwangwiro, ife tikudziwa zimenezo, mwaona. Bingu linali Liwu la Mulungu, pamene Chisindikizocho chinatsegulidwa.

264 Tsopano, kodi kavalo woyera akutanthauza chiyani? Tsopano, apa ndi pamene vumbulutsolo likubwera. Ndine wotsimikiza basi za izi, monga ine ndaimira pano, kudziwa kuti awa ndi Mawu.

265 Ine ndawerengapo bukhu lirilonse pa izo limene ine ndikanakhoza kulipeza. Ndipo ndi . . . ine . . . Nthawi yotsiriza imene ine ndinali—ndinayesera kuti ndidutse mu izo, kuphunzitsa chabe izo, pafupifupi zaka sarte zapitazo, ine ndinatenga bukhulo . . . Winawake anali atandiuza ine

kuti a Adventist anali nako kuwala kochuluka pa Kudza kwachiwiri kwa Khristu kuposa anthu aliwonse amene iwo ankawadziwa, kotero ine ndinapeza ena a mabuku awo abwino, kuti ndiwerenge izo. Ine ndinapeza bukhu la Smith la Daniele, la mavumbulutso. Ndipo iye anati kavalo woyera uyu amene anatulukira apo anali woyera, ndipo chiphiphiritso chake chinali mgonjetsi. Ndipo mu kugonjetsa uku. . . Ambiri a inu abale a Adventist pano mukulidziwa bukhulo, ndiponso ambiri ena a inu, nanunso, powerenga izo. Ndipo—ndipo ena, ine ndinawerenga awiri kapena atatu. Ine ndinawerenga, ndipo ine sindingatchule. . . Pali mabuku ena awiri amene ine ndinawerenga, ndipo anthu onsewo ankavomereza kuti uko kunali kulondola. Iwo anali aphunzitsi abwino, ayenera kukhala ena mwa opambana, okhala nako kuwala kopambana. Kotero ine ndinaganiza, "Chabwino, ngati ine sindikudziwa, ine ndidzangonena zimene iwo ananena, kuyesetsa kuphunzitsa izo mwanjira imeneyo."

266 Iwo anapereka kufotokoza kwabwino kwambiri kwa izo, chomwe izo zinkatanthauza kwenikweni. Ndipo iwo anati, "Tsopano, apa pali kavalo woyera, ndipo kavalo woyera ndi mphamvu, wopereka mphamvu." Ndipo anati, "Munthu amene anakhala pa iye, anali—kavalo woyera, unali Mzimu Woyera umene unatulukira mu m'badwo woyambirira ndipo unagonjetsa m'badwo umenewo kwa Ufumu wa Mulungu. Iye anali nawo uta mdzanja lake, chimene chinkatanthauza, monga Cupid, iye ankaponyera mivi yachikondi kulowa m'mitima ya anthu, chikondi cha Mulungu, ndipo iye anagonjetsa."

267 Tsopano, izo zikumveka bwino kwambiri, koma izo si Choonadi. Ayi, bwana. Eya. Izo sizinali. Choyera chimatanthauza kulungama. Ife—ife tikuzindikira zimenezo. Choyera chimatanthauza kulungama. Aphunzitsi anaphunzitsa izo, kuti iwo unali Mzimu Woyera ukugonjetsa mu m'badwo woyamba; koma vumbulutso langa, mwa Mzimu Woyera, si mwanjira imeneyo.

268 Vumbulutso langa, mwa Mzimu Woyera, ndiro: Khristu ndi Mzimu Woyera ndi Munthu yemwe yemweyo, kokha mwa mawonekedwe osiyana. *Kotero, apa* payima Khristu, Mwanawankhosa. Ife tikudziwa kuti Iye anali Mwanawankhosa. Iye anali atayima *apa* ali ndi Bukhu mdzanja Lake; ndipo *apo* pakupita wokwera pa kavalo woyera, mwaona, kotero iwo sunali Mzimu Woyera.

269 Tsopano, icho ndi chimodzi cha zinsinsi za mmasiku otsiriza, momwe Khristu angakhalire anthu atatu mwa Mmodzi. Si anthu atatu osiyanasiyana, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, kukhala Amulungu atatu, monga autatu amayesera kutiuza ife kuti Izo ziri. Ndi atatu, ndi mawonetseredwe atatu a Munthu yemwe yemweyo. Kapena, inu mukhoza kuwatcha iwo maudindo atatu. Ngati iwe ukuyankhula kwa atumiki, iwe sungagwiritse ntchito

udindo; chifukwa, chabwino, ine ndinapezeka ndikuganiza, kuti ndiri pa tepi. Kotero ine ndikuwuzani inu. . . Chifukwa, Khristu sakanakhoza kunena kuti, "Ine ndidzapempha udindo Wanga, ndipo Iwo udzakutumizirani inu udindo wina." Ife tikudziwa zimenezo. Koma ngati inu mukufuna kuchipanga icho. . . Ndi zikhumbo zitatu za Mulungu yemwe yemweyo. Mukuona? Si Amulungu atatu. Zikhumbo zitatu za Mulungu yemweyo! Mukuona?

270 Ndipo kotero Khristu akanakhoza bwanji kukhala kunja *uko*, kavalo woyera, akugonjetsa, ndipo atayima *apa* ali ndi Bukhu mdzanja Lake? Si choncho, ngakhalebe. Uyo si Khristu.

271 Zindikirani tsopano, Mzimu Woyera (mu vumbulutso) ndi Khristu, ndi, Mzimu Woyera ndi Khristu mmawonekedwe ena. Kulondola.

272 Zindikirani, iye ndi Mwanawankhosa amene anatsegula Mabukhu, ndipo Mwanawankhosayo ndi Khristu. Ndipo Khristu sakuwonekanso, kuchokera pamenepo, koma Iye akuwonekera mu Bukhu la Chivumbulutso, mutu wa 19, akubwera pa kavalo woyera.

273 Ngati inu mungafune kuti muwerenge zimenezo, tiyeni titsegule ku Chivumbulutso 19:11, sikisi-. . . Ndipo tingowerenga izo mofulumira ndithu tsopano pamene tiri—pamene tiri. . . Ife tiri nayo nthawi yokwanira, ine ndikuyembekeza, kotero zipangitsa izo kukhala bwino pang'ono pokha kwa ife. 19, 19:11, kuyambira pa ndime ya 11, ndipo tiwerenge mpaka mmusi, kuphatikiza ya 16.

> *Ndipo ine ndinawona kumwamba kutatseguka,. . . taonani kavalo woyera;* (osati pa dziko lapansi; Kumwamba, mwaona) *ndipo iye wakukhala* pa *iye anatchedwa Wokhulupirika. . . Woona,. . . mu* chirungamo *iye akuweruza ndi kuchita nkhondo.*
>
> *Maso ake anali. . .* malawi *a moto, ndipo pamutu pake* panali *makorona ambiri,* (tayang'anani pa koronayo!); *ndipo iye anali nalo dzina lolembedwa, limene palibe munthu* ankalidziwa, *koma. . . mwiniwake.*

274 Ine ndikukhumba ndikanayima pa ilo miniti yokha. Oh, mai! Ine ndiri nalo lingaliro labwino, koma. . . Mwinamwake ine ndikanakhoza, ngati inu. . . [Osonkhana akuti, "Pitirirani!"—Mkonzi].

275 Mwaona, palibe amene akulidziwa Ilo. Kodi inu munadziwapo kuti Dzina la *Yehova* si lolondola? Aliyense amadziwa. Dr. Vayle, inu mukudziwa kuti izo nzoona. Omasulirawo sakanakhoza konse kulimasulira Ilo. Ilo limatchulidwa J-u-h-v. . . J-v-h-u, ine ndikutanthauza. Ilo si *Yehova*. Iwo sakanakhoza kulikhudza Ilo. Iwo sakudziwa chimene Ilo liri. Analitcha Ilo *Yehova*, koma ilo silinali Dzina Lake.

276 Penyani, nthawi iliyonse chigonjetso chikapambanidwa, kapena chinachake chikachitika, dzina limasinthidwa.

277 Tayang'anani mmasiku a Abrahamu. Iye anali, poyamba, Abram, ndipo sakanakhoza konse kukhala naye mwana ameneyo mpaka dzina lake litasinthidwa kukhala Abraham. Ndipo Sarra, S-a-r-r-a, sakanakhala nako kanthu koma chiberekero chakufa mpaka dzina lake litasinthidwa kukhala S-a-r-a-h.

278 *Yakobo* amatanthauza "wolanda, wonyenga," ndipo ndicho chimene iye anachita. Iye anadziveka chikopa cha nkhosa pa iyemwini, ndipo anawanyenga abambo ake mneneri, kuti atenge maufulu obadwa nawo. Iye ananyika timitengo ta popula mmadzi, nazilocha izo, kumaziwopsyeza ng'ombe pamene izo zinali ndi bele ndi. . .ndi ana awo, kuti apange ng'ombe ndi nkhosa za mangamanga. Sanali kanthu koma wonyenga!

279 Koma usiku wina iye anagwira Chinachake chenicheni, ndipo iye anadziwa kuti Icho chinali chenicheni. Ndipo iye anakhala nacho Icho, ndipo iye anagwiritsitsa mpaka iye anagonjetsa. Ndipo dzina lake linasinthidwa, ndipo anamutcha *Israeli*, kutanthauza "kalonga wokhala nayo mphamvu pamaso pa Mulungu."

280 Nkulondola uko? Wogonjetsa aliyense!

281 Simoni anali nsodzi. Koma pamene chikhulupiriro chake chinagwira ndi kudziwa kuti ameneyo anali Yesu, pamene Iye anamuuza iye kuti Iye anali Mesiya, ndi kumuuza iye yemwe dzina lake linali ndi lomwe linali dzina la abambo ake, iye anagonjetsedwa, ndipo anasintha kuchokera pokhala Simoni nkudzakhala Petro.

282 Saulo, dzina labwino. Saulo, anali mfumu nthawi yina mu Israeli, koma iye, *Saulo*, silinayenere kukhala mtumwi. Likhoza kukhala bwino kwa mfumu, koma osati mtumwi. Kotero Yesu anasintha dzina lake (kuchokera ku chiyani?) kuchokera pokhala Saulo nkudzakhala Paulo.

Tayang'anani pa "Ana a bingu," ndi mpaka mmusi.

283 Ndipo, Yesu, Dzina Lake pa dziko lapansi linali "Muwomboli," Yesu. Pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anali Muwomboli, izo nzoona. Koma pamene Iye anagonjetsa imfa ndi gehena, nazilaka izo, nakwera Mmwamba, Iye analandira Dzina latsopano. Icho ndi chifukwa chake iwo amafuula momwe iwo amachitira, ndipo iwo samamva kanthu.

284 Izo zidzawululidwa mu Mabingu. Uh-huh. Mukuona? Zindikirani zinsinsi. Iye akubwera, atakwera. . .Payenera kukhala Chinachake choti chiwusinthe Mpingo uwu. Inu mukudziwa zimenezo. Payenera kukhala Chinachake. Zindikirani, "Palibe munthu ankadziwa, koma Iyemwini."

Tsopano, zindikirani, "Palibe munthu ankadziwa, koma Iyemwini."

Ndipo iye anavekedwa mkanjo woviikidwa mu mwazi: ndipo dzina lake linkatchedwa Mawu a Mulungu.

Oh, mai! Zindikirani!

Ndipo ankhondo amene anali kumwamba anamutsatira Iye ali pa akavalo oyera, atavala bafuta wofewa, woyera ndi waukhondo.

Ndipo kuchokera m'kamwa mwake munatuluka *lupanga lakuthwa, kuti ndi ilo iye akakanthe mafuko: ndipo iye adzawalamulira iwo ndi ndodo ya chitsulo: ndipo iye* adzaponda *moponderamo mphesa wa ukali ndi mkwiyo wa Mulungu Wamphamvuzonse.*

Ndipo iye anali nalo *pa chovala chake ndi pa ntchafu yake dzina lolembedwa, MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE.*

285 Apo pakudza Mesiya. Ndi Uyo *apo*; osati munthu uyu ali pa kavalo uyu kumbuyo *kuno*. Tayang'anani kusiyana kwake. Apa Iye wayima ali ndi Bukhu mdzanja Lake, *apa*, ntchito ya chiwombolo ili chabe . . . Iye anali asanatengebe malo Ake apobe. Kotero, uyo sanali Khristu amene anatuluka, Mzimu Woyera.

286 Osati kutsutsana ndi amuna otchuka amenewo. Ayi, bwana, ine sindimachita zimenezo. Ine sindingafune kuti ndichite zimenezo, koma ili ndi lomwe—lomwe vumbulutso langa la Izo liri. Mukuona? Ngati inu muli ndi chinachake chosiyana, chabwino, izo ziri bwino, koma izo siziri bwino ndi ine. Mukuona, ine—ine ndikuzikhulupirira Izo mwanjira iyi. Mwaona, tsopano, inu mukudziwa chiyani. Mukuona?

287 Ndipo, zindikirani, Khristu sakuwonekanso, mwaona, kuyambira pa nthawi imeneyo. Koma Iye ali pa kavalo woyera. Kotero ngati munthu uyu akukwera kavalo woyera, iye ndi wonamizira chabe wa Khristu. Mukuona? Inu mukumvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

288 Zindikirani, wokwera pa kavalo woyerayo alibe dzina lirilonse. Iye akhoza kugwiritsa ntchito maudindo awiri kapena atatu, mukuona, koma iye alibe dzina lirilonse.

289 Koma Khristu ali nalo Dzina! Ndi chiyani ilo? Mawu a Mulungu. Ndicho chimene ilo liri. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu, anasandulika thupi." Mukuona? Wokwerayo alibe dzina, koma Khristu akutchedwa "Mawu a Mulungu." Ndicho chimene Iye ali. Iye akutchedwa chomwecho. Tsopano Iye ali nalo Dzina limene palibe munthu akulidziwa; koma Iye akutchedwa, "Mawu a Mulungu."

Munthu uyu sakutchedwa kanthu, mwaona, koma iye ali pa kavalo woyera.

290 Wokwerayo alibe mivi ya uta wake. Kodi inu munazindikira? Iye anali ndi uta, koma apo palibe chirichonse chikunenedwa za kukhala nayo mivi iliyonse, kotero iye ayenera kukhala wopusitsa. Kulondola. Mwinamwake iye ali ndi mabingu ambiri, koma alibe mphezi. Koma inu mupeza kuti, Khristu anali nazo ziwiri zonse mphezi ndi bingu, pakuti kuchokera mkamwa Mwake mukutuluka Lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo Iye akukantha mafuko ndi Ilo. Munthu uyu sangakhoze kukantha kalikonse, mwaona, koma iye akusewera gawo la wachinyengo. Iye akupita, atakwera pa kavalo woyera, akupita uko kuti akagonjetse.

291 Khristu ali nalo Lupanga lakuthwa, ndipo, penyani, Ilo likubwera kuchokera mkamwa Mwake. Mawu amoyo, ndiwo, Mawu a Mulungu owululidwa kwa antchito Ake. Monga Iye ananenera kwa Mose, "Pita, ukayime apo, ndipo ukagwire ndodo imeneyo kutsidyako; ukaitane ntchentche," ndipo apo panali ntchentche. Ndithudi. Chirichonse chimene iye ananena, Iye amachichita icho; ndipo icho chimafika pochitika, Mawu Ake amoyo. Mulungu ndi Mawu Ake ndi Munthu yemweyo. Mulungu ndi Mawu.

292 Ndi ndani wokwera mwachinsinsi uyu wa m'badwo wa mpingo woyamba ndiye? Ndi ndani iye? Tiyeni tiganize za izo. Ndi ndani uyu wokwera mwachinsinsi amene akuyambira mu m'badwo wa mpingo woyamba ndipo akukwera mpaka kukafika uko ku Muyaya, akupita mpaka kumapeto?

293 Chisindikizo Chachiwiri chikutulukira ndipo akupitirirabe mpaka uko kumapeto. Chisindikizo Chachitatu chikutulukira ndipo akupitirirabe mpaka kumapeto. Chachinayi, Chachisanu, Chachisanu Ndi Chimodzi, Chachisanu Ndi Chiwiri, chirichonse cha izo, chikutsirizira kuno kumapeto komwe. Ndipo pa nthawi yotsiriza, Mabuku awa amene akhala okulungidwa nthawi yonseyi, ali ndi zinsinsi izi mmenemo, Iwo akumatulidwa. Kenako umo mukutuluka zinsinsi, kuti tiwone zomwe izo ziri. Koma, makamaka, izo zinayambira mu m'badwo wa mpingo woyamba, chifukwa mpingo, m'badwo wa mpingo woyamba, unalandira Uthenga wonga Uwu.

294 "Wokwera pakavalo woyera anatulukira." Mukuona? Ndi ndani ameneyu? Iye ndi wamphamvu mu mphamvu yake yogonjetsera. Iye ndi munthu wamkulu mu mphamvu yake yogonjetsa. Inu mukufuna ine ndikuuzeni inu amene iye ali? Iye ndi wotsutsakhristu. Ndendende chomwe iye ali. Tsopano, chifukwa, inu mukuona, ngati ali wotsutsakhristu; Yesu ananena, kuti, "Iwiriyo ikanadzakhala yoyandikana kwambiri mpaka ukanadzanyenga ngakhale Osankhidwa omwe (Mkwatibwi) ngati kukanakhala kotheka." Wotsutsakhristu, ndi mzimu wotsutsakhristu.

295 Kumbukirani, mmibadwo ya mpingo, pamene ife tinatsegula

m'badwo wa mpingo woyamba kumbuyo uko, ife tinapeza kuti Mzimu Woyera unkatsutsa chinthu chinachake chimene iwo anachiyamba mu m'badwo wa mpingo umenewo, ndipo icho chinkatchedwa "ntchito za Anikolai." Inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. *Nikao* amatanthauza "kugonjetsa." *Laity* amatanthauza "mpingo," anthu wamba. *Chinikolai*, "kugonjetsa anthu wamba." "Kuwuchotsapo Mzimu Woyera mu Mpingo ndi kuwupereka Iwo wonse kwa munthu mmodzi woyera. Kumulola iye kukhala bwana wa chonsecho." Inu mwadutsamo mu zimenezo, mwaona, Chinikolai. Zindikirani, Chinikolai chinali "zo—zoyankhulidwa" mu mpingo umodzi. Icho chinadzakhala "chiphunzitso," mu m'badwo wa mpingo wotsatirawo. Ndipo mu m'badwo wa mpingo wachitatu, icho chinali "chokakamiza," ndipo iwo anadzakhala nawo Msonkhano waku Nicaea. Ndipo panali pamenepo chinadzapangidwa kukhala chi—chiphunzitso mu mpingo. Ndipo chinthu choyamba chimene chinachitika chinali chiyani? Bungwe linachokera mu zimenezo! Tsopano, nkulondola uko?

296 Ndiwuzeni ine kumene mpingo woyamba wa bungwe unachokera. Mpingo wa Roma Katolika! Ndiuzeni ine ngati mu Chivumbulutso samanena, mu Bukhu la Chivumbulutso 17, kuti, "Iye anali hule, ndipo ana ake aakazi anali timahule." Icho ndi chinthu chomwecho chimene chinachita bungwe limodzi naye, "timahule." "Kutenga chonyansa, uve wa ziwerewere zawo, kukhala ziphunzitso." "Kumaphunzitsa malamulo a anthu ngati Chiphunzitso." Zindikirani.

297 Yang'anani, iye akuyamba kupita kukagonjetsa. Zindikirani, iye alibe korona. Wokwera pa kavalo woyera, amene ine ndikumukamba apa. Mukuona? "Uta; ndipo korona anapatsidwa kwa iye, pambuyo pake." Mukuona? Iye analibe korona, kuyamba ndi kuyamba, koma korona anadzapatsidwa kwa iye. Zindikirani, mtsogolo mwake iye anadzapatsidwa korona, eya, atatu a iwo, atatu pa mmodzi. Izo zinali zaka firii handiredi mtsogolo mwake, ku Nicaea Council. Pamene iye anawuyambitsa, mzimu wa Chinikolai, kuti upange bungwe pakati pa anthu. Ndiyeno iwo unapitirira, kumapitirira, kumapitirira, chinadzakhala "choyankhulidwa," kenako iwo unadzakhala "chiphunzitso."

298 Inu mukukumbukira, Khristu akuyankhulanso kwa mpingo, anati, "Iwe umadana nazo ntchito za Anikolai, zimene Ine ndimadana nazo, nanenso." Kuyesetsa kugonjetsa, kuwutengera Mzimu Woyera pa munthu mmodzi yekha woyera; iye ankakhoza kukhululukira machimo onse ndi chirichonse.

299 Ndipo ife tangowerenga izo pamenepo, Paulo anayankhula za izo. Chinthu icho chikanadzakhala mmasiku otsiriza. Ndipo iye sakanakhoza kuwululidwa kufikira mmasiku otsiriza.

"Ndiye, Iye amene amaloleza, adzawuchotsa Mzimu wa Mulungu pamenepo; ndiye kenako iye adzadziulula yekha."

300 Lero iye ali pansi pa kudzizimbaisa kwa kavalo woyera. Penyani momwe iye akusinthira kuchokera pa kavalo woyera uyo, mu maminiti pang'ono. Iye sakukhala kavalo woyera kokha; iye akudzakhalanso chirombo chokhala nayo mitu yambiri ndi nyanga. Mukuona? Mukuona? Kavalo woyera, iye ndi wachinyengo tsopano, ndipo ndicho chifukwa chake anthu sanazidziwe izi nthawi yonseyi. Iwo ankalingalira pa zimenezo. Koma ndi izi apa tsopano, izo ziwululidwa mwa Lemba. Zindikirani.

301 Pamene Chinikolai, mwaona, wotsutsakhristu, iye potsiriza akudzakhala mwa munthu, kenako iye akudzavekedwa korona. Pamene iye akuyamba, ngati mzimu wa Chinikolai mu mpingo, iye ndi mzimu. Inu sumungawuveke korona mzimu. Koma zaka firii handiredi mtsogolo mwake, iye anadzakhala papa, ndipo kenako iwo anamuveka iye korona. Iye analibe korona, kuyamba ndi kuyamba. Koma iye anadzapeza korona, mtsogolo mwake, mukuona, pamene mzimuwo unadzakhala mu thupi. Mukuona? Iye anadzakhala munthu. Chiphunzitso cha Chinikolai chinadzakhala munthu, zitatero iwo akanakhoza kumuveka iye korona. Iwo sakanakhoza kuchita zimenezo, chifukwa, iye anali chiphunzitso chabe.

302 Ulemelero! Zindikirani! Ndipo pamene Mzimu Woyera uwu umene ife tiri nawo usandulika thupi kwa ife, Umene ali pakati pathu tsopano mwa mawonekedwe a Mzimu Woyera, ukasandulika thupi kwa ife, mwa Umunthu wa Yesu Khristu, ife tidzamuveka Iye korona kukhala Mfumu ya mafumu. Uko nkulondola. Mukuona?

303 Tsopano, kumbukirani, pafupi nthawi imene Khristu anadzakhala pa Mpandowachifumu, wotsutsakhristu anadzakhala pa mpandowachifumu, Yudasi. Pafupifupi nthawi imene Khristu anachoka pa dziko lapansi, Yudasi anachoka pa dziko lapansi. Basi pafupifupi nthawi yomwe Mzimu Woyera unabwerera, wotsutsakhristu anadzabwerera.

304 Inu mukudziwa, Yohane ananena cha apa, "Ana aang'ono, ine sindikufuna kuti mukhale osadziwa, inu mukudziwa, zokhudza wotsutsakhristu, amene wabwera kale ndipo akugwira ntchito mwa ana a kusamvera." Wotsutsakhristu nthawi imeneyo, anali ali kumeneko, anayamba kupanga mmenemo mzimu wa Chinikolai, kuti apange bungwe.

305 Nzosadabwitsa kuti ine ndinkadana nacho chinthu chimenecho! Mukuona? Mukuona? Ndi zimenezotu. Sindinali ine; chinali Chinachake mkati umu. Ndi chimenecho chinthucho. Icho chatulukira. Kodi inu mwachiwona icho? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndipo ine ndinali mozungulira mbali zonse za icho. Ine sindimakhoza kuchiwona icho kufikira pano. Ndipo

ine ndikuchidziwa icho tsopano. Ndi icho pamenepo. Mzimu wa Chinikolai umenewo, Mulungu ankawuda.

306 Ndipo tsopano mzimu umenewo unadzakhala mu thupi, ndipo iwo anauveka iwo korona. Ndipo ndi izi apa pomwe, zomwe Baibulo linanena kuti iwo akanadzachita nawo iwo. Ndi zangwiro. Oh, mai! Kukhala mu thupi! Iye anadzakhala munthu, ndipo zitatero iwo anamuveka iye korona.

307 Muwerenge, zindikirani! Kapena, muwerenge, kani, momwe Daniele akunenera kuti iye adzalanda ufumu wa mpingo. Kodi inu mungafune mutawerenga izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ife tiri nayo nthawi yochitira izo, sichoncho ife? ["Ameni."] Chabwino. Mvetserani. Tiyeni tibwerere ku Daniele, mphindi chabe. Tsegulaninso ku Bukhu la Daniele, ndipo ife tiwerenga kwa mphindi chabe. Ndipo ife mwina sitikhala nawo maminiti fifitini ena, twente, kapena sarte, kapena chinachake monga chomwecho. Ziribwino? ["Ameni."]

308 Tiyeni tipeze Daniele, mutu wa 11, ndipo tiyeni titenge ndime ya 21. Apa pali Daniele, Daniele akuyankhula tsopano momwe munthu uyu ati adzalandire.

> *Ndipo mu* dziko *lake adzaimirira munthu woyipa,* (akunena, Roma), *amene sadzampatsa ulemelero wa ufumuwo:* (tsopano penyani) *koma iye adzabwera* mwa mtendere. . . *kubweramo mwa* mtendere, *ndipo adzawutenga ufumuwo mwa chinyengo.*

309 Ndendende momwe izo zinadzachitikira! Ndizo zomwe Daniele anati wotsutsakhristu uyu akanadzachita. Iye adzakwanira pa malo a anthu. Inde, zidzakwanira pa zawo—pa zokonda zawo za tsiku lino, za matchalitchi. Pakuti, mu m'badwo wa mpingo uwu, iwo sakufuna Mawu, Khristu, koma iwo akufuna tchalitchi. Chinthu choyamba, iwo samakufunsa iwe ngati uli Mkhristu. "Ndiwe wa mpingo uti? Mpingo uti?" Iwo sakufuna Khristu, Mawu. Iwe ukapita, kukawauza iwo za Mawu ndi momwe angawongokere, iwo samafuna Zimenezo. Iwo amafuna chinachake, kuti azingokhala moyo uliwonse umene iwo akufuna kutero, ndi kumakhalabe a mpingo ndi kupeza umboni wawo. Mukuona? Mukuona? Kotero, iye akukwaniritsa chokhumbacho ndendende basi. Ndipo, kumbukirani, iye potsiriza anatchedwa "mkazi," mu Baibulo, ndipo iye anali hule ndipo anali ndi ana aakazi. Zikungokwanira pa chosowekera cha tsikuli, zimene anthu akufuna. Ndi zimenezotu.

310 Mulungu walonjeza izo. Pamene Mawu akanidwa, ndiye iwo amatembenuzidwira kwa zokhumba zawo. Tiyeni tiwerenge Atesalonika kachiwiri. Tiyeni. . . Ine ndikufuna kuti inu muwone apa miniti yokha. Eya, chabwino, ife tinawerenga izo, kanthawi kapitako. Atesalonika wachiwiri 2:9-11. Ananena kuti iwo akanadzatero. "Kuchikana, kukana Choonadi, iwo akanadzaperekedwa ku malingaliro achitayiko, ndipo

akanadzakhulupirira bodza ndipo akanadzalangidwa nalo ilo." Tsopano ndicho chimene—ndicho chimene Mzimu Woyera unanena.

311 Tsopano, kodi icho si chikhumbo cha mpingo lero? Iwe ukayesera kuwauza anthu kuti iwo ayenera kuchita *ichi, icho,* kapena *chinacho,* ndipo iwo amakudziwitsa iwe mwamsanga kuti iwo ndi Amethodisti, Apresbateria, kapena china-chonsecho, iwo "sasowa kupalasa nawo mu ngalawa yako." Mukuona? Zedi. Iwo amafuna zimenezo.

312 Ndipo Mulungu anati, "Ngati iwo akufuna zimenezo, ine ndingowalola iwo kuti akhale nazo. Ndipo Ine makamaka ndidzawapangitsa iwo kukhulupirira kuti icho ndi Choonadi, chifukwa Ine ndidzawapatsa iwo malingaliro achitayiko okhudza Choonadi." Tsopano tayang'anani apa chimene Baibulo likunena, nalonso, "Monga Yane ndi Yambure anamutsutsa Mose, momwemonso adzatero anthu awa mmasiku otsiriza, adzakhala nawo malingaliro achitayiko okhudza Choonadi; ndipo adzatembenuza chisomo cha Mulungu wathu kukhala zilakolako, kumamukana Ambuye Mulungu."

313 Tsopano inu mukuona pamene izo ziri; osati Akatolika okha, koma Achiprotestanti. Ndi chinthu chonsecho. Chinthu chonsecho ndi dziko la bungwe. Ndi ameneyo wokwera pakavalo-woyera, pansi pa—njira ya—ya a—a—(woyera) wolungama, mpingo, mwaona, koma wotsutsakhristu. Ziyenera kuwoneka mofanana. Pa kavalo, ngakhale, monga ngati Khristu akubwera pa kavalo. Mukuona? Oh, wotsutsa, zoyandikana kwambiri zikanakhoza kunyenga Osankhidwa omwe! Ndipo apa iye ali. Iye ndi wotsutsakhristu.

314 Iye anayamba kukwera mu m'badwo wa mpingo woyamba. Tsopano iye akukwera mpaka mmusi, mpaka mmusi kudutsa mu m'badwo uliwonse. Tsopano mpenyeni iye. Inu mukuti, "Kumbuyo komwe, kumbuyo komwe mu nthawi ya atumwi?" Iye ankatchedwa "Chinikolai" kumeneko. Kenako, mu m'badwo wa mpingo wotsatira, kenako iye anadzakhala "chiphunzitso" mu mpingo. Poyamba, iye anali chabe "choyankhulidwa," kenako iye anadzakhala "chiphunzitso."

315 Otukumuka, anthu otchuka, ovala-bwino, ophunzira mwapamwamba, opukutidwa, sankafuna zaphokoso zonsezo mu mpingo. Ayi, iwo, "Sankafuna zinthu zonse za Mzimu Woyera zimenezo. Uyenera kukhala mpingo! Ndipo ife tonse tidzadzera mu Khonsolo ya Nicaea, ndi zina zotero, ku Roma." Ndiye pamene iwo anabwera kumeneko, iwo anawutenga mpingowo, ndipo anatenga chikunja, Roma Katolika-. . . kapena chikunja, Roma wachikunja, ndi zamatsenga pang'ono. Ndipo anatenga a—Astarte, "mfumukazi ya kumwamba," ndipo anamutembenuza iye kuti akhale Maria, mayi. Kupanga opembedzera kuchokera mwa anthu akufa, ndi

zina zotero. Ndipo anatenga mkate wosatupitsa wozungulira uja, umene iwo umayikidwabe kukhala wozungulira pamenepo, ndikumawutcha iwo thupi la Khristu, "chifukwa iwo umayimira mayi wakumwamba." Ndipo Mkatolika amadutsa pamenepo, ndipo amazilemba yekha mtanda. Chifukwa, kuwala kumene kumayaka mmenemo, kumayenera kukhala mkate wosatupitsa womwe watembenuzidwa kukhala Mulungu, mwa mphamvu ya wansembe. Pamene, si kanthu mdziko koma chikunja basi. Mukuona? Uko nkulondola.

316 Ine sindikumvetsa basi. Chabwino, inde, ine ndikumvetsa. Inde, ndikutero. Inde, bwana! Ine ndikuzimvetsa izo, mwa chisomo cha Mulungu. Ndithudi.

317 Tsopano zindikirani. Oh, mai, momwe iwo angachitire izo! Mukuona? Ndipo iwo apatsidwa zokhumba zawo. Ayi, izo nzoona, inu simusowa kuti muchite Zimenezo. Ayi, bwana. Ngati inu simukufuna kuchita Izo, inu simukakamizidwa kuti muchite Zimenezo. Ngati inu simukufuna kuti mugwirizane ndi njira ya Mulungu ya moyo ndi zinthu, ndi kupembedza, inu simukusowa kuti muchite Izo. Mulungu samamupangitsa aliyense kuti achite Zimenezo.

318 Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Ngati dzina lanu linayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa limenelo asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi, inu mudzakhala okondwa kwambiri kuchita Zimenezo, inu simungayembekezere kwa miniti kuti muchite Zimenezo.

319 Tayang'anani apa. Inu mukuti, "Ine ndikupangitsani inu kuti mumvetse, ine ndine wachipembedzo basi!" Chabwino, izo zikhoza kukhala zoona.

320 Penyani, ndani anganene kuti ansembe aja sanali achipembedzo, mmasiku a Ambuye Yesu? Ndani anganene kuti Israeli sanali wachipembedzo, mchipululu? Pamene iwo anali ngakhale . . .

"Chabwino, Mulungu wandidalitsa ine nthawi zambiri chotero!"

321 Inde, Iye anawachitira iwo, nawonso. Iwo sankasowa ngakhale kugwira ntchito kuti akhale moyo. Iye ankawadyetsa iwo kuchokera kumwamba. Ndipo Yesu anati, "Iwo ali, mmodzi aliyense, anatayika ndipo anapita ndipo anafa."

322 "Makolo athu," iwo ankati, "anadya mana mchipululu, kwa zaka forte."

323 Yesu anati, "Ndipo iwo ali, mmodzi aliyense, anafa, analekanitsidwa Kwamuyaya." Mukuona? Iye anati, "Koma Ine ndine Mkate wa Moyo umene wabwera kuchokera kwa Mulungu Kumwamba. Munthu akadya Mkate uwu, iye sadzafa konse." Mukuona? Iye ndi Mtengo wa Moyo.

324 Ingozindikirani motani ndi pamene Yesu anabwera. Ansembe amenewo, iwo anabwera uko, achipembedzo kwambiri. Mnyamata, palibe amene angati iwo sanali anthu abwino. Mai! Iwo ankayenda pa mzere wa lamulo limenelo. Chirichonse chimene mpingo unkanena, iwo ankachichita icho. Ngati iwo satero, iwo ankagendedwa. Ndipo kotero Iye anatulukira . . . Inu mukudziwa chimene Yesu anawatcha iwo? Yohane anawatcha iwo, "Inu mulu wa njoka mu udzu! Musamaganize, kuti chifukwa ndinu wa bungwe limenelo, muli nacho chochita chirichonse ndi Mulungu." Ndipo Yesu anati, "Inu ndinu wa atate anu, mdierekezi." Anati, "Nthawi iliyonse imene Mulungu atumiza mneneri, chimachitika ndi chiyani? Inu mumamugenda iye ndi kumuponyera iye mmanda. Ndipo tsopano inu mukupita uko ndi kukakongoletsa manda ake."

325 Kodi icho si chinthu chomwecho chimene mpingo wa Katolika wachita? Tayang'anani pa Joan waku Arc, ndi Patrick Woyera, ndi ena onse a iwo. Iwowo ndi amene anawayika iwo mmenemo. Ndipo kenako anadzakumba thupi la Joan waku Arc, ndipo analiponyera ilo mu mtsinje, zaka handiredi zingapo mtsogolo mwake. Ndipo anamuwotcha iye poganizira kuti anali mfiti.

326 "Ndinu wa atate wanu, mdierekezi, ndipo ntchito zake inu mukuchita." Ndizo ndendende. Izi zidzapita ku dziko lonse. Mukuona? Kulondola! Ndicho chimene Yesu ananena.

327 Ndipo inu mukuganiza kuti izo zonse ziri bwino, zikuwoneka zabwino kwambiri, kavalo woyera uyo. Koma taonani chimene inu muli nacho. Ndicho ndendende chimene chikukwera pa iye. Tsopano, koma Iye anati iwo ankafuna zimenezo, kotero Iye adzawapatsa iwo chinyengo champhamvu.

328 Kumbukirani, hule ili la Chivumbulutso 17, iye anali chinsinsi, "CHINSINSI, BABELONI, MAYI WA TIMAHULE." Ndipo Yohane anamusilira iye. Basi monga ngati munthu uyu . . . Taonani, dikirani, ife tifike apa ndi kumuwona iye akumuyang'ana kavalo uyu apa. Mukuona? Koma inu munazindikira iye anali . . . Chimene chinachitika chinali ichi, kuti, "Iye anamusirira iye ndi chikhumbo chachikulu." Koma chinsinsicho chinali, chakuti, "iye anamwa magazi a ofera a Khristu." Mpingo wokongola utakhala pamenepo, utavekedwa mu mlangali ndi golide, "Ndipo iye anali nacho chikho mdzanja lake, cha zonyansa za ziwerewere zake."

329 Chiwerewere ndi chiyani? Ndiko kukhala moyo mosalungama. Ndicho chiphunzitso chake chimene iye anali kuchipereka. Kuwatenga Mawu a Mulungu ndi kuwapanga Iwo kukhala opanda mphamvu, ndi zina za "Tikuoneni Maria," ndi mitundu ina yonse iyi ya zinthu, ndi kumazipereka izo. "Ndipo mafumu a dziko lapansi anachita naye ziwerewere iye."

"Chabwino," inu mukuti, "ndiwo mpingo wa Katolika."

330 Koma iye anali "mayi wa timahule," mwaona, chinthu chomwecho chimene iye anali. Ndi zimenezotu.

331 Chinachitika ndi chiyani? Pamene wokonzanso anafa ndipo uthenga wake nkufa, inu-. . . Inu munawupanga iwo bungwe, ndi kuyikamo gulu la "Ma Ricky " mmenemo, ndi kuyambitsa chinthucho kubwereranso kuti muzikhala momwe inu mukufunira kutero. Inu simunafune kukhala ndi Mawu. Mmalo momapitirira nawo Mawu, iwo anakhala apo pomwe, "*Ichi* ndi Icho." Huh! Inu musamachite zimenezo.

Iye, ndi Chimenecho, mwaona, Iyeyo kumwamba Uko!

332 Zindikirani, ndicho chinthu chimodzi. Ife tikufuna kugunda malo ena angapo okha tisanafike potseka.

333 Iye ndi kalonga amene anali woti adzawononge; anthu a Daniele. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Tsopano ine ndipanga ichi, ngati inu mungondithandiza ndi kupirira nane kwa maminiti pang'ono, ine ndi—ndizipanga izo mofulumira basi mmene ine ndingathere. Koma ndikufuna kuchipanga icho motsimikiza, chifukwa ine. . . Mzimu Woyera unandipatsa ine Icho, motsimikiza basi monga momwe ine ndaimira pano. Mukuona? Mukuona?

334 Tsopano taonani, tiyeni titenge, tibwerere ku Daniele kachiwiri, miniti yokha. Ine ndikufuna kuti ndikuwerengereni inu chinachake, chimene. . . Ngati simubwerera mmbuyo, zonse ziribwino. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge Daniele 9, Daniele 9. Ndipo ndikufuna kuwerenga ndime ya 26 ndi ya 27 ya Daniele 9. Ndipo, penyani, ngati iye anali mmodziyo woti adzawononge anthu a Daniele, chimene iye anali woti adzachite.

> *Ndipo atapita masabata sikisite thuu Mesiya adzadulidwa,. . .*

335 Mwaona, ndiwo masabata sikisite thuu amene Iye akanadzadulidwa, kuchokera mu masabata sevente.

> *. . . osati kwa iyemwini:* koma kwa *anthu* ndipo *kalonga* (ndiwo ulamuliro wolowezana apa) *amene ati adzabwere* (amene *ati* adzabwere) *adzawononga mzindawo ndi. . . malo opatulika; ndipo kumathero kwake kudzakhala chigumula* chachikulu, *ndipo kufikira chimaliziro cha nkhondo zipasuko zidzakhala zotsimikizika.*

336 Ine ndikufuna kukufunsani anthu inu chinachake. Khristu atatha kudulidwa padziko lapansi, mu zaka zitatu ndi theka za utumiki Wake, ndipo nchiyani chinawononga kachisi? Ndani anamuwononga iye? Roma! Zedi. Konstantini kapena, ayi, ine ndikupempha chikhululukiro chanu, Tito, mtsogoleri wankhondo wa Roma, iye anamuwononga kalongayo. Tsopano zindikirani.

Penyani ichi, abwenzi. Bwerani mpaka mmusi momwe, pa khoma ili.

337 Pamene Yesu anabadwa, chinjoka chofiira kumwamba chinadzaima pa mkaziyo, kuti chimulikhwire Mwana wake mwamsanga pamene Iye anabadwa. Nkulondola uko? Anali ndani ameneyo, anayesetsa kuti amulikhwire Mwanayo pamene Iye ankabadwa? Roma. Mukuona? Ndi chimenecho chinjoka chofiiracho. Apa pali kalonga wanu. Apa pali chirombo chanu. Mukuona? Ndi amenewo apo, aliyense wa iwo, chimodzimodzi basi, mwaona, "kumulikhwira Mwanayo." Mulungu anamukwatulira Iye Kumwamba ndipo anakakhala pa Mpandowachifumu Wake. Ndiko kumene Khristu ali tsopano kufikira nthawi yoikika. Mukuona? Tsopano, penyani chimene iye ati adzachite.

338 Tsopano, oh, tsopano, ine ndikukhulupirira kuti ine ndinali kuyankhula kwa winawake kuno. Iye ayenera kuti anali M'bale Roberson lero, kapena winawake yemwe ine ndinali kumuyankhula, za ichi; osati za ichi apa, koma pa chinthu chomwecho basi. Ine ndikukhulupirira ine ndinalalikira pa izo muno, osati kale kwambiri, chimene chiti chidzachitike kwa United States uyu, pa nkhani ya ndalama iyi. Mukuona? Chabwino, ife tsopano tikulipira ngongole zathu pa misonkho yomwe iti idzalipiridwe zaka forte kuchokera lero. Ndiwo utali wake momwe ife tatsalirira mmbuyo. Kodi inu munatsegulapo KAIR kumtunda uko, kapena Lifeline, ndi kumvetsera kwa iyo, mwaona, kuchokera ku Washington? Bwanji, ife tagwa pachuma kwathunthu. Ndizo zonse.

339 Chavuta ndi chiyani? Golide yense wasungidwa, ndipo Ayuda ali ndi bondi. Iye adzakhala Roma. Tsopano penyani. Ife tikuwadziwa omwe ali ndi masitolo akuluakulu, koma Roma ali ndi gawo lalikulu la chuma cha dziko lapansi. China chonsecho, chiri ndi Ayuda. Tsopano penyani izi. Tsopano tangomvetserani kwa izi, momwe Mzimu Woyera unabweretsera izi kwa ine.

> *Ndipo iye adzatsimikizira panganolo ndi ambiri kwa sabata imodzi:* (tsopano penyani) *ndipo mkati mwa sabatayo iye adzachititsa kuti nsembe ndi* zoyenerazo *zithe,. . . .kwa kufalikira kwa* zonyansa *iye adzapangitsa izo kupasuka, ngakhale mpaka chimaliziro, ndipo icho chotsimikizikacho chidzatsanuliridwa pa opasulidwa.*

340 Penyani! Oh, iye ndi chinthu chothyathyalika bwanji! Ndi uyu apa. Tsopano, ife tachipeza chithunzi chathu ndipo tikudziwa kuti iye ndi Roma. Ife tikudziwa kuti iye ndi wokwera pakavalo woyera. Ife tikudziwa kuti iye anapita monga chiphunzitso. Ndiyeno kodi Roma wachikunja anali chiyani? Anatembenuzidwa nkudzakhala Roma waupapa, ndipo anavekedwa korona.

341 Tsopano penyani, “Mu nthawi yotsiriza.” Osati mmasiku oyambirira pamene Khristu anali kulalikira, koma, “mu nthawi yotsiriza,” gawo lotsiriza la sabata, kumene ife tangotenga kumene masabata sevente a Daniele. Ndipo Khristu ananenera kwa zaka zitatu ndi theka, ndipo zaka zina zitatu ndi theka zikuyembekezeredwabe. Nkulondola uko? Ndipo kalonga uyu mu nthawi imeneyo adzapanga pangano ndi anthu a Daniele, amene ali Ayuda.

Ndi pamene Mkwatibwi akutengedwapo tsopano. Iye sadzaziwona izo.

342 Zindikirani, mu theka lotsiriza la sabata la Daniele, anthu akupanga pangano. Kalonga uyu akupanga pangano ndi Roma, akupanga nawo pangano iwo, mosakaika chifukwa cha chuma, pakuti Akatolika ndi Ayuda akugwirizira chuma cha dziko lapansi.

343 Ine ndinali ku Vatican. Ine ndinawona korona wa patatuyo. Ndimayenera kukhala ndi zoyankhulana ndi papa; Baron von Blomberg anandipezera mpata umenewo, pa . . . Lachitatu masana nthawi ya firii koloko.

344 Ndipo pamene iwo ananditengera ine kwa mfumuyo, iwo anachotsa ngolekera za thalauza yanga. Izo zonse nzabwino. Anandiwuza ine kuti ndisatembenuze nsana wanga, pochoka kwa iye. Izo zonse nzabwino.

Koma ine ndinati, “Ine ndiyenera kukachita chiyani pamaso pa munthu uyu?”

345 Anati, “Chabwino, inu mukangolowa mkatimo ndipo mukagwade pansi ndi bondo limodzi ndipo mukapsyopsyone chala chake.”

346 Ine ndinati, “Izo ndiye ayi. Izo ndiye ayi. Ayi, bwana.” Ine ndinati, “Ine ndidza—ine ndidzamutcha munthu aliyense ‘m’bale’ amene akufuna kukhala ‘m’bale.’ Ine ndidzamutcha iye ‘m’busa,’ ngati iye akufuna kukhala nawo udindo woterowo. Koma, kupembedza munthu, izo zonse ndi za kwa Yesu Khristu.” Mukuona? Ayi. Ayi, bwana. Osapsyopsyona dzanja lirilonse la munthu monga chomwecho. Ayi, ndithudi. Kotero, ine sindinachite zimenezo.

347 Koma ndimayenera kudutsa mu Vatican monse. Bwanji, iwe sungakhoze kugula ndi madola handiredi billioni billioni. Chabwino, mukanati . . . Ndipo tangoganizani, “Chuma cha mdziko,” Baibulo linati, “chinapezeka mwa iye.” Oh, tangoganizani za malo opambana, kuchulukitsa mabillioni . . .

348 Nchifukwa chiyani chikominisi chinawuka chakuno mu Russia? Izo zimangondipangitsa ine kudwala mmimba mwanga, kuwamva alaliki ambiri akukuwa za chikominisi, ndipo samadziwa nkomwe chimene iwo akubwebwetera. Uko nkulondola. Chikominisi sichiri kanthu. Icho ndi chida mdzanja

la Mulungu, kuti abweretse chobwezera pa dziko lapansi, chifukwa cha magazi a oyera. Uko nkulondola.

349 Ndipo Mpingo ukadzatengedwapo, Roma ndi—ndi Ayuda adzapanga pangano kwa wina ndi mzake. Baibulo linati iwo adzatero, ndi anthu oyera. Ndipo tsopano zindikirani, iwo adzapanga izo chifukwa (chifukwa chiyani?) fuko lino lidzagwa pa chuma. Ndipo dziko lina lonse lapansi lomwe liri pamlingo wa golide lagwa pa chuma. Inu mukudziwa zimenezo. Ngati ife tikukhala moyo pa misonkho, ngongole zosalipidwa, za zaka forte kuchokera tsopano, ife tiri pati?

350 Pali chinthu chimodzi chokha chimene chikhoza kuchitika, ndicho, kuyitanitsa ndalamayo ndi kulipira ngongolezo. Ndipo ife sitingathe kuchita zimenezo. Wall Street ili nazo izo, ndipo Wall Street imalamulidwa ndi Ayuda. Zina zonsezo ziri mu Vatican. Ndipo Ayuda ali nazo zotsalazo mu Wall Street, ndi malonda a mdziko. Ife sitingaziyitanitse izo.

351 Ndipo ngati iwo angakhoze kuchita zimenezo, inu mukuganiza . . . Anyamata amowa awa ndi—ndi anthu onse a fodya awa, amene, mabillioni kuchulukitsa mabillioni a madola pachaka, ndi kuthetsa misonkho yonse ya phindu lawo pofuna kuti aziripirira zithunzi zakale zonyansa ndi zinthu monga zimenezo. Ndi kumapita ku Arizona uko, ndi kukagula mamillioni a maekara a malo, kapena masauzande, ndi kukakumbira zitsime zazikulu izo, pa madola fifite sauzande, ndi kulipira izo ndi msonkho wa phindu. Ndipo iwo nkukakuika iwe mu ndende ngati sungalipire wako. Ndi kutenga ndalamazo ngati achotsera msonkho, nkukumbira zitsime mwamsanga, ndi kukasalaza kumalako ndi zimakina. Ndipo iwo amachita chiyani? Iwo amakaikako ntchito zomanga nyumba kumeneko, mu nthawi yotsatira, ndi ndalama zawo zimene iwo anapeza. Iwo amayenera kupanga kusungitsako chuma. Ndi kukaikako nyumba, ntchito zomanga, kumeneko, ndi kuzigulitsa izo mamillioni a madola. Kodi inu mukuganiza kuti anthu amenewo anganyengerere, kuti asinthe ndalama?

352 Monga munthu uyu cha kuno mu . . . Dzina lake ndani? Castro anachitira. Iye anachita chinthu chanzeru chokhacho chimene iye anayamba wachichitapo, ndiye, pamene iye anathetsa mabondi, anawalipira iwo ndi kuwathetsa iwo.

353 Zindikirani, koma ife sitingathe kuchita zimenezo. Anyamata awa sangalole zimenezo. Amalonda olemera a padziko lapansi azigwira izo.

354 Ndiyeno pali chinthu chimodzi chokha choti muchite. Mpingo wa Katolika ukhoza kulipira izo. Ndi iwo wokhawo umene ali ndi ndalama. Ndipo iwo ukhoza kuchita izo, ndipo iwo udzazichita zimenezo. Ndipo pochita izi, kuti utenge izo, iwo udzagwirizana ndi Ayuda, kuti apange pangano. Ndipo pamene iwo udzapanga pangano ili ndi Ayuda . . . Tsopano,

kumbukirani, ine ndikuzitenga izi kuchokera mu Lemba. Ndipo tsopano, pamene iwo udzachita izi, ndi kupanga pangano ili, ife tikuzindikira, mu Daniele 8:23 ndi 25, "iwo udzachititsa kuti luso lipambane," ndipo luso ndiko *kupanga katundu*, "mdzanja lake." Ndipo iye adzapanga pangano ili ndi Ayuda.

355 Ndipo, pakati pa zaka zitatu ndi theka, izi, iye adzaswa pangano lake, mwamsanga akadzakwaniritsa chimene amafuna kuchita, ndipo adzayamba kulamulira ndalama za Ayuda. Ndipo pamene iye adzachite zimenezo . . . Oh, mai! Oh, mai!

356 Iye akutchedwa wotsutsakhristu mpaka kumapeto a m'badwo wa mpingo, pakuti iye ali . . . iye ndi ana ake ndi otsutsa Khristu ndi Mawu. Munthu uyu akutchedwa wotsutsakhristu.

357 Tsopano, iye adzafika pozigwira ndalamazo. Ndipo apo ndi pamene ine ndikuganiza kuti izo zidzafikapo. Miniti yokha, pamene ine ndikunena izi, ndiye ine ndikufuna kuti ndibwerere kwa izo mu miniti.

358 Iye akutchedwa wotsutsakhristu, ndipo adzatchedwa wotsutsakhristu, pamaso pa Mulungu, mpaka mu nthawi yotsiriza. Tsopano, koma kenako iye adzatchedwa chinthu chinachakenso.

359 Tsopano, pamene iye adzatenge ulamuliro wa ndalama zonsezo, "Ndiye iye adzaswa pangano ili ndi Ayuda," monga Daniele apa ananenera kuti iye akanadzachita izo, "pakati pa theka lotsiriza la masabata sevente," a Daniele. Ndipo akadzatero, m'bale, kodi iye adzachita chiyani? Iye adzatenga malonda onse adziko lapansi ndi zachuma, adzapanga pangano ndi dziko lapansi, chifukwa iye adzagwirizira chuma cha dziko lapansi, kwathunthu. Ndipo panthawi imeneyo, aneneri awiri amenewo adzawuka powonekera ndipo adzaitana handiredi ndi forte-foro sauzande amenewo. Ndiye chidzachitike ndi chiyani? Zikadzatero chilemba cha chirombo, cha Chivumbulutso 13, chidzayambika, chifukwa iye wagwira zachuma zonse, malonda, ndi chirichonse cha mdziko. Ndipo chidzachitike ndi chiyani zikadzatero? Chilemba cha chirombo chidzayambika, kuti, "Palibe munthu adzathe kugula kapena kugulitsa, kupatula iye amene ali nacho chilemba cha chirombo."

360 Tikuthokoza Mulungu, Mpingo udzakhala ukusangalala mu zaka zitatu ndi theka zopambana mu Ulemelero, sudzasowa kuti udzadutse zimenezo.

361 Tsopano zindikirani, pa nthawi yotsiriza, pa mapeto a mibadwo ya mpingo tsopano, iye akutchedwa . . . Iye ndi ana ake akutchedwa otsutsakhristu, chifukwa chirichonse chimene chikutsutsa Khristu ndi chotsutsa-Khristu. Ndipo chirichonse chimene chikutsutsa Mawu chikutsutsana ndi Khristu, chifukwa Khristu ndi Mawu. Tsopano iye ndi wotsutsakhristu.

362 Ndiye, mu Chivumbulutso 12:7-9, pamene Satana waponyedwa kunja, wotineneza. Inu mukufuna kuti mulembe

zimenezo, chifukwa ine ndikufuna kuti inu mukawerenge izo. Ife tiribe nthawi tsopano; ili pafupi, twente kapena fifitini kuti ikwane teni, mwaona. Koma mu Chivumbulutso 12:7-9, "Satana," mzimu, "mdierekezi," amene ali mmwamba umo tsopano, "wowaneneza abale athu." Chabwino.

363 Mpingo ukutengedwera mmwamba, ndipo Satana akuponyedwa kunja. Pamene Mpingo ukupita mmwamba, Satana akubwera pansi, ndiye Satana akudzilowetsa yekha mu thupi la wotsutsakhristu ndipo akutchedwa "chirombo." Kenako, Chivumbulutso 13, iye akuyika chilembacho. Mukuona?

364 "Pamene Iye amene akumuloleza," kokha tsopano, Chikhristu chasiyidwa pa dziko lapansi mu chiyero chake, pa chifukwa chakuti, "Iye amene akumuloleza."

365 Kumbukirani kumbuyo kuno mu Atesalonika, "Atakhala mu kachisi wa Mulungu, kumadzitcha yekha Mulungu, kumakhululukira machimo pa dziko lapansi." Ndipo izo zidzapitirira, "ndipo kusaeruzika kudzachuluka," ndi kumapitirira. Chifukwa, izo sizidzadziwika, apobe, mpaka nthawi yake yoti awululidwe itaitanidwa.

366 Ndipo kenako Mpingo udzakwatulidwa. Ndipo pamene Iwo udzakwatulidwa, ndiye iye adzadzisintha yekha kuchokera pokhala wotsutsakhristu tsopano, oh, mai, "mpingo, mpingo waukulu ndi zimenezo," tsopano iye akudzakhala "chirombo." Uh-huh! Ine ndikukhumba ndikanakhoza kuwapangitsa anthu kuziwona zimenezo.

367 Tsopano kumbukirani, wotsutsakhristu ndi chirombo ndi mzimu womwe womwewo. Ndi umenewo utatuwo. Inde, bwana. Awo ndi magawo atatu a mphamvu yomweyo ya mdierekezi. Kumbukirani, Chinikolai, mwaona, iwo unkayenera kukhala mu thupi usanavekedwe korona. Mukuona? Tsopano penyani ichi, magawo atatu. Gawo loyamba, iye akutchedwa wotsutsa Khristu; gawo lachiwiri, iye akutchedwa mneneri wabodza; gawo lachitatu, iye akutchedwa chirombo.

368 Zindikirani, Chinikolai, chiphunzitso chotsutsakhristu chimene chinayamba mmasiku a Paulo, motsutsa Mawu a Mulungu, wotsutsakhristu.

369 Kenako iye akudzatchedwa, kachiwiri, mneneri wabodza. Amene, pamene chiphunzitsocho chikudzakhala munthu, iye anali mneneri kwa chiphunzitso cha utsogoleri wolowezana, cha—utsogoleri wolowezana wa mpingo wa Katolika. Papa anali mneneri kwa mawu abodza, ndipo izo zinamupanga iye kukhala mneneri wabodza.

370 Gawo lachitatu ali chirombo, munthu amene akuvekedwa korona mmasiku otsiriza, ali ndi mphamvu iliyonse imene Roma wachikunja anayamba wakhalapo nayo. Chifukwa, chirombo cha mitu-seveni, chinjoka, chinaponyedwa kuchokera kumwamba, ndipo chinadzabwera mu thupi mwa mneneri

wabodza. Ndi zimenezotu pamenepo, iye anali ndi akorona seveni, ndipo anaponyedwa kunja ndi kuponyedwa pa dziko lapansi ndi pa nyanja. Chabwino.

371 Kodi ife tikunena chiyani? Ndi ndani wokwera uyu, wokwera pa kavalo uyu? Kodi inu mukudziwa chimene iye ali? Ndi munthu wapamwamba wa Satana.

372 Ine ndinapita usiku wina, abale awiri akhala mu tchalitchi muno tsopano, M'bale Norman, kumbuyo uko, ndipo, ine ndikukhulupirira, ndi M'bale Fred, ife tinapita kukamumva munthu akuphunzitsa za wotsutsakhristu. Munthu wodziwika bwino, mmodzi wa opambana amene a Assemblies of God ali nawo, ndipo kutanthauzira kwake kwa wotsutsakhristu kunali, kwakuti, "Iwo adzatenga vitamini ya mtundu winawake, kuchokera mwa—mwa munthu, ndi kudzausamutsa moyo uwu kuchokera mwa munthu nkudzawulowetsa mu fano lalikulu limene liti lidzamate. . . lizidzayendera mdadada wa mu mzinda pa nthawi. Ndipo ndicho. . . " Kodi inu mungakhoze kulingalira munthu wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, kukhala pansi pa chinyengo choterocho monga icho, kapena kumadzinenera kuti ali?

373 Pamene, apa pali Baibulo, likunena yemwe wotsutsakhristu ali. Sikuti ali. . . Iye ndi munthu. Zindikirani, wokwera uyu siali kanthu kena koma munthu wapamwamba wa Satana, mdierekezi ali mu thupi. Iye ndi namatetule wamaphunziro. Tsopano, ine ndikuyembekeza kuti inu mwatsegula makutu anu. Iwo anali kumuyesa mmodzi wa ana ake, osati kale kwambiri, pa programu ya pa televizioni, kuti awone ngati iye sanali wanzeru kwambiri kuposa munthu wotsatirayo, kuti apikisane nawo pa mpando wa u Purezidenti. Mukuona? Koma, komabe, iye ndi wanzeru kwambiri; chimodzimodzinso Satana. Iye amayesetsa kuzigulitsa izo. Iye anazigulitsa izo kwa Eva. Iye anazigulitsa izo kwa ife. Ife takhala tikufuna munthuwapamwamba. Ife tamupeza iye. Chabwino. Dziko lonse likufuna munthuwapamwamba. Iwo amupeza iye. Mungodikirira mpaka Mpingo udzapite mmwamba, ndipo Satana waponyedwa kunja; iye adzakhala mu thupi. Uko nkulondola. Iwo akufuna winawake amene angagwire kwenikweni ntchitoyo. Iye adzaichita iyo.

374 Wophunzira! Uyu ali. . . munthuwapamwamba wa Satana, wokhala nawo maphunziro, ndi wanzeru, wa fioloje ya mpingo ya mawu ake omwe, za zopanga iyemwini. Ndipo iye akukwera kavalo wake woyera wachipembedzo, kuti akawanyenge anthu. Ndipo iye adzagonjetsa chipembedzo chirichonse cha mdziko, chifukwa iwo onse akukalowa mu chitaganya cha—cha. . . cha mipingo, ndi chitaganya cha mipingo ya mdziko lonse lapansi. Ndipo iwo amanga kale zinyumba zawo, ndipo chirichonse chikukhala mu mzere momwe. Palibe chinthu chimodzi chatsalira. Chipembedzo chirichonse chadziphatika

mkati mmenemo, chitaganya cha mipingo. Ndipo nchiyani chikuimira icho kumbuyo? Roma. Ndipo papa tsopano akufuula, "Ndife tonse amodzi. Tiyeni tibwere pamodzi ndipo tiziyenda limodzi."

375 Ndipo anthu awa, ngakhale ena a inu anthu a Full Gospel, mumakana, mumayenera kukana chiphunzitso chanu chauvangeri, kuti mutenge sitepe yotero monga iyo. Kodi inu mwachita chiyani? Akhungu kwambiri, kwa chinthu chachibungwe chimenecho, inu mwakana Choonadi. Ndipo Choonadi chinaikidwa pamaso pawo, ndipo iwo—iwo anachoka kwa Icho, ndipo anachisiya Icho. Ndipo tsopano iwo "aperekedwa kwa chinyengo champhamvu, kuti akhulupirire bodza ndi kudzawonongedwa nalo ilo." Ndizo ndendende chimene icho chiri.

376 Ndipo wotsutsakhristu akuzitenga izo zonse. Ndipo Baibulo linanena, kuti, "Iye anawanyenga onse," a, ma l awiri, "onse pa nkhope ya dziko lapansi, amene maina awo sanalembedwe pansi pa Zisindikizo zimenezo kuchokera ku maziko a dziko lapansi." Hum! Tsopano, ngati Baibulo linati iye anachita izo, iye anachita izo.

377 Iwo amati, "Chabwino, ndine wa. . ." Ndi zimenezotu pamenepo. Eya. Ndizo ndendende basi. Ilo ndi bungwe lomwelo la mahule. Iko ndi kachitidwe komweko kamene kanayamba pachiyambi, komwe kali kotsutsakhristu, kudutsa monsemo.

378 Ine ndidzamva kuchokera kwa iwo, koma ndicho. . . Ndicho Choonadi. Ine ndikuyembekezera kutero. Ameni.

379 Tsopano, zindikirani, iye adzagonjetsa. Ndipo pafupifupi watero mwa kugwira kwake pakali pano, pamene iye akadali wotsutsakhristu, iye asanakhale chirombo. Inu mukunena za chilango chankhanza? Inu mungoyembekeza. Penyani zomwe iwo amene adzatsalire pano pa dziko lapansi ati adzadutsemo. Uh-huh. "Kudzakhala kulira, ndi kubuula, ndi kukukuta kwa mano. Pakuti chinjokacho, Roma, chinalavula madzi kuchokera mkamwa mwake, kuti chipange nkhondo ndi otsalira a mbewu ya mkaziyo, amene anasiyidwa pa dziko lapansi Mkwatibwi atatha kusankhidwa ndi kutengedwapo. Ndipo chinjokacho chinachita nkhondo ndi otsalirawo, sankafuna kulowamo, ndipo anasakidwa."

380 Ndipo Mpingo weniweni ukanadzadutsa mu zimenezo ngati kukanakhala kotheka; koma, inu mukuona, iwo ayikidwa pansi pa Magazi awa, mwa chisomo cha Khristu, ndipo sangakhoze kudutsa mu Chisautso chirichonse. Iwo alibe nthawi ya Chisautso. Chinthu chotsatira kwa Mpingo ndi Mkwatulo. Ameni, ndi ameni! Matamando apite kwa Mulungu. Oh, momwe ine ndimazikondera izi!

381 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Ife tikuyankhula za chomwe mgonjetsi ati adzachite, ndipo iye adzagonjetsadi kwenikweni.

Iye wachita kale icho. Zinasokedwa kale basi, ndizo zonse; adzazisoka izo, ndi ndalama, kukhumbira konyansa. Ndizo ndendende. Iwo amakonda ndalama kwambiri kuposa Mulungu. Chirichonse chimene iwo amaganiza tsopano ndicho, "Ali nazo ndalama zingati?" Ndi chiyani icho?

382 Inu mukudziwa, izo zakhala zikunenedwa, nthawi zambiri, "Upatseni mpingo ndalama, ndipo iwo udzalisintha dziko. Upatseni mpingo ndalama, ndipo iwo udzatumiza avangeli ku dziko lonse lapansi. Ndipo kodi iwo udzachita chiyani? Iwo udzagonjetsera dziko kwa Khristu."

383 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, mzanga wosauka, wakhungu. Dziko silimapindulidwa ndi ndalama, koma ndi Magazi a Yesu Khristu. Mpatseni Mulungu amuna omwe ali amuna ochirimika, amene adzayime pamenepo pa Mawu amenewo, kukhala moyo kapena kufa; amene adzagonjetse. Uh-huh. Padzakhala chinthu chimodzi chokha chomwe chingadzagonjetse, iwo amene ali ndi maina awo atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Ndicho chinthu chokhacho chomwe chidzamve Iwo. Ndalama sizidzakhala nako kalikonse kochita nazo izo; zidzawatumiza iwo kutali mu miyambo yawo ya zipembedzo.

384 Tiyeni tiwone. Inde, namatetule wophunzira, iye adzakhala. Iye adzakhala wanzeru. Mai, mai, mai! Ndipo ana ake onse momuzungulira iye adzakhala anzeru, Ph.D., LL.D., ma L awiri.D., Q.S.D., A.B.C.D.E.F. mpaka mmusi ku Z. Iwo adzakhala nazo zonsezo, anzeru. Chifukwa chiyani? Izo zikutsatira dongosolo la Satana. Kuchenjera kwa ukathyali kulikonse kotsutsa Baibulo ndi kwa Satana.

385 Ndicho ndendende chimene iye anamutengera Eva. Eva anati, "Oh, kwalembedwa, Mulungu anati ife tisamachite zimenezo."

386 Iye anati, "Koma, dikira. Ndithudi Mulungu sadzachita izo. Koma ine nditsegula maso ako ndipo ndikupatsa iwe nzeru zina." Iye anazipeza izo.

387 Ife takhala tikumufuna iye. Ife tampeza iye, nafenso, fuko lino. Zindikirani, iye adzagonjetsa dziko lonse lachipembedzo. Iye adzagonjetsa, adzapanga pangano ndi anthu a Daniele. Ndi izi apa, monse muwiri mwa anthu Amitundu ndi mwa anthu a Daniele, Ayuda kwa masabata otsiriza. Ndipo ife tiri pano, ngakhale kuzijambula izo pa mabolodi. Ndipo inu mukuziwona izo, mwangwiro, apo ndi pamene izo ziri. Tikuthokoza Mulungu. Ndi uyo pamenepo. Kachitidwe ka chibungwe kameneko ndi ka mdierekezi. Ndipo palibe kunyengerera pa zimenezo, nkomwe. Mukuona? Ndendende. Ndiwo muzu wa mdierekezi. Ndiwo . . .

388 Tsopano, osati anthu, osati anthu ali mmenemowo. Iwo ndi anthu a Mulungu, ambiri a iwo. Koma, inu mukudziwa chiyani, pamene ife tidzafika apa, mpaka tikadzatenga Malipenga

awa akuwomba; ndipo, nthawi yotsatira ine ndikadzabwera kuno, kuwomba kwa Malipenga awa. Kumbukirani, pamene iwo, a mngelo wotsiriza . . . Mngelo wachitatu uyo anabwera kumeneko, "Tulukani mwa iye, anthu Anga!" Pamene Mngelo ameneyo akuwuluka, ndi nthawi yomweyo imene Uthenga uwo ukudzagwera kuno kwa Lipenga lotsiriza, Uthenga wa mngelo wotsiriza, Chisindikizo chotsiriza chikutsegulidwa. Zonsezo zikuchitika pa nthawi imodzi. Inde, bwana. Zonse zikukhazikika ndi kupita ku Muyaya.

389 Tsopano chiyani? Pa nthawi yomweyo imene munthu uyu akugonjetsa . . . Kenako ine nditseka. Mulungu adzachita chinachake pamenepo, nayenso. Tiyeni tisangomupatsa Satana kubwekerera konse apa, mwaona. Tiyeni tisayankhule za iye, palimodzi. Mukuona? Pamene chinthu chachikulu ichi chikuchitika kunja uko, dongosolo lalikulu ili likuthera mu mabungwe awa, mu mgwirizano, kotero kuti iwo akhoze kudzisonkhanitsa okha limodzi ndi kuyima motsutsa chikominisi, ndipo osadziwa kuti Mulungu anadzutsa chikominisi kuti chiwagonjetse iwo. Ndithudi.

390 Chiyani—chiyani—chiyani chinapangitsa kuti chikominisi chiwuke ku Russia? Chifukwa cha chidetso cha mpingo wa Roma ndi ena onsewo. Iwo anatenga ndalama zonse zimene zinali mu Russia, ndipo anawazunza anthu mpaka ku imfa, ndipo osawapatsa iwo kalikonse, ndipo mmalo mwake, ndipo nkumakhala basi monga ngati dziko lonselo.

391 Ine ndinali uko ku Mexico, osati kale kwambiri, ndipo ndinawawona ana aang'ono osauka amenewo. Dziko lirilonse la Chikatolika silimadzithandiza lokha nkomwe. Palibe limodzi la iwo. Ndifunseni ine kuti. Ndiwonetseni ine kumene iwo ali. Dziko lirilonse lolamulidwa ndi Chikatolika silingakhoze ngakhale kudzithandiza lokha. France, Italy, ndi onse amenewo, Mexico, kulikonse komwe mungapite, iwo siali odzithandiza okha. Chifukwa chiyani? Mpingo unatenga chirichonse chimene iwo anali nacho. Ndi chifukwa chake Russia anawuthamangitsa iwo. Penyani chimene chinachitika.

392 Ine ndikuzidziwa izi, inemwini. Ine ndinali nditayima kumeneko. Ndipo inu mukanakhoza kuganiza kuti chisangalalo chagolide chinali chikuchitika, inu mumamva mabelu akulira. Ndipo apa mkazi wamng'ono wosauka, akubwera chotsika mu msewu, akukwakwaza mapazi ake. Ndipo bambo atayangata khanda; ndipo awiri kapena atatu a iwo, akulira. Mkaziyo amakapanga kudzitunduza kwa mkazi wina wakufa kumeneko. Anali naye iye . . . Ankaganiza kuti iye akanadzapita Kumwamba, pochita zimenezo. Oh, ndi chinthu chomvetsa chisoni bwanji!

393 Kenako ine ndinawona, nditayima kumusi uko, apa panabwera . . . Chuma chawo sichikuima mokhazikika!

Mpingo umatenga chirichonse chimene iwo ali nacho. Apa, Pancho wamng'ono, mwinamwake—mwinamwake Pancho amatanthauza Frank. Iye akubwera kumeneko, ndipo iye ndi womanga njerwa, ndipo iye amalandira—iye amalandira mapeso twente pa sabata. Koma zingatengere mapeso twente onsewo, kuti adzigulire nsapato. Ndicho chuma chawo. Koma tsopano, apa, nanga bwanji ndiye ngati—ngati iye, pokhala womanga ndiponso woyala njerwa, ndipo amalandira mapeso twente pa sabata, mongoyerekeza chabe. Ine sindikudziwa zomwe iye amapeza, koma tingoti chuma cha mtundu woterowo momwe chikuyendetsedwera. Zindikirani, tsopano, ngati iye amapeza mapeso twente pa sabata.

394 Apa pakubwera Chico, mwaona, zomwe zimatanthauza "wamng'ono," ndipo amagwirira ntchito kumeneko pafupifupi mapeso faivi pa sabata. Ndipo ali ndi ana teni oti aziwadyetsa, koma padzakhala winawake akugogoda pa chitseko chake, [M'bale Branham akugogoda pa guwa kangapo—Mkonzi]. kuti adzatenge pafupifupi mapeso faivi amenewo, kapena foro a iwo, mulimonse, kuti akalipirire kandulo yamafuta kuti ikayatsidwe pa guwa la golide, la madola millioni chifukwa cha machimo ake. Ndi zimenezotu pamenepo. Ndiko kulinganiza kwake kwa chuma. Umo ndi momwe maiko aliri.

395 Chinthucho chimatenga zonsezo. Mpingo umatenga izo zonse. Iwo wangokhala nacho m'manja mwake. Ndizo zonse. Ndipo iye, ali ndi ndalama za Ayuda, mu pangano limenelo, monga Baibulo linanenera, kuti iwo adzatenga chinthu chonsecho.

396 Ndiye kenako iye adzasandulika chirombo. Iye adzaswa pangano lake, ndipo iye adzalanda. Iye adzang'amba mbewu ina yonse ya mkazi ameneyo, monga chomwecho. Ndi kulavula madzi kuchokera mkamwa mwake; kudzachita nkhondo. Ndipo kudzakhala kulira, ndi kubuula, ndi kukukuta kwa mano.

397 Ndipo Mkwatibwi adzakhala akukwatiwa, mu Ulemelero, mwaona, nthawi yomweyo. Usadzaziphonye izo, mzanga. Mulungu andithandize ine! Ine—ine ndikufuna ndidzakakhale kumeneko. Ine sindikusamala mtengo wake. Ine—ine ndikufuna ndidzakakhale kumeneko.

398 Tsopano, zindikirani, mu nthawi yomweyo imene izi zikuchitika, basi izi zisanachitike, kani, pa dziko lapansi, Mulungu walonjeza . . . Pamene zosokonezeka zonse izo za zipembedzo, kutsutsana kusiyana kwawo pa tizikhulupiriro tawo, Mulungu analonjeza kuti akanadzatitumizira ife mneneri woona wa Mawu owona, ndi Uthenga; kuti tibwerere ku Mawu apachiyambi a Mulungu, ndi "Chikhulupiriro cha makolo," kutsitsa Mphamvu ya Mzimu Woyera pakati pa anthu, ndi mphamvu yomwe iti idzamukweze iye pamwamba pa zinthu izi ndi kudzamutengera iye mkati, pa nthawi yomweyo. Inde.

Mawu omwewo akutsimikiziridwa, a Yesu Khristu, kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! "Taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, kufikira chimaliziro. Ndipo ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Ine ndidzakhala ndi inu. Kanthawi pang'ono, ndipo iwo sadzandiwonanso Ine," chifukwa iwo adzazipanga okha bungwe ndipo adzamwazikana. "Koma inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu. Ine ndidzakhala ngakhale mwa inu, mpaka ku chimaliziro." Pamene Iye anati ukali Wake udzatsanuliridwa pambuyo pa chimaliziro. Ndi zimenezotu. O Mulungu!

399 Ndi ndani wokwera pa kavalo woyera uyo? Inu sindinu akhungu. Inu mukuona yemwe iye ali. Ndi wotsutsakhristu uja, ndi mzimu wachinyengo uwo umene wapita tsopano ndi kukakwawira mkati. Anapanga . . . Ndipo, ndiye, mukuona, Mulungu akumangobwerezabwereza zimenezo. Iye akuwonetsera izo monga munthu akupita ndi kavalo woyera, ndipo ali ndi uta wake wopanda muvi. Iye ndi wopusitsa. Iye alibe mphamvu. Mukuti, "Mphamvu ya mpingo!" Ili kuti iyo? Iwo amachita chiyani? Iwo amati, "Ife ndife mpingo wapachiyambi." Mpingo wapachiyambi unkatulutsa ziwanda, unkachiritsa odwala, ndi kuwukitsa akufa, unkawona masomphenya, ndi china chirichonse. Zirikuti tsopano? Mukuona? Ndi wopusitsa, uta wopanda muvi. Huh! Uko nkulondola.

400 Koma, inu mukuona, pamene Khristu adzabwera, Lupanga linatuluka kuchokera mkamwa Mwake, monga kung'anima kwa mphezi. Ilo linapita ndi kukawatha adani Ake, ndi kumuponyera kunja mdierekezi. Ilo linadula china chirichonse. Ndipo Iye anabwera, chovala Chake choviyikidwa mu mwazi, ndipo pa ntchafu Yake panalembedwa, "Mawu a Mulungu." Ameni. Apa Iye akubwera, ndi ankhondo Ake, akubwera kuchokera Kumwamba.

401 Wokwera pa kavalo woyera ameneyo wakhala ali mdzikoli nthawi zonse. Iye adzasintha kuchoka pokhala wotsutsakhristu. Iye akuchita zimenezo, ndipo akudzakhala mneneri wabodza. Mwaona, iye poyamba anayamba, wotsutsakhristu, mzimu; kenako iye anadzakhala mneneri wabodza; kenako, mtsogolo, pamene mdierekezi adzaponyedwa kunja, iye adzakhala mu thupi pamenepo ndi mdierekezi. Magawo atatu! Loyamba, iye ndi mdierekezi, kuyamba ndi kuyamba, mzimu wa mdierekezi; kenako iye akukhala mneneri wabodza, mphunzitsi wa chiphunzitso chabodza; chinthu chotsatira, iye akubwera ngati mdierekezi kumene mwiniwake, ali mu thupi. Mukuona? Ndi uyo pamenepo.

402 Ndipo pa nthawi yomweyo pamene mdierekezi uyu akugwa kuchokera Kumwamba ndi kudzakhala mu thupi la munthu, Mzimu Woyera ukukwera mmwamba ndi kubwera pansi mmatupi a anthu. Ameni. Oh, mai! Ndi nthawi yotani!

Mawa usiku, Mulungu akalola, Chisindikizo Chachiwiri.

403 Inu mukumukonda Iye? Tsopano, inu mukukhulupirira Izo?

404 Ine ndingozimitsa tepiyo. Tsopano ine ndikamvetsera kuchokera kwa Iyo, inu mukudziwa zimenezo, mwaona, koma ine ndikuyembekeza kutero.

405 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, m'bale. Ine basi tsopano ndikudziwa, kwa nthawi imodzi mmoyo wanga, chifukwa chimene Mzimu umenewo nthawizonse wakhala ukundichenjeza ine motsutsa izo, bungwe limenelo. Ndine wothokoza kwa Ambuye Mulungu pondiwonetsa ine zinthu zimenezi. Ine ndikudziwa kuti Icho ndi Choonadi. Ndi icho pamenepo, kuwululidwa pomwepo apo. Apa iye akukwera mpaka kudutsa mu m'badwowo, ndipo akubwera pomwe pano ndi kudziwonetsera yekha pansi apa pomwe, mwangwiro basi monga iye angakhoze kukhalira. Mwaona, ndi iyeyo. Tsopano ife sitinanyengedwe pa zimenezo. Tsopano muli nawo maso anu otseguka. Muzikhala kutali ndi zinthu za mtundu umenewo. Ndipo muziwakonda Ambuye ndi mtima wanu wonse, ndipo muzikhala kumene ndi Iye. Inde, bwana. Tulukani mu Babeloni!

406 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Zinthu zitatu: zotsimikiziridwa ndi Mawu, zosonyezedwa ndi chithunzi, zowonetseredwa ndi ntchito za Mzimu, kutsimikizira kuti Iwo ndi Mawu.

407 Mulole Mawu abwere pa mipango iyi, Ambuye. Mudzachiritse odwala. Mudzachiritse munthu wodwala aliyense amene alipo, Ambuye, ndi iwo omwe ali kunja uko amene akulembera ndi kumaimba.

408 Atate, pa ora lino, pali machiritso ena amene akuyenera kuchitidwa pakali pano, ndipo ife tikupitirira ku msonkhano wa machiritso. Koma, Ambuye, ndi solo imeneyo, ife tikufuna kuti iyo ikhale mu dongosolo basi, Ambuye. Ndipo zinthu izi ziyenera kubwera.

409 Ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwatenge mawu awa tsopano amene anenedwa, ndipo muwapange iwo akhale enieni kwa anthu. Muwalole iwo kuti awawone Iwo, Ambuye. Atafinyidwa kwa nthawi, ndipo, Inu mukudziwa, Atate, kotero ine ndikupemphera kuti zokwanira zanenedwa kuti Mzimu Woyera utenge Izo ndi kuziwulula Izo mmitima. Iwo amene amalemba Malemba, mulole kuti iwo akawawerenge Iwo. Iwo amene akupanga matepi kapena—kapena—kapena kumvetsera matepi, mulole iwo akaziphunzire Izo; osati kukayika kutanthauzira kwawo kwawo kwa Iwo tsopano, koma kukangophunzira Mawu. Perekani izi, Atate. Mu Dzina la Yesu, ine ndikuzipereka izo zonse kwa Inu, ndi kwa ulemelero Wanu. Ameni.

410 [M'bale akulosera—Mkonzi]. Ameni. Oh, zikomo Inu, Ambuye!

Tiyeni tingomutamanda Iye.

411 Oh, ngati pali winawake pano amene sakumudziwa Iye mu kukhululuka, chitani izo tsopano. Inu mwamva chidzudzulo cholunjika, champhamvu chimenecho. Ngati mukuyembekezera konse kuti muyandikire pafupi, chitani izo tsopano, kwa masiku zikatha izi.

412 Bwanji ngati uko kukanakhala kumatula kwa Chisindikizo chimenecho? Bwanji ngati uyo anali Mngelo yemwe anatumiza kumeneko, amene anandiphulitsa, pafupifupi, kundichotsa ine pansi, tsiku lina, nditayima kumbuyo uko, pamene mboni zitatu zayima pafupi. Zimene ine ndinakuuzani inu ine ndisanapiteko, "Pakhoza kudzakhala kuphulika kumene pafupifupi kudzandinyamulire ine mmwamba." Ndipo ine ndinatengedwera mmwamba ndi Angelo asanu ndi awiri, ndipo ndinabwera chakummawa. Chinthucho chinakhala ngati chinandigwedeza ine kuchokera pansi.

413 Nkulondola uko, M'bale Norman, M'bale Fred Sothmann, amene anaima ndi ine pamene izo zinkachitika, pamwamba pa Tucson? Ndipo—a . . . Nditakhala, ndikuchotsa chisoso pa zovala zanga, ndendende zomwe masomphenyawo ananena. Ndipo kunali kum'mwera kwa . . . cha ku Tucson. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, M'bale Fred, M'bale Norman. Ndi awo pamenepo. Imiririrani pa mapazi anu, kuti anthu akhoze kuwona kuti inu munali pamenepo, mboni. Ine sindinayambe ndamvapo chirichonse chonga icho, mmoyo wanga.

414 Ndipo, nthawi yomweyo, iwo sanasake, tsiku lonselo. Ine ndinamupempha Fred, m'mawa wotsatira. Iye sakudziwa izi. Ine ndinamupempha iye kuti apite kukasaka, ndinapitirira kumati, "Kachiteni zimenezo. Kachiteni zimenezo."

415 Koma Iye anati, Iye anandiuza ine kumbuyo uko, "Iye sakachita zimenezo. Iwe ukupita Kummawa, pakali pano."

416 Ndipo Angelo asanu ndi awiri amenewo! Kuphulika koyamba, iye anatsegula. Eya. Bwanji ngati izo ziri? Ife tiri pa ora lotsiriza. Mukuona?

Ine ndinkonda . . .

Tiyeni timupembedze Iye.

Ine ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine

Tiyeni tiyimirire.

Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

417 Tiyeni tiweramitse mitima yathu tsopano, abale, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu. Alongo anga, ine ndayankhula moyipa kwa inu, koma ndimachita izo mwa

chikondi chaumulungu. Ine ndimachita izo chifukwa ine ndimakukondani inu; za kukhala ndi tsitsi lalitali, ndi kumavala ndi kumachita molondola. Ine ndachita izi chifukwa cha chikondi chaumulungu. Tiyeni tiyeretse chikumbumtima chathu tsopano pamene—pamene Clorox wa Mulungu. . .

418 M'mawa, mwinamwake nthawi idzakhala itatha kwambiri. Iye akhoza kutulukira. Zinthu izi zikubwera monga chonchi, abale, akhoza kukhala mathero a udindo wa umkhalapakati. Kodi inu munayamba mwaganizapo za zimenezo? Chabwino, ine sindikudziwa kuti izo ndi choncho. Ine sindikunena kuti ndi choncho. Koma bwanji ngati izo ndi choncho? Bwanji ngati izo ndi choncho? Nanga bwanji zimenezo? Sipadzakhalanso chiwombolo; zapita, pa nthawi imeneyo. Ine ndikuyembekeza kuti sichoncho, koma pali kuthekera kuti izo ndi choncho.

Ine ndimkonda Iye, ine. . .

Tiyeretseni ife, Ambuye. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

. . .ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

419 Lidalitsike Dzina la Ambuye! Ulemelero kwa Mulungu! Ine ndimakonda kumverera kokoma kumeneko. Kodi inu simukumverera Iko? Mzimu Woyera basi, ngati, ukusambitsa mokuzungulirani inu, kumayenda mozungulira ndi Iwo. Oh, zodabwitsa bwanji! Oh, taganizani za chifundo Chake!

Ine ndinkonda Iye, ine ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

420 Usayiwale Zimenezo, mzanga. Usayiwale Zimenezo. Uzitengere Zimenezo kwanu limodzi nawe. Ukakhale nazo Zimenezo. Ukazigwirizire Izo pa pilo wako. Usayiwale Zimenezo. Ukakhale ndi Zimenezo. Mulungu akudalitseni inu tsopano.

M'bale Neville, m'busa wanu.

63-0318 Chisindikizo Choyamba
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chivumbulutso Cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org